

CHISINDIKIZO CHACHISANU

NDI CHIWIRI



Zikomo inu, m'bale. Pamene ife tiri chiyimire, tiyeni tipemphere.

² Mulungu Wamphamvuzonse, mwini wa Moyo, ndi wopereka wa mphatso zonse zabwino, zauzimu, ife tiri indedi oyamika tsopano chifukwa cha nthawi iyi yopambana kwambiri, yapayokha, ya chiyanjano mu Kukhalapo Kwanu; ikupanga kupambana kwakukulu mu miyoyo yathu, Ambuye, nthawi yomwe ife sitidzayiywala konse, ziribe kanthu kaya ife tiyenera kukhala motalika chotani. Ndipo ife tikupemphera, Mulungu, kuti pa usiku wotsekera uwu...Ife tikuzindikira Lemba, pa tsiku la kutseka kwa phwando, Yesu anayima pakati pa iwo ndipo anafuwula, “Ngati munthu aliyense amva ludzu, muloleni iye abwere kwa Ine!” Ndipo ine ndikupemphera, Atate Akumwamba, kuti icho chibwereze kachiwiri usiku uno, kuti ife tikhoza kumva Liwu la Ambuye wathu likutiyanira ife, ndi kutiyitanira ife mu utumiki kwa Iye, kuyenda mwapafupi. Ife tikumverera kuti ife tamva Liwu Lake kale, mu kutsegula kwa Zisindikizo izi, likulankhula kuti ndi tsiku lotsiriza, ndipo nthawi ili pafupi. Perekani madalitso awa omwe ife tikuwapempha, Atate, mu Dzina la Yesu Khristu, ndi kwa ulemerero Wake. Amen.

Khalani pansi.

³ Ine ndikufuna kuwonjezera ichi, kuti, mwa misonkhano yonse ine ndinakhalapo nayo mu moyo wanga, ine ndikukhulupirira sabata ino yakhala nthawi ya ulemerero kwambiri ya moyo wanga wonse mu kutumikira. Ziribe kanthu zomwe ine ndiri nazo...ine ndawona zozizwitsa zazikulu zitachitidwa, zedi, kale, ndi misonkhano ya machiritso, koma izi ziri zoposa izo. Yakhala imodzi ya nthawi zazikulu, zopambana za moyo wanga, ndizo kukhala pano. Ndi kuwona kachisi wamng'ono akutenga mawonekedwe osiyana awa; osati kokha chokhacho, koma cha mkati kutenga mawonekedwe osiyana!

⁴ Ndipo, tsopano, ine ndinali kumufunsa Billy; iye anachedwa kwambiri, pa kubwera ndi kudzanditenga ine. Iye anati panali gulu lina labatizidwa. Lomwe, likufika kupitirira zana, sabata ino, la anthu omwe akubatizidwa mu Dzina la Ambuye wathu Yesu Khristu. Koteru, ife tiri—tiri othokoza. Ndipo Mulungu akudalitseni inu!

⁵ Ndipo, tsopano, ngati inu mulibe mpingo kwanu, ife tikukuyitanani inu kuno, kuti muzibwera ndi kudzayanjana

ndi ife. Ingokumbukirani kuti mpingo uli wotseguka. Ife sitiri chipembedzo, ndipo ine ndikuyembekeza ndi kudalira kuti iwo sudzakhala chipembedzo. Chiyanjano chokha kumene amuna ndi akazi, ndi anyamata ndi asungwana, amakomana pozungulira gome la Mulungu, ndi kuyanjana pozungulira Mawu, ndipo ife tiri nazo zinthu zonse mofanana.

⁶ Tsopano, ndipo ife tiri naye m'busa wodabwitsa, mwamuna weniweni wa Mulungu, ndipo ine ndiri wothokoza kwambiri chifukwa cha icho. Ngati inu mudzakumbukire, masomphenya, chaka chapitacho, Chakudya chiya chinasungidwa mmalo. Ndipo izo ziri chimodzimidzi zolondola. Ndipo ife tiri . . .

⁷ Ife tiri nawo malo tsopano, okwanira, a makalasi a Sande sukulu, a misinkhu yonse, ndipo ife tiri oyamikira basi chifukwa cha mwayi uwu. Amodzi ena anena, nthawi yina, ngati iwo akanangokhala ndi makalasi a Sande sukulu kumene iwo akanakhoza kumatumiza ana awo. Tsopano, inu, iwo ali nawo iwo tsopano. Kotero, tsopano, kotero inu musingobwerabe ndi kudzakhala ndi ife ngati inu mulibe mpingo kwanu.

⁸ Chifukwa, ngati inu muli nawo mpingo wabwino kumene inu mukupitako, ndipo amalalikira Uthenga, zina zotero, bwanji, ndilo—ndilo basi gulu lina la ife, inu mukuwona, kwina kwake. Koma ngati inu mulibe kwanu, ndipo inu muli . . .

⁹ Ine ndamva kuti ambiri anali, asamukira muno kuchokera ku mbali zina za dziko, kudzapanga uwu mpingo wawo kwawo. Ndipo ife ndithudi tikukulandira inu kuno ku Mawu a Ambuye. Ndipo ine ndikukumbukira, ine ndikuganiza, pamene ine ndinkachoka, ine ndinakuwuzani inu kuti—kuti misonkhano, malingana ndi momwe ine ndinali wokhudzidwa, ikanakhala pano pa kachisi.

¹⁰ Ine sindikudziwabe zonse zomwe Ambuye ali nazo kwa ine mtsogolo. Ine ndikudalira izo ku dzanja Lake, osati matsenga ena kapena chirichonse. Ine ndikungodikira basi, tsiku ndi tsiku, kuti Iye anditsogolere ine ku malo komwe ine ndingakhoze kukhala wotumikira bwino kwa Iye. Ndipo pamene Iye wathana nane ine, ndiye ine ndikudalira kuti Iye adzandirandira Ine Kwathu, mu mtendere.

¹¹ Ndipo, tsopano, ine ndiri woyamikira chifukwa cha mgwirizano wa anthu a kachisiyu. Monga Billy anali kundiwuza ine sabata ino, kuti, ine ndikuganiza, khomo lirilonse lomwe layimiridwa pano pozungulira kachisi uyu liri naye winawake ndi iwo. Iwo anatseguka, makomo anu ndi malo, ndi kutengeramo anthu omwe sakanakhala nawo malo aliwonse woti apiteko. Tsopano, ndiwo machitidwe enieni a Chikhristu. Ndipo makomo ena angodzazitsamo aliyense mu ngodya yaying'ono iliyonse yomwe iwo akanakhoza, kuwapezera anthu malo oti akhalemo.

¹² Chifukwa, iyi yakhala nthawi yovuta, pa chifukwa cha ichi, chochitika cha mtundu wina chomwe chakhala chikuchitika, cha masewero a mdziko, mtundu wina wa basiketibolo kapena chinachake, ndipo—ndipo kusungitsa malo kunali kutapangidwa. Kuwonjezera gulu lalikulu kuchokera . . .

¹³ Ine ndikuganiza, ayimiridwa pano mu mpingo wawung’ono uno, pafupi, kuzungulira zigawo makumi awiri ndi zisanu ndi zitatu kapena makumi atatu zayimiridwa pomwe pano mu mpingo, pambali pa mafuko akunja awiri, kotero, ndi kachitsitsimutso kakang’ono aka. Kotero, icho chikutenga malo okulirapo pang’ono, iwowokha. Kudziwa za . . .

¹⁴ Ine ndinali kufunsa lero, ndi anthu ena. Ine ndinati, “Ine ndamva kuti panalibe anthu ambiri a ku Jeffersonville pozungulira, mu msonkhano.”

¹⁵ Winawake analankhula, anati, “Ife sitingakhoze kulowa mkati.” Chabwino, icho, icho chinali chimenecho. Icho chinali chifukwa chake. Ena a polisi, ndi ena otero, amafuna kubwera ku msonkhano, koma anati, anali akulankhula pozungulira, anati, koma iwo anabwera ndipo iwo sakanakhoza kulowa mkati, kuti anali atadzaza kale isanakwane ngakhale nthawi yomwe iwo akanalowera mkati. Kotero iwo anali nayo nthawi yawo, mwinamwake, kanthawi kena, ndipo iwo sanabwere. Kotero tsopano anthu akubwera kuchokera ku malo ena, kotero ife tiri oyamikira kwambiri.

¹⁶ Tsopano, ine sindikudziwa. Chinthu chotsatira chimene chiti chitsatire ichi, chikanakhala Malipenga Asanu ndi awiri, mu uthenga wina. Koma, mu Zisindikizo, mwakuchitika chirichonse chaphatikizidwamo. Mibadwo ya mpingo kubwera mmusi, ndipo ife tinayiyika iyo poyamba, chomwe chinali kwambiri—chomwe chinali chofunikira kwambiri, koma . . . cha nthawi imeneyo. Tsopano, kutsegula kwa Zisindikizo kukuwonetsa kumene Mpingo ukupita, ndi momwe Iwo ukuthera. Ndipo tsopano, ine ndikuganiza, Atate Akumwamba akhala ndithudi achisomo kwa ife, pakutilola ife kuwona zomwe ife tiri nazo.

¹⁷ Ndipo ine ndikunena ichi, kuyang’ana pa zolemba zakale zomwe ine ndinalalikirapo, zaka zambiri zapitazo, ine ndinali kumangobwera ndi kumanena zomwe ine ndimagaliza kuti zinali zolondola, ndipo ndikumapitirira. Izo zinali kunja kwa mzere. Ndipo tsopano, zinayi zonse za Zisindikizo izo, ine ndinali nazo izo mwa pafupi ulaliki wa maminiti makumi awiri, zonse za izo. Okwera pakavalo anayi, a Chivumbulutso, ine ndinawaponya iwo onse pamodzi ndipo ndinati, “Kavalo mmodzi anapita mu kuyera,” ine ndinati, “mwinamwake ndiwo—m—m’badwo woyambirira. Ndipo kavalo wotsatira analowa mu njala,” ndiyeno nkumapitirira monga choncho. Koma, mai, pamene Mawu anatsegulidwa kwenikweni, Izo zinali mailosi mazana kwa izi.

18 Kotero, icho chikutikakamiza ife kuyang'anira ndi kuyembekezera. Ndipo mwinamwake inali yoti idzakhale nthawi iyi kuti tichite izo. Apo pakhoza kukhala zinthu zambiri zomwe zanenedwa, zomwe zikhoza kukhala zosagwirizanika ndi anthu ena. Koma ine ndikukhulupirira, pamene nthawi yaikulu yotsirizitsa ibwera, ndipo ife nkukumana naye Ambuye wathu, inu mudzapeza kuti Izo zinali zolondola. Izo—Izo—Izo ziri kwenikweni.

19 Tsopano, anthu amene ali ochokera kunja kwa mzinda, kuchokera kozungulira ku malo osiyana, kubwera muno kuchokera ku zigawo zosiyana ndi mafuko, momwe ine ndikuyamikira kudzipereka kwanu kuyenda mtunda wonse, ndi kutenga matchuthi anu. Ndipo ena a iwo opanda ngakhale malo woti akhalepo! Ine—ine ndikudziwa, chifukwa ine ndakhala wokhoza kuthandiza ena a iwo kupeza malo woti akhalepo. Wopanda ngakhale ndalama kuti azidyera, kapena china chirichonse, ndipo kotero...ndipo ngakhale kubwera, chonchobe, kuyembekezera chinachake kuti chichitika, kuti chisamalire za izo. Ndipo ndi chikhulupiriro chachikulu chotero mu iwo, kuti ziribe kanthu ngati iwo atapita wopanda chakudya, kapena ngakhale malo woti akhalepo, iwo akufuna kubwera kudzamva izo, zinthu izo zikuchitika, chonchobe. Uko nkuyima kwenikweni, inu mukudziwa. Ndipo aliyense wakhala basi mwathunthu!

20 Ine ndinakumana naye mulamu wanga kumbuyo uko, yemwe anali—a...ankamanga tchalitchi ndi njerwa, ndi zina zotero. Ndipo ine ndinali kumuwuza iye momwe ine ndinayamikira ntchito yake. Ine sindiri—womanga ndi njerwa, kapena kudziwa kanthu za izo. Koma ine ndimadziwa chomwe ngodya yowongoka ili, ndipo ngati iyo yamangidwa mwa mtundu wabwino.

21 Ndipo iye anati, “ine ndikuwuzani inu.” Iye anati, “Sipanakhalepo nthawi yoteroyo, nkomwe, yomwe iwe unawonapo chiyanjano chotero pakati pa anthu, pamene iwo onse akugwirira ntchito limodzi.”

22 M'bale Woods, M'bale Roberson, ndi aliyense amangodziyika mu malo awo, chirichonse. Ndipo m'bale yemwe—yemwe anayika masipikala,...ine ndikutanthawuza zowulutsira mawu pa gulu ndi chirichonse, mu mpingo. Iwo anati, “Chirichonse chinangogwira ntchito molondola.” Pamene iwo asowa chinachake, pamakhala munthu atayima pamenepo kuti achite icho. Kotero ziri...Mulungu ali mwathunthu mu dongosolo lonse. Ife tiri othokoza kwambiri chifukwa cha ichi.

23 Opereka kwakukulu ambiri mu mpingo, kuti athandize kuchita izi, wotero monga M'bale wathu Dauch ndi mlongo Dauch akhala apa, ndi ena ambiri omwe anapereka molemera ku cholinga ichi. Ndipo ine ndikuganiza, panthawi yake

yomwe, iwo osasowa npang'ono pomwe ndipo izo zonse kukhala zitalipiridwira. Kotero ife tiri oyamikira kwambiri kwa izo.

²⁴ Kumbukirani, ndi mpingo wanu, pakuti inu ndinu wantchito wa Khristu. Ndipo ndicho chomwe iwo wamangidwira pano, khomo lotseguka kuti lipange antchito, ndipo kwa antchito omwe ali kale antchito a Khristu, kuti abweremo ndi kusangalala iwoeni pozungulira chiyanjano cha Yesu Khristu. Ndipo ife tikufuna inu kuti mudziwe kuti aliyense ali wolandiridwa.

²⁵ Ndipo tsopano pamene inu mundimva ine nthawizina, pansi pa nthawi yakudzoza, kukhala ngati kung'ambira pansi katani pa bungwe, ine—ine sindikutanthawuza izo motsutsa abusa anu, kapena motsutsa m'bale aliyense, mlongo, mu mpingo. Chifukwa, kuwonjezera apo, Mulungu ali nawo anthu mu bungwe lililonse lomwe liripo. Koma Iye samalandira bungwe; Iye amalandira payekha wa mu bungwe. Ndipo a... Izo sizitengera bungwe.

²⁶ Chotero, pamene anthu akhala omangidwa kwambiri pozungulira bungwe, ndiye iwo sangakhoze kuwona kanthu kalikonse koma basi chimene mpingo ukunena, inu mukuwona. Ndipo icho chimapangitsa kusayanjana nawo ena, ndipo kali kachitidwe komwe Mulungu sakukondweretsedwa nako, ndipo icho chiri mchitidwe wa mdziko chosayikidwa konse ndi Mulungu.

²⁷ Kotero, tsopano, ine sindikutanthawuza munthu aliyense. Katolika, Chiyuda, chirichonse chomwe chingakhale, kapena—kapena Methodist, Baptist, Presbateria, bungwe lililonse, wopanda mabungwe, ndi—ndi wopanda zipembedzo, ndi onse, Mulungu ali nawo ana Ake atakhala mmenemo. Mukuwona? Ndipo nthawi zambiri ine ndikukhulupirira iwo ali kunjira uko ndi cholinga, kuti apereke Kuwala, kusololamo awo amene ali okonzedweratu kuchokera konse kozungulira kulikonse. Ndipo—ndipo pa tsiku lalikulu ilo, ife tidzawona ndiye, Mpingo wa Ambuye Yesu Khristu udzayitanidwira ku—ku nthawi ya kukumana kwakukulu mu mlengalenga, ndipo ife tonse tidzapita mmwamba kukakumana naye Iye. Ndipo ndiri—ndiri kuyembekezera ora limenelo

Tsopano, pali zambiri zomwe zikanakhoza kukhala zitanenedwa!

²⁸ Ndipo usiku uno, pa kutsiriza, usiku wotsekera, monga kawirikawiri, aliyense ali... Mu msonkhano wa machiritso, ine ndimapeza, pansi pa kuyembekezera zinthu zazikulu kuti zichitidwe mu msonkhano wa machiritso, umene umawapanga iwo kumangika, amanjenje. Ndiyeno ine ndikupeza chinthu chomwecho usiku uno, kuti aliyense ali pansi pa kuyembekezera kwa kuwona momwe... Ndipo usiku uliwonse, wakhala mwanjira iyo, pa kutsegula kwa Zisindikizo zimenezo.

²⁹ Tsopano ine ndikufuna kupanga izi momveka kwenikweni. Nthawi iliyonse, nthawi iliyonse yomwe Zisindikizo zabwera pa malo; chirichonse chomwe ine ndinakhulupirirapo pa Izo, ndipo ndawerenga za anthu ena, zakhala zosiyana kwa zomwe zabwera kwa ine mu chipinda.

³⁰ Ndipo malingaliro anga, pa nthawi ino . . . Chifukwa chomwe ine ndinakhala ndi msonkhano wa machiritso uja mmawa uno, chifukwa malingaliro a umunthu wanga akukhala kutali chotero kwa njira ya kaganizidwe kanga komwe. Ine ndayesera kukhala mu—mu chipinda mithunzi itakokeredwa pansi, ndipo nyali itayatsidwa. Ili liri tsiku lachisanu ndi chitatu. Ndipo osati ngakhale kukwera mu galimoto yanga, ku—kuti ndipite kulikonse.

³¹ Ine ndinachita kupita ndi abale ena, kumusi ku mabanki, kukasayina zipepala zina ndi zinthu, pa ndalama ndi zinthu zomwe zinabwerekedwa kwa mpingo uno. Koma ine—koma ine ndinabwera molunjika kumene mmbuyo, ndi kupita kukawerenga.

³² Ndipo chinthu chachirendo, sipanakhale munthu mmodzi ananena chirichonse. Kapena, kawirikawiri, iwo amagogoda, ndi kukoka, ndi pozungulira. Sipanakhale chinthu chimodzi. Icho chakhala chopambana kwambiri.

³³ Kumene ine ndakhala ndikudya, kwa M'bale Wood. Kawirikawiri malo awo amadzaza pozungulira ndi magalimoto. Ndipo iwo anali nawo anthu asanu ndi awiri kapena khumi anali oti abwere kudzakhala nawo iwo pa nthawi iyi, ndipo palibe mmodzi wa iwo anabwera.

³⁴ Ndiye, mmawa uno, ine sindidzawuyiwala mmawa uno, chisomo cha Mpulumutsi wathu kwa wantchito Wake wotopa, wofooka. Pamene, ine ndinali nditayankha funso la munthu wosawuka, ndipo, mwakukhoza kwa kulingalira kwanga, kumaganiza kuti ine ndinachita cholondola. Ndipo, zonse mwadzidzidzi, ngati kuti ine ndinali—ine ndinali nditatenga chinachake kwa mwana, ine ndinali wotsutsika kwambiri, ndipo sindinadziwe chimene icho chinali. Ndipo ine ndinaganiza, mwinamwake pokhala kuti ine ndinali kuthamangira kufika ku utumiki wamachiritso uja, mwinamwake winawake mosimidwa chotero akudwala, amene anali woti apemphereredwe pomwepo. Ndipo ine ndinafunsa osonkhana. Mu maminiti pang'ono, icho chinawululidwa. Ndipo winawake anati, “Kodi inu simuwerenga wanu—werenganinso phunziro lanu?” kapena chinachake. Ndipo nthawi imeneyo, ine ndinatenga kachidutswa kakang'ono ka pepala ndi kuwerenga izo kachiwiri, kuwona zomwe iko kanaanena. Ndipo ndinayang'ana pansi pa Bukhu, ndipo izo zinali palimodzi zosiyana, funso lomwe ine ndinali kuyankha. Mukuwona?

³⁵ Ine nditangopereka ichi kwa inu. Pamene Chauzimu chibweramo, ndilo lingaliro la Khristu. Inu mumakhala kutali kwambiri mutachoka ku kuganiza kwanu, mpaka, mu malingaliro anu omwe, ine...Ichi, inu...ine sindiri... Musati mundirole ine kuyesa kufotokoza izo, chifukwa ine sindingakhoze. Mukuwona? Ine sindingakhoze kuchita icho. Palibe aliyense angakhoze kuchita icho.

³⁶ Akanakhoza bwanji munthu uja, ndiye Eliya, kuyima pamenepo pa phiri, pansu pa Kukhalapo kwa Mulungu, ndi kukokera pansu moto kuchokera kumwamba, ndiyeno mvula pambuyo pake pomwe pa moto? Ndiyeno nkutseka miyamba, ndipo iyo sinavumbe kwa zaka zitatu ndi miyezi isanu ndi umodzi, ndi kupita mmbuyo momwe ndi kukayitana mvula, pa tsiku lomwelo! Ndipo pansu pa kudzoza kumeneko, momwe... Ndipo anatenga ansembe mazana anayi ndipo anawapha iwo; ndiyeno nkuthamangira ku chipululu, kufuwulira moyo wake, pa kuwopsyeza kwa mkazi mmodzi. Mukuwona? Yezebeli, iye analumbira kuti iye akanatenga moyo wake. Pamene, Ahabu ndi onse a iwo anali kumeneko, kukawona Kukhalapo kwa Mulungu ndi chozizwitsa chachikulu chitachitika. Mwawona, wake... Mzimu unali utamuchokera iye. Mu njira yachibadwa yake ya kaganizidwe, iye sanadziwe momwe angaganizire, mwawona. Iye sakanakhoza kudziganzira iyemwini.

³⁷ Ndipo, kumbukirani, Mngelo anamuyika iye ku tulo, ndipo anamupumitsa iye. Anamuwutsa iye, namupatsa iye mikate ina; ndiye nkumuyikanso iye ku tulo, ndipo nkumupumitsa iye; ndi kumuwutsa iye, ndi kumupatsa iye mikate ina kachiwiri. Ndipo ife sitikudziwa chomwe chinachitika kwa munthuyo, kwa masiku makumi anayi. Ndiye iye anakokedwa kubwerera mu mphanga, kwina kwake, ndipo Mulungu anamuyitana iye.

³⁸ Musati muyesere kufotokoza Chauzimu icho. Inu simungakhoze kuchita izo. Mukuwona? Chinthu chokha choti muchite, ndicho basi kupita patsogolo pomwe. Ndipo ine ndimayesa kudzipanga ndekha kumveka monga ine ndingathere, koma kuchokera apo ine ndidza...ine ndikuganiza sindidzayesanso izo kachiwiri. Inu mudzangokhulupirira mwamtheradi, kapena ayi. Ndipo ndiri...Inu mudzawona, patsogolo pang'ono, chifukwa chake.

Tsopano, ine ndayesera kukhala woona mtima. Mulungu akudziwa izo.

³⁹ Ndipo funso lija mmawa uno. Ine ndimayesa kuyankha ilo basi moona mtima momwe ine ndimadziwira. Ine ndinangowerenga gawo loyamba la ndime, ndipo ilo linali... sizikanakhala ziri zolondola. Koma Mzimu Woyera, kumvetse kuti ine...malingaliro anga...Mwaona, penyani, masiku awiri kapena atatu otsiriza, chomwe chakhala chikuchitika. Mwawona, ine—ine ndinatcha mazana asanu ndi awiri...

“zikwi zisanu ndi ziwiri,” mazana asanu ndi awiri. Mmawawu, ndinali kuyesa, ndipo icho chinagwidwa ndi anthu, onani, ndipo icho chinasonyeza kuti inu munali tcheru. Tsopano, limodzi lina, pamene ine ndimayesa kunena kuti “nkhunda,” ndipo ine ndinayitcha iyo mwanawankhosa; koma ine ndinachigwira icho pomwepo. Ndiyeno, apa, limodzi ine sindinagwire pa icho, Mzimu Woyera unatembenuka mmbuyo pomwepo ndi kundiyitanira ine kwa icho.

⁴⁰ Ndiko kutsimikizira kwapawiri kuti zinthu izi ndi zolondola. Izo ziri. . . Mulungu ali kuyang’anirapo, kuti awone kuti Izo nzolondola. Uko nkulondola. Iye akufuna kutero. Iye akufuna inu kuti mudziwe kuti Ichu ndi Chowonadi.

⁴¹ Iye ali Mmodzi yemwe akutumiza Izo, chifukwa izo zedi sizinali. . . Izo zinali basi ngati zochuluka kwa ine, pophonzira, monga izo zakhalira kwa inu. Ndipo kotero ife tiri. . . ine ndiri woyamikira kwambiri chifukwa cha chi—chi—chidziwitso, kudziwa tsopano za Ambuye, ora limene ife tikukhalamoli; mwawona, kukhala mu nthawi yotsiriza kumene, kusanafike kupita kwa Mpingo. Tsopano basi. . .

⁴² Ife takhala tikulankhula, kotero tiyeni tingopempha madalitso Ake pa Mawu kachiwiri.

⁴³ Atate athu Akumwamba, apa pakubwera usiku wopambana uja, ora lopambana lomwe chinthu chopambana chachitika. Ichu chakhala ponse pozungulira anthu. Ndipo, Atate, ine ndikupemphera kuti usiku uno zikadziwike, kupyola mthunzi wa kukayikira, kwa mitima ya anthu ndi malingaliro, kuti iwo akanadziwa kuti Mulungu akanali pa Mpandowachifumu, ndi kuti Iye akanakonda anthu Ake.

⁴⁴ Ndipo liri ora, ora lomwe dziko layembekezera kuliwona, liri tsopano kuyandikira, pakuti ilo likulirira chiwombolo chathu. Ife tikukhoza kuwona zipangizo zakonzeka kulibweretsanso ilo. Ife tikukhoza kuwona zipangizo zakonzeka kuwubweretsa Mpingo mu Kukhalapo kwa Khristu. Ife tikukhoza kuwona m—Mkwatibwi akutenga mawonekedwe, akuvala chovala cha chikwati, kukonzekera. Ife tikukhoza kuwona magetsi akuthwanima. Ife tikudziwa kuti tiri pa mapeto.

⁴⁵ Tsopano, Atate Akumwamba, pamene ichi chikupita patsogolo tsopano kukalalikira, kapena kukaphunzitsa pa chochitika chachikulu ichi, champhamvu chimene chinachitika mu Ulemerero, zaka zina zikwi ziwiri zapitazo, ndipo chinaperekedwa kwa mtumwi wokonedwa wamkulu, Yohane. Ndipo usiku uno ife tiri oti tilankhule pa Ichu. Lolani Mzimu Woyera ubwere patsogolo tsopano mu Mphamvu Yake yopambana ya vumbulutso, kuti Iye akhoze kuwulula kwa ife chinthu icho chimene Iye akufuna ife kuti tidziwe, monga Iye wachitira mu usiku ungapo wapitawo. Ife tikudzipereka tokha kwa Inu, palimodzi ndi Mawu, mu Dzina la Yesu. Amen.

46 Tsopano, pamene inu mukufuna kutsegula, mwinamwake, mu Mabaibulo anu. Ndipo iyi ili chabe ndime yayifupi, ndime imodzi ya Lemba. Koma, iyo ili ndime yotsiriza, iyo ikupezeka . . . Chisindikizo chotsiriza, kani.

Tsopano, usiku watha ife tinali kulankhula pa Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi.

47 Chisindikizo Choyamba, kukhala wotsutsakhristu akuwonetsedwa. Nthawi yake inapita nidusa, ndipo ife tinawona momwe iye anatulukira.

48 Momwe Chamoyo chimene chinawonetsedwa, pa Mphamvu ya Mulungu chimene chinapita ndi mphamvu ya wotsutsakhristu, kukamenyana naye iye! Ine sindikukhulupirira kuti apo pangakhale funso mu malingaliro a aliyense pa izo.

49 Ndiye ife tinapeza kuti, ndi mwamsanga zitatha izo, m'badwo wa mpingo uwo, Zamoyo izo zinapita.

50 Zinatha kupyola, ife tinapeza kuti, ife tinasintha, chithunzi chonse pamenepo, palibenso Zamoyo zomwe zikutuluka. Mukuwona? Koma, uko kunali kuwonetsa, kubwera patsogolo, uko mu nthawi ya Chisawutso, utatha Mpingo kutuluka.

51 Zikugwirizana mwangwiro bwanji izo ndi mibadwo ya mpingo! Ine sindikuwona dontho limodzi, chinthu chimodzi chimene sichinagwirizane mwangwiro, ngakhale ku mibadwo ndi chirichonse, ndi nthawi. Taganizani za izo. Izo zikusonyeza, uyo anayenera kukhala Mulungu anachita izo. Malingaliro a munthu sakanakhoza kukwanitsa izo. Ndipo tsopano ife tikupeza izo kuti, nafenso, ife . . .

52 Ambuye atilore ife titenge Lemba, Lemba Loyera, chimene Yesu anati chikanadzachitika. Ndipo ife tikanachipeza bwanji icho konse? Ndipo apa, chikubwerapo ndi kuwulula, ndi kuchibweretsa icho chimodzimodzi basi. Ulaliki wake pamenepo, poyankha izo, kukubweretsa chimodzimodzi pa nsonga, zisanu ndi chimodzi za Zisindikizo, koma Iye anadumpha Chachisanu ndi chiwiri. Mukuwona?

53 Ndiye pamene Zisindikizo zinatsegulidwa, Mulungu, zindikirani apa, Iye anadumpha kuwulula ngakhale chiphiphiritso chirichonse cha Chachisanu ndi chiwiri Icho. Mukuwona? Ndicho chinsinsi changwiro ndi Mulungu. Zindikirani. Tsopano ife tiwerenga mu Baibulo, mu—Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri. Chimene chikupezeka mu Chivumbulutso, mutu wa 8.

Ndipo pamene iye anali atatsegula chisindikizo chachisanu ndi chiwiri, munali chete m'mwamba pafupi kadanga ka theka la ora.

54 Ndipo ndizo zonse ife tiri nazo pa icho. Tsopano ife tizindikira.

55 Ndipo kuyesa kusakhala motalika kwambiri, chifukwa ambiri a inu mukhala pa msewu, komabe, usiku uno, kumapita kwanu. Ndipo ine ndinaganiza kachiwiri, kukhala ndi msokhano wa machiritso mmawa uno, chimene chikanakulolani inu kupita mmawa, simukanasowa kuyembekezera. Ndipo tsopano ife. . .

56 Ndipo ine, nanenso, ine ndiyenera kupita ku—ku Tucson, Arizona, kumene ine ndimakhala. Ndipo ndiko kwathu tsopano. Ndiyeno ine—ine ndikufuna kuti ndibwerere kuno, Ambuye akalola, kuzungulira. . . Banja likufuna kubwerera kwa masiku pang’ono mu Juni. Ndipo, tsopano, mwinamwake ine ndidzafika pokomana nanu inu nonse kumusi kuno, msonkhano mu nthawi imeneyo.

57 Utumiki wanga wotsatira wosankhidwa uli Albuquerque, New Mexico. Ine ndikuganiza ndi pa naini, teni ndi leveni. Ine ndidzakhala kumeneko Lachinai ndi Lachisanu Labwino. Kotero, ine ndimati ndikhale ndi chinthu chonse, ndipo ine ndinali nawo malonjezo ena komwe ine sindinakhoze kuwakwanitsa iwo mpaka nthawi imeneyo, kotero ine ndidzakhala ndi Lachinai usiku ndi Lachisanu usiku, ku Albuquerque, New Mexico.

58 Ndiyeno—ndiyeno w—wotsatira, wodziwika, pafupi, uli mwakungolankhula. Ife sitikudziwa motsimikiza. Ndiko kuti ndikhale ndi amzanga abwino, a—a gulu la *The Midnight Cry*, ku. . . kumtunda ku Southern Pines, North Carolina.

59 Ndipo iwo ali pa foni mkati umo tsopano, omwe, iwo atumiza matelegiramu, uthenga, ndi chirichonse, ndipo kubwera pafupi apa, kwa gulu lina la anthu, ku Little Rock; la anthu a Dzina la Yesu omwe ine ndinali nawo misonkhano, cha ku Cow Palace chirimwe chatha. Iwo ali ndi msonkhano wawukulu wawo ku Little Rock, Arkansas. Ndipo iwo akhala, kuyambira chaka chatha, kufuna pafupi usiku umodzi. Kapena, akufuna wonse wa iwo, koma iwo akhoza kukhalabe okonzeka ngakhale kwa usiku umodzi. Ndipo kotero ine ndinawawuza iwo, posadziwa basi choti ndichite, ine ndinati iwo akhoza kulengeza izo, “mwakungolankhula.” Ndiye iwo adzadziwitsa izo mtsogolo pang’ono.

60 Kodi iye amangondiyitana? A-ha. Chabwino. Mukuti chiyani? [M’bale akuti, “Hot Springs.”—Mkonzi.] Hot Springs, ndi choncho? Ine ndinalakwitsa. [“Twente folo.”] Twente folo ya. . . [“Meyi.”] Meyi? [Wina akuti, “Twente folo mpaka twente eyiti ya Juni.”] Twente folo mpaka twente eyiti ya Juni. Tsopano izo zalengezedwa, “mwakungolankhula,” izo ziri, “ngati chiri chifuniro cha Ambuye.” Mwawona? Ndidzatero. . .

61 Apa pali chifukwa chimene ine ndimakondera kuchita zinthu izo. Inu mudzaphunzira mtsogolo pang’ono, tsopano, mwaona. Pamene ine ndipita ku malo, ine ndimakonda kuponda phazi langa pansi pamenepo, podziwa kuti Mulungu

anati, “Pitani uko.” Ndiye ngati mdani awuka kulikonse, ine ndimati, “Ine ndiri pano mu Dzina la Ambuye Yesu. Sunthira mmbuyo basi!” Mukuwona? Mukuwona? Mukuwona? Ndipo iwe uli—iwe uli wotsimikiza, malo ako, mwawona. Pamene Iye akutumiza iwe kulikonse, Iye akusamalira iwe. Mukuwona? Koma ngati iwe upita, molingalira, ndiye ine sindikudziwa; Iye mwina sangakhale kumeneko. Koteri ine—ine ndikufuna kukhala wotsimikiza momwe ine ndingakhalire. Ine ndakhala ndikutenga yambiri imene Iye sanandiwuze kuti ndiyitenge, koma ine—ine ndimakonda kukhala wotsimikiza momwe kungathekere. Ambuye akudalitseni inu nonse tsopano.

⁶² Tsopano, tsopano ife tikuzindikira, iyi pokhala ndime imodzi chabe apa, ife tikanafuna kuchita chinachake chaching’ono chabe—chaching’ono ng’ono tisanafike apa. Inu muzindikira, ife tinalumpha mutu wa 7. Mutu wa 6 ukutsirizitsa Chachisanu ndi chimodzi, Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi. Koma pakati pa Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi ndi Chachisanu ndi chiwiri, pali chinachake chimene chikuchitika. Mukuwona? Ndipo momwe—momwe mokoma izo zayikiridwa basi pa malo ake oyenera, pakati pa mutu wa 6 ndi wa 7. Tsopano inu muzindikira mu mutu wa 7, ife tinazindikira, pakati pa Chachisanu ndi chimodzi ndi Chachisanu ndi chiwiri, pali kadanga. Kadanga, pakati, pa mutu wa 6 ndi wa 7 wa Bukhu la Chivumbulutso, ndipo pali pakati pa Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi ndi Chachisanu ndi chiwiri pamene danga ili likuperekedwa. Tsopano ife tikufuna kuzindikira ichi. Ndi chofunikira kwambiri kuti ife tizindikire kanthawi kakang’ono aka.

⁶³ Tsopano kumbukirani, utatha mutu wa 4 wa Chivumbulutso, Mpingo wapita. Atatha—okwera pakavalo anayi atapita kunja, Mpingo wapita. Mukuwona? Chirichonse chimene chinachitika kwa Mpingo, chinachitika mpaka pa mutu wa 4 wa Bukhu la Chivumbulutso. Chirichonse chimene chinachitika mu kusuntha kwa wotsutsakhristu, chinapitirira mpaka ku mutu wa 4. Ndipo Chisindikizo Chachinai cha Chivumbulutso, zonse za wotsutsakhristu ndi Khristu, zinatsirizika. Ndipo wotsutsakhristu akubwera ku chiwonongeko chake, ndipo ndi ankhondo ake; ndipo Khristu akubwera ndi ankhondo Ake.

⁶⁴ Iyo ndi nkondo yakale imene inayamba kale mmbuyo, kuseri kwa nthawi. Ndiyeno iwo anali . . . Satana ndi angelo ake anakankhidwira kunja, ndiyeno iwo anabwera ku dziko lapansi. Ndipo nkondoyo inayambika kachiwiri, chifukwa Eva anaswa chotchinga kuchoka kumene iye anali wopatulidwa, kuseri kwa Mawu a Mulungu. Ndipo kuchokera pa ora lomwelo, Satana anapambana nkondo pa Mawu a Mulungu, chifukwa mmodzi wa omumvera Ake, wofookayo, analekerera zigwiriro. Ndipo ndicho chimodzimidzi momwe iye wapambanira nkondo

nthawi iliyonse, zakhala chifukwa mmodzi wa omumvera Ake analekerera chigwiriro kuchoka ku Mawu.

65 Ndipo icho chinachitika mu m’badwo wa mpingo wotsiriza uwu, kupyolera mu kachitidwe ka bungwe. Kamene, mpingo weniweni, wona, woyera wa Mulungu wamoyo, wokhala ndi wokwera wabodza, sunakhoze kulandira Mawu, ndipo unatembenuza mpingo kuchoka ku Mawu kupita ku nthano.

66 Tsopano, ndi angati akudziwa kuti ndi nthano zomwe mpingo wa Roma Katolika wamangidwirapo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Kodi iwo amavomereza izo? Mwamtheradi. Zedi. Ndithudi, iwo amavomereza izo. Sindizo zonse. Akatolika, zedi, sichingapweteke kumverera kwawo pang’ono, chifukwa iwo amadziwa izo. Iwo angowonjezera imodzi yatsopano, apa osati kale litali lapitalo, kuti Mariya anawukitsidwa. Inu mukukumbukira iyo, pano zaka pang’ono zapitazo, pafupi zaka khumi. Ndi angati akukumbukira izo? [“Ameni.”] Pepala, mmenemo. Zedi. Mukuwona? Chirichonse, “nthano” yatsopano. Mwawona, ziri zonse nthano, osati Mawu. Mukuwona?

67 Wansembe, pa kulankhulana posachedwapa, iye anati, “Bambo Branham,” iye anati, “Mulungu ali mu mpingo Wake.”

Ine ndinati, “Mulungu ali mu Mawu Ake.”

Iye anati, “Ife sitiyenera kumatsutsana.”

68 Ine ndinati, “Ine sindikutsutsa. Ine ndikungolankhulapo neno. Mulungu ali mu Mawu Ake. Uko nkulondola. ‘Aliyense amene ati adzachotse chirichonse kwa Iwo, kapena kuwonjezera chirichonse kwa Iwo,’ anatero Mawu.”

69 Iye anati, “Chabwino, Mulungu anapereka... Khristu anawupatsa mpingo Wake mphamvu, ndipo anawawuza iwo: chirichonse chimene iwo ati amange pa dziko lapansi, chikhala chomangidwa Kumwamba; ndipo chiyani. . .”

Ine ndinati, “Izo ziri chimodzimodzi Chowonadi.”

70 Iye anati, “Ife tiri nazo, pa . . . pa mfundo iyi, kuti ife tiri nayo mphamvu yomasula tchimo.”

71 Ndipo ine ndinati, “Ngati inu mungachite izo mwanjira yomwe zinaperekedwera kwa Mpingo, ndi momwe iwo ankachitira izo, ine ndivomereza izo. Ngati inu muchita, pali madzi apa, kuti ‘mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu kwa chikhululukiro cha machimo anu,’ mwawona, osati mwa wina kumakuwuzani inu kuti machimo anu achotsedwa.” Mukuwona? Mukuwona? Ndizo chimodzimodzi.

72 Muyang’aneni Petro ndi mafungulo, pa Tsiku la Pentekoste. Kumbukirani, iye ali nawo mafungulo omwe iwo akuwanena. Ndipo a—anthu anati, “Amuna ndi abale, ife tingakhoze kuchita chiyani kuti tipulumutsidwe?”

73 Petro anati, “Lapani, mmodzi aliyense wa inu, batizidwani mu Dzina la Yesu Khristu” (za chiyani?) “kwa chikhululukiro cha machimo, ndiyeno inu mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera. Pakuti lonjezo liri kwa inu, ndi kwa ana anu, iwo omwe ali kutali, ngakhale onse amene Ambuye Mulungu wathu adzawayitana.” Uko nkulondola. Kotero icho chikukhazikitsa izo kwa nthawizonse. Izo zonse zatha. Icho chinachita izo.

74 Tsopano, koma, inu mukuwona, wotsutsakhristu akubwera mkati, monga momwe ife tachijambulira icho ndi kuchiwonetsa icho. Ndi vumbulutso lotani! Mai, mai! Ndipo kuganiza, zaka zonse izi, ife tachiwona icho chikusunthira mmwamba. Ndipo apa chiri mwamtheradi, molunjika PAKUTHI ATERO AMBUYE.

75 Tsopano, ndipo ife tikuzindikira kadanga aka tsopano, pakati pa, mutu wa 6 ndi wa 7. Tsopano, mutu wa 7 wa Chivumbulutso, apa pali k—k. . .kuwulula chochitika. Izo siziri apa mwachabe. Izo sizinayikidwemo, pakati pa izi, mwachabe. Mukuwona? Izo ziri apa kwa cholinga, ndipo ndilo vumbulutso lomwe likuwulula chinachake. Zindikirani momwe mwachinsinsi ndi mwamasamu zikukwanira mu Lemba kumene! Mwawona? Chimodzimodzi.

76 Kodi inu mumakhulupirira mu masamu a Mulungu? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ngati inu simutero, inu muli motsimikiza otayika mu. . .Inu motsimikiza mutayika mu Mawu, ngati inu muyamba kuyika folo kapena sikisi, kapena—kapena chinachake, pambali pa mawu a mwamasamu okha kuyenda mwa dongosolo. Inu ndithudi mudzakhala ndi chowonekera chanu, ng’ombe ikudya udzu pamwamba pa mtengo, penapake. Inu ndithudi zizakutherani. Chifukwa, Mulungu samatero. . .Mawu Ake onse amayenda kwathunthu mu—mu—mumasamu. Inde, bwana. Mwangwiwo, mwangwiwo zedi! Palibe bukhu lina lolembedwa monga Ilo, monga Ilo, angwiwo chotero mu masa—masamu.

77 Tsopano, m—mutu wa 8 ukuwulula kokha chowoneka cha—chowoneka cha Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri, pamene palibe kanthu kalikonse komwe kakuwululidwa, tsopano, palibe chinthu. Izo sizinawululidwe mu Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri. . .tsopano, chiribe chochita ndi mutu wa 7 wa—wa Chivumbulutso. Ndiko kuwulula, kwa Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri, kuli duu mwangwiwo. Ndipo ngati ine ndikanangokhala nayo nthawi. . .Ine ndiyesa malo angapo, kuti ndikuwonetseni inu.

78 Njira yonse mmbuyo, kuchokera ku Genesis, ichi Chachisanu ndi chiwiri mut- . . .kapena Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri ichi chiri—chiri—chiri kunenedwa. Kuchokera kuchiyambi komwe, mu Genesis, ichi Chachisanu ndi chiwiri Chis- . . .

79 Zisindikizo izi zimasunthira mmwamba kumene. Kodi inu simunakhoze kukumbukira, mmawawu, pobweretsa zinthu izi?

Ndipo yang'anani, usiku uno, pozibweretsa izo. Ndipo inu mupeza, pamene izo zifika ku Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri icho, iye akudukiza. [M'bale Branham akhwatcha chala chake kamodzi—Mkonzi.] Inde.

⁸⁰ Yesu Khristu, mu kulankhula, Iyemwini, ananena za nthawi yotsiriza. Ndi pamene Iye anafika. . . Analankhula zonse Zisindikizo zisanu ndi chimodzi. Pamene Iye anafika ku Chachisanu ndi chiwiri, Iye anayima. Ndi zimenezotu, onani. Ndi chinthu chachikulu.

⁸¹ Tsopano, tsopano, ife tilankhula apa tsopano pa mutu uwu wa 7, miniti yokha, ku—kukhala ngati kuchilumikiza icho mkati, pakati pa Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi ndi Chachisanu ndi chiwiri. Chifukwa ndicho chipangizo chokhacho chomwe ife tiri nacho kuti tipitirire nacho, pakali pano, chiri Chachisanu ndi chimodzi. . . pakati pa Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi ndi Chachisanu ndi chiwiri, kuli kuyitanidwa kwa Israeli.

⁸² Tsopano, ine ndiri ndiri nawo amzanga abwino a Mboni za Yehova ambiri amene akhala apa, ndizo zonse. . . kapena akhala ali. Mwina ena a iwo akadali a Mboni za Yehova. Koma iwo nthawizonse akhala akuyika, Bambo Russell anatero, zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi awa, kukhala mu Mkwatibwi wa Khristu wauzimu. Mwawona? Iwo. . . Sindiwo.

⁸³ Izo ziribe chochita mu m'badwo wa mpingo, nkomwe. Iwo ali mwamtheradi Israeli. Tsopano, ife tiwerenga mu maminiti pang'ono. Tsopano, kadanga aka, pakati pa Chachisanu ndi chimodzi. . . Zisindikizo, ziri kuyitana ndi kusindikiza kwa Ayuda zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi oyitanidwa mu nthawi ya Chisawutso, Mpingo utatha kupita. Mwawona? Ziribe kanthu kochita nawo m'badwo wa mpingo, nkomwe. O, kuyitanidwa, ndipo mwangwiro mwa chiyanjano ndi Lemba. Masabata atatu ndi theka otsiriza a Daniele, operekedwa kwa "anthu" a Danieli, onani. Osati Amitundu, kwa "anthu" a Danieli, ndipo Danieli anali Myuda!

⁸⁴ Tsopano zindikirani, Israeli, Israeli amakhulupirira aneneri ake okha, ndipo, iwo atayamba kutsimikiziridwa.

⁸⁵ Ndipo palibe paliponse kupyola mu m'badwo wa mpingo, kuyambira mu Mpingo woyambirira wa utumwi, kuti mpingo wa Chiprotetanti unayamba wakhala naye mneneri. Ndiwuzeni ine yemwe iye anali, ndipo ndiwonetseni icho kwa ine. Palibe! Iwo anali naye, mu m'badwo woyambirira wa utumwi, mmodzi wotchedwa Agabasi, amene anali mneneri wotsimikiziridwa. Koma mu. . . Pamene Amitundu analowa mkati, mu cholowa cha Mulungu, ndipo Paulo anatembenukira kwa Amitundu. Atatha Petro, monga ife tinawerengera usiku watha, anali atalandira kuchokera kwa Ambuye, kuti, "Iye anali kuwatenga a—anthu kuchokera kwa Amitundu, kwa

Dzina Lake, Mkwatibwi Wake,” ndiye iwo sanakhalepo naye, pa masamba a mbiriyakale, mneneri Wamitundu. Tsopano inu mungobwerera mmbuyo kupyola mu mbiriyakale ndipo mupeze. Chifukwa? Chimodzimodzi, izo zikanakhala zosiyana kwa Mawu. Chimodzimodzi.

⁸⁶ Pamene woyamba anatuluka, anali mkango, amenewo anali Mawu a mneneri.

Wotsatira anapita apo, anali ntchito, nsembe.

Wotsatira kubwera apo, anali kukanika kwa—kwa munthu.

⁸⁷ Koma ife talonjedwa, mu tsiku lotsiriza, kuti izo zidzabwerera kwa Mpingo kachiwiri, kwa phindu la kuwongola onse amene asocheretsedwa, aphonya, osakonzedwa, asiyidwa osakonzedwa. Pakuti, zanenedweratu apa kuti Uthenga wa mngelo wa chisanu ndi chiwiri udzatsiriza zinsinsi za Mulungu. Ndipo, ndiye, ife tapita kupyola mu Izo zonse. Ife tikuwona kuti Izo ziri mwangwiro mu chiyanjano nalo Lemba. Ndicho chifukwa chake.

⁸⁸ Tsopano, kodi inu mukanakhoza kulingalira, pamene munthu uyu abwera powonekera? Pamene iye atero, kumbukirani, zidzakhala zonyozeka kwambiri ndi zinthu, mpaka mipingo idzaphonya izo njira zotalikitsa. Ndipo kodi mukanakhoza inu kulingalira, mipingo, ikadali pansi pa mwambo wa okonzanso, ukanadzalandira konse mneneri wochokera kwa Mulungu, yemwe akanadzakhala molimba motsutsa zophunzitsa zawo ndi mabungwe?

⁸⁹ Tsopano, pali munthu mmodzi yekha yemwe akanakhoza kukwaniritsa icho, Mzimu umodzi wokha umene unakhalapo konse pa dziko lapansi, umene ine ndikuwudziwa. Ukanakhoza mwina kukhala... Iye anayenera kukhala Eliya, mu nthawi yake. Ndipo izo zinanenedweratu kuti zikanadzakhala, zomwe sikanthu koma Mzimu wa Khristu.

⁹⁰ Pamene Khristu anabwera, Iye anali chidzalo. Iye anali Mneneri. Iye anali m—Mulungu wa aneneri. Mukuwona? Mukuwona?

⁹¹ Khristu, penyani momwe iwo anamudera Iye. Koma Iye anabwera chimodzimodzi momwe Mawu anati Iye adzabwera. Koma pokhala kuti Iye anali Mneneri, iwo anadzichititsa mwano okha kuchoka ku Ufumu wa Mulungu, powutcha Mzimu wa Mulungu, umene unali kuzindikira za mu mtima ndi zina zotero, “mzimu woyipa.” Anati, “Iye anali i—Iye anali wam’bwebwe, kapena mdierekezi,” ndi izo.

⁹² Wam’bwebwe ndi mdierekezi, mwaona, mzimu wa Mdierekezi. Ndithudi. Kodi inu mumadziwa izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—MKonzi.] Mwamtheradi. Kunena—mwam’bwebwe kuli kukopera kwa mneneri, chimene mwamtheradi chiri mwano pamaso pa Mulungu.

93 Tsopano zindikirani. Kuyitanidwa, mwa mgwirizano wangwiro ndi Malemba, a zaka zitatu ndi theka limodzi zotsiriza za Daniele.

94 Zindikirani, Israeli wokhulupirira—okhulupirira okha akuwuzidwa, mu Chipangano Chakale, kuti akhulupirire aneneri awo atatha mneneriyo kutsimikiziridwa. “Ngati pakhala mmodzi pakati pa inu, yemwe ali wauzimu kapena mneneri, Ine Ambuye Wanga-...Mulungu wanu ndidzadzidziwitsa Ndekha kwa iye ndi kulankhula kwa iye mmasomphenya, ndi kupyolera mmaloto, kumasulira maloto.” Winawake akakhala nalo loto, mneneri adzakhala wokhoza kulimasulira ilo. Ndipo ngati—ngati iye ali ndi masomphenya, iye alankhula iwo. “Ine ndidzadzizindikiritisa Ndekha kwa iye kupyolera mmasomphenya ndi maloto, kudzizindikiritisa Ndekha. Ndipo ngati chimene iye anena chifika pochitika, ndiye mvereni mneneri ameneyo, chifukwa Ine ndiri ndi iye. Ngati sizichitika, ndiye musamuwope iye nkomwe.” Eya. Uko nkulondola. “Chokanipo, ingomusiyani iye yekha, mwawona.” Tsopano ndizo...

95 Tsopano, Israeli nthawizonse akhulupirira izo. Ndipo kodi inu simukuwona? Chifukwa chiyani?

Tsopano ine ndikufuna inu mumvetse phunziro ili bwino, usiku uno, tsopano.

96 Bwanji? Chifukwa, ndilo langizo lochokera kwa Mulungu, kwa iwo. Ine sindikusamala kaya Amitundu atenga matraki ochuluka bwanji kukamwaza kumeneko. Ine sindikusamala kaya inu mupita mochuluka chotani kupyola mu Israeli ndi Baibulo pansi pa mkono wanu, kutsimikizira *izi, izo*, kapena *zina*; iwo sadzalandira konse kanthu koma mneneri. Ndizo chimodzimodzi zolondola. Pakuti, mneneri ali mmodzi yekhayo yemwe angakhoze kutenga Mawu Auzimu ndi kuwayika Iwo mu malo Ake, ndipo nkukhala mneneri wotsimikiziridwa. Iwo adzakhulupirira izo. Uko nkulondola.

97 Pamene ine ndinali kulankhula kwa Myuda cha kuno ku Benton Harbor, pamene John Rhyn uja, pokhala wakhungu moyo wake wonse, pafupifupi, analandira kupenya kwake. Iwo ananditengera ine kumeneko, nyumba ija ya Davide. Ndipo rabbi uyu anatuluka ndi ndevu zake zazitali. Iye anati, “Ndi mwa ulamuliro wanji inu munamupatsira John Rhyn kupenya kwake?”

Ine ndinati, “Mu Dzina la Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu.”

98 Iye anati, “Izo zikhale kutali kuti Mulungu nkukhala ndi Mwana!” Mukuwona? Ndipo iye anati, “Inu anthu simungakhoze kumudula Mulungu mu zidutswa zitatu ndi kumupereka Iye kwa Myuda. Kupanga Amulungu atatu kuchokera mwa Iye; inu ndinu gulu la achikunja!”

99 Ine ndinati, “Ine sindimamudula Iye mu zidutswa zitatu.” Ine ndinati, “Rabbi, kodi chingakhale chinthu chachirendo kwa inu kuti mukhulupirire mmodzi wa aneneri anu kuti ananena chinachake cholakwika?”

Iye anati, “Aneneri athu samanena kanthu kolakwika.”

Ine ndinati, “Ndi ndani yemwe Yesaya 9:6 ankamunena?”

Iye anati, “Mesiya.”

100 Ine ndinati, “Ndiye, Mesiya adzakhala Mneneri-Munthu. Nkulondola uko?”

Anati, “Inde, bwana. Uko nkulondola.”

101 Ine ndinati, “Ndiwonetseni ine pamene Yesu anaphonya izo.” Iye anati. . . Ine ndinati, “Ndi ubale wanji Mesiya-Mneneri ati adzakhale nawo kwa Mulungu?”

Iye anati, “Iye adzakhala Mulungu.”

Ine ndinati, “Uko nkulondola. Tsopano inu muli nazo izo pa Mawu.”

102 Kotero ndithandizeni ine, Myuda uyo atayima pamenepo ndipo misozi yake ikutsika mmasaya mwake, anati, “Ine ndidzakumvani inu nthawiyina mtsogolo.”

Ine ndinati, “Mphunzitsi, inu mukukhulupirira zimenezo?”

103 Ndipo iye anati, “Penyani,” iye anati, “Mulungu ali wokhoza mwa miyala iyi kuwukitsa ana kwa Abrahamu.” Ine ndinadziwa kuti iye anali mu Chipangano Chatsopano.

Ine ndinati, “Kulondola, Rabbi! Tsopano bwanji zimenezo?”

104 Iye anati, “Ngati ine ndikanalalikirira zimenezo, ine ndikanakhala kumusi uko,” inu mukudziwa kumene malo awo akukhala pa phiri kumeneko, “kumusi uko mu msewu, kupempha chakudya changa.”

105 Ine ndinati, “Ine kuli bwino ndikhale ndiri kumusi uko ndikupempha chakudya changa.” Myuda akadali nawo manja ake pa ndalama, inu mukudziwa. Mukuwona? Mukuwona? “Ine kuli bwino. . .” Ndipo dzina lake mu golide, pa. . . ine ndinati, “Ine kuli bwino ndikhale ndiri kumusi uko, ndikudya mikate yamchereyo ndi kumamwa madzi a mkhwawa, ndipo kumadziwa kuti ine ndinali mu chiyanjano naye Mulungu, ndi zowona; kuposa ine ndikanakhala kuno ndi dzina langa pa nyumba iyo, mu zolemba za golide monga choncho, ndi kumadziwa kuti ine ndinali kutali ndi Mulungu. Ine nkumadziwa izo.” Iye sakanamveranso kwa ine konse, kotero iye analowa mkati.

106 Koma ndi zimenezo. Inu simungakhoze kumudula Mulungu pawiri kapena zidutswa zitatu, zotchedwa “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera,” ndi kupanga Amulungu atatu ndi kumupereka iye kwa Myuda. Lamulo lake lomwe liri, “Iwe sudzakhala nayo milungu yina patsogolo pa Ine. Ine ndine Yehova Mulungu

wako.” Kodi Yesu ananena chiyani? Yesu anati,” ‘Mverani inu, O Israeli, Ine ndine Ambuye Mulungu wanu, Mulungu mmodzi.’” Osati atatu; inu simungapereke izo kwa iwo. Ayi. Palibe mneneri yemwe ati adzalankhule konse za Amulungu atatu. Ayi. Palibe. Inu simudzamva za izo. Ayi, bwana. Icho nchikunja ndi kusapembedza monga komwe izo zinachokera. Inde, bwana.

¹⁰⁷ Zindikirani. Koma aneneri awa adzabwera. Osati kokha icho. . . M—mneneri, tsopano, ndi Chivumbulutso 11. Ife tawerenga zina za izo. Ndipo ine ndikufuna inu mukawerenge izo pamene mukuwerenga, pa matepi ndi zina zotero. Iwo ali mwamtheradi aneneri otsimikiziridwa, mwa chizindikiro cha aneneri. Ndiye Israeli akamva izo.

¹⁰⁸ Tsopano, kwa inu, amzanga a Mboni za Yehova, mvetsani tsopano kuti awa, zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi, alibe chochita naye Mkwatibwi. Palibe chidutswa chimodzi cha Lemba kuti chithandizire zimenezo. Ayi, bwana. Iwo siali ayi. Iwo ali Ayuda. Osankhidwa omwe akuyitanidwa mu nthawi ya zaka zitatu ndi theka zotsiriza za masabata makumi asanu ndi awiri a Daniele. Tsopano ndizo. . .

¹⁰⁹ Ine—ine ndikubwerezabe izi. Osati mochuluka kwambiri kwa inu nonse apa, koma, onani, anthu, matepi awa amapita kulikonse, inu mukuwona. Ndipo inu mukumvetsa izo. Inu mukandimva ine ndikubwereza. Ndi kwa cholinga chimenecho.

¹¹⁰ Zindikirani. Tsopano onani momwe iwo anachita ku, khungu, inu mukuwona momwe iwo anali nalo. . . Yesu, kapena. . . Mulungu anachita kuwachititsa khungu Ayuda, kuwaletsa iwo kumuzindikira Yesu. Ngati iwo akanadziwa, ngati iwo akanadziwa kokha kuti izo. . . Powona chizindikiro chomwe Iye anachita, ngati iwo akanakhala pa siteji yawo yolondola, monga iwo analiri mmbuyo pansi pa lamulo pamene Mulungu anawalamulira iwo za mneneri, ndipo iwo anali atamuwona Yesu akuchita izo, iwo akanati, “Uyu ndi Mesiya.” Chifukwa chiyani zinali izo?

¹¹¹ Iwo mu m’badwo umenewo, omwe maina awo anali atalembedwa pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa, atumwi Ake ndi ena otero, iwo anachiwona icho ndipo anachizindikira icho.

¹¹² Bwanji sanatero ena onse a iwo? Mwawona, iwo anachititsidwa khungu. Iwo sakanakhoza kuchiwona icho. Iwo sakuchiwona icho, panobe. Ndipo iwo sachiwona icho mpaka iye atabadwa monga fuko, pa nthawi imodzi. Kuti. . .

¹¹³ Mawu sangakhoze kulephera. Kumbukirani, Mawu sangakhoze kulephera. Sindikusamala kaya inu muli nazo zogirigisha zingati, ndi zonse zomwe zikuchitika, komabe Mawu amenewo sangakhoze kulephera. Izo zikhala chimodzimidzi

mwanjira yomwe Mulungu anati izo zinali. Mukuwona? Tsopano, ife tikuzindikira kuti zinthu izi ziyenera kuchitika.

114 Ndipo ndicho chifukwa chake iwo sanamuzindikire Yesu pamene Iye anadzizindikiritsa Yekha mwanangwiro kuti ndi Mneneri.

115 Ngakhale wamng’ono—mkazi wamng’ono uja wa Chisamariya atayima pamenepo pa chitsime. Iye anali asanafikepo mu Samariya; Iye anangopita uko, anati Iye anali nako kusowa kuti adzere njira imeneyo, ndipo Iye anapita kumeneko. Ndipo kumeneko kunali mkazi wamng’ono uja. Ndipo iye, mu chikhalidwe chake, iye anali mu makonzedwe abwino kuti alandire Uthenga kuposa ansembe achipembedzo awo ndi zinthu za tsiku lija. Iye anachita izo. Zedi. Tsopano, mukuwona?

116 Koma, mu nkhope ya kukana kwawo konse, komabe mmodzi wa anthu olemkezeka awo anavomereza kuti iwo ankadziwa kuti Iye anali mphunzitsi wotumidwa kuchokera kwa Mulungu.

117 Ine ndinali kulankhula kwa mmodzi wa madokotala abwino amene alipo ku mayiko a kummwela, mu ofesi yake, osati kale litali. Katswiri wabwino kwambiri mu Louisville, mwamuna woyima weniweni. Ndipo ine ndinati kwa iye, ine ndinati, “Dokotala, ine ndikufuna ndikufunseni inu funso.”

Iye anati, “Chabwino.”

118 Ine ndinati, “Ine ndinazindikira chizindikiro chanu cha ung’ang’a, ndodo. Inu muli nayo njoka itazengezedwa pa mtengo. Chimenecho chikuyimira chiyani?”

Iye anati, “Ine sindikudziwa.”

119 Ndipo ine ndinati, “Icho chikuyimira ichi: icho chinali chiphiphiritso cha machiritso Auzimu, pamene Mose anakwezera mmwamba njoka ya mkuwa mu chipululu, mwawona, chomwe chinali kokha chiphiphiritso, chiphiphiritso chabe cha Khristu wona.”

120 Tsopano, lero, mankhwala ali chiphiphiritso cha machiritso Auzimu. Ndipo ngakhale ambiri a iwo samakhulupirira izo, dokotala wabwino weniweni amakhulupirira izo. Koma ena a iwo samakhulupirira izo. Koma choyimira chawo chomwe chimene iwo amagwirapo chimachitira umboni ku Mphamvu ya Mulungu Wamphamvuzonse, kaya iwo akufuna kukhulupirira izo kapena ayi. Mukuwona? Uko nkulondola. Apo pali njoka ya mkuwa itapachikika pa mtengo, pa choyimira zamankhwala.

121 Tsopano zindikirani Ayuda awa. Tsopano, mamba a khungu anali pa maso a anthu awa. Iwo, iwo sakanakhoza kuchitira mwina; icho chinali pamenepo, ndipo Mulungu anayika icho apo. Ndipo iwo ali pamenepo mpaka m’badwo umene iwo alonjezedwa, kubwera uku kwa aneneri. Inu mukhoza kutumiza amishonare, inu mukhoza kuchita chirichonse chomwe inu

mukufuna kuteru; Israeli sadzatembenuka konse mpaka aneneri awa atabwera powonekera, ndipo izo zidzakhala utachitika Mkwatulo wa Mpingo wa Amitundu.

¹²² Palibenso choposa kuti m'badwo wa ng'ombe ukanakhoza kulandira kuyitana kwa mkango, pakuti Mulungu wanena mu Mawu Ake kuti Mzimu wa ng'ombe unatuluka. Ndipo m'badwo wa okonzanso, munthu anatuluka. Mukuwona? Inu chabe. . .

¹²³ Ndicho chinthu chokhacho inu. . . iwo akhoza kulandira. Ndicho. . . Ndipo, mmenemo tsopano, iwo achititsidwa khungu. Ndizo basi zonse zomwe ziri kwa izo. Tsopano zindikirani.

¹²⁴ Koma m'badwo uli kubwera pamene Amitundu adzakhale atathana nawo. Pali mtengo, ndipo mizu inali Yachiyuda, ndipo iwo unadulidwapo; ndipo Amitundu anamezanitsidwa mmenemo, “wakuthengo, mtengo wa azitona,” ndipo iwo ukubereka chipatso chake. Tsopano, pamene Mkwatibwi wa Amitundu uyo wadulidwa, mtengo wa Mkwatibwi uja ine ndimawunena, ndipo watengedwera mmwamba mu Kukhalapo kwa Mulungu; Mulungu adzawafutapo Amitundu osakhulupirira awo, cha kuno ku mbali (anamwali ogona), ndi kumezetza kachiwiri. Iye analonjeza kudzachita izo.

¹²⁵ Ndipo mpaka nthawi imeneyo, inu mukungoyenera kudziwa kumene. . . Ngati inu mukudziwa kumene inu mukupita, chabwino, zabwino. Ngati inu simukudziwa, bwanji, inu mukupunthwa mu mdima.

¹²⁶ Tsopano, ndipo pamene Ayuda adzatembenuzidwe, mu m'badwo umenewo. Tsopano, monga m'badwo wa mpingo, pansu pa mphamvu ya lonjezo lodzozedwa, iwo adzalandira Khristu; koma, tsopano, osati pamene Amitundu ali mkati. Tsopano ife tikhoza kuwona mtundu wa uthenga womwe aneneri awiri awa, a Chivumbulutso mutu wa 11, ati adzalalikire. Tsopano inu momveka mukhoza kupenya chimodzimidzi chomwe iwo ati adzachte. Pakuti, otsalira, kapena zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi, okonzedweratu, akulandira Chisindikizo cha Mulungu.

¹²⁷ Tiyeni tingowerenga. Tsopano mverani mwacheru kwenikweni tsopano. Tsopano ine ndikufuna kuti inu muwerenge nane ine, ngati inu mungakhoze, chifukwa ine ndifanizira mmbuyo kwa izi mwa pang'ono ng'ono pokha. Mutu wa 7, tsopano, izi ziri pakati pa Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi ndi Chachisanu ndi chiwiri.

. . . *zitatha zinthu izi—zitatha zinthu izi* (Zisindikizo izi) . . .

¹²⁸ Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi chinamasulidwa, ndipo ndiyo nthawi ya Chisawutso. Aliyense akumvetsa zimenezo tsopano? [Osonkhana ati, “Ameni.”] Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi chinamasulidwa, ndipo Chisawutso chinayambika. Zitatha izi, chiyani?

...zitatha zinthu izi ine ndinawona angelo anayi akuyima pa ngodya zinai za dziko lapansi, akugwira mphepo zinayi za dziko lapansi, kuti iyo isawombe pa dziko lapansi, kapena pa nyanja, kapena pa mtengo uliwonse. (Angelo anayi!)

Ndipo ine ndinawona mngelo wina akutsika kuchokera kummawa, ali nacho chisindikizo cha Mulungu wamoyo: ndipo iye analira ndi liwu lalikulu kwa angelo anayiwo, kwa omwe kunapatsiswa kuwononga nyanja, dziko lapansi...nyanja,

Akunena, Musawononge dziko lapansi, ngakhale nyanja, kapena mitengo, mpaka ife titasindikiza antchito...

129 Osati Mkwatibwi. “Antchito.” Osati ana. “Antchito.” Israeli nthawizonse wakhala ali antchito a Mulungu. Mpingo uli ana, mwawona, mwa kubadwa. Israeli ali wantchito Wake. Yang’anani, malo aliwonse, ziri nthawizonse. Abrahamu anali wantchito Wake. Ife sitiri antchito. Ife tiri ana, ana amuna ndi aakazi. Eya.

...cha...cha Mulungu wathu mu mphumi zawo.

130 Tsopano yang’anani.

...Mulungu wathu mu mphumi zawo.

Ndipo ine ndinamva chiwerengero cha iwo omwe anasindikizidwa:...

131 Tsopano ine ndikufuna inu mumvere mwatcheru ku kuwerenga kwa iwo.

...ndipo apo anasindikizidwa zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi a mafuko onse a ana a Israeli.

132 Iye mwangwiwo akuwatchula iwo. Tsopano, ngati apo papezeka pali Muisraeli wozindikira za mu mtima wa Chibritishi atakhala apa, mverani momwe izi zikuchotsera mphepo kuchokera mwa izo, mwawona.

A fuko la Yuda anasindikizidwa zikwi khumi ndi ziwiri. (Analitchula, “fuko.”) A fuko la Rubeni anasindikizidwa zikwi khumi ndi ziwiri. A fuko la Gadi...zikwi khumi ndi ziwiri...

133 Yang’anani lanu—yang’anani mafuko anu tsopano.

Ndipo a fuko la Aseri anasindikizidwa zikwi khumi ndi ziwiri...fuko la Nefitali anasindikizidwa zikwi khumi ndi ziwiri...fuko la—la Manase...zikwi khumi ndi ziwiri.

Ndipo fuko la Simioni...anasindikizidwa zikwi khumi ndi ziwiri. A fuko la—la Levi anasindikizidwa zikwi khumi ndi ziwiri. A fuko la Esakara...zikwi

khumi ndi ziwiri. (Isakara, ine ndikuganiza inu mumatchula chotero.) . . . *zikwi khumi ndi ziwiri.*

. . . *fuko la Zebuloni . . . zikwi khumi ndi ziwiri.* Ndipo *fuko la Yosefe anasindikizidwa zikwi khumi ndi ziwiri.* A onse. . . *A fuko la Benjamini anasindikizidwa zikwi khumi ndi ziwiri.*

134 Tsopano, apo pali mafuko khumi ndi ziwiri, zikwi khumi ndi ziwiri kuchokera mu fuko. Khumi ndi ziwiri kuchulukitsa khumi ndi ziwiri. . . ndi chiyani? [Osonkhana ati, “Zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi.”—Mkonzi.] Zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi. Tsopano yang’anani. Iwo anali, onse, a mafuko a Israeli.

135 Tsopano yang’anani, “Zitatha izi. . .” Tsopano apa pakubwera gulu lina. Tsopano, Mkwatibwi wapita, ife tikudziwa izo. Koma liyang’anani gulu ili lomwe likubwera.

Zitatha izi ine ndinawona, ndipo, tawonani, unyinji wavukulu, womwe palibe munthu akanawuwerenga, wa mafuko onse, . . . mitundu, ndi anthu, ndi lirime, anayima pamaso pa mpandowachifumu, ndi pamaso pa Mwanawankhosa, atavekedwa mu miinjiro yoyera, ndi kanjeza mu dzanja lawo;

Ndipo analira ndi liwu lokweza, kunena, Chipulumutso kwa Mulungu wathu yemwe akhala pa mpandowachifumu, ndi kwa Mwanawankhosa.

Ndipo mafuko onse . . . anayima pozungulira kuzinga mpandowachifumu, ndi pozinga mkulu ndi zamoyo zinai, ndipo anagwa pamaso pa mpandowachifumu pa nkhope zawo, ndipo anapembedza Mulungu,

Kunena, Ameni: Madalitso, . . . ulemerero, . . . nzeru, . . . mathokozo, . . . ulemu, . . . chirimiko, . . . mphamvu, zikhale kwa Mulungu wathu kwa nthawi za nthawi. Ameni.

Ndipo mmodzi wa akulu. . .

136 Tsopano iye ali pamaso pa akulu apa. Monga, ife tamuwonera iye, monse kupyola mu Zisindikizo.

Ndipo mmodzi wa akulu anayankha, kunena kwa ine, Awa ndi ndani. . .

137 Tsopano, Yohane, pokhala Myuda, anawazindikira anthu ake omwe. Iye anawawona iwo mwa mawonekedwe a fuko. Nkulondola uko? Iye anawazindikira ndi kulitchula limodzi lililonse la mafuko.

138 Koma tsopano, pamene iye akuwawona awa, iye akukhala ngati akudabwitsidwa. Ndipo mkulu akudziwa izo, kotero iye akuti:

... Ndani awa omwe avekedwa mu miinjira yoyera?
ndipo akuchokera kuti iwo?

139 Yohane, akuyankha tsopano:

Ndipo ine ndinanena kwa iye, Bwana, inu mukudziwa.

140 Yohane sankawadziwa iwo, mwawona; mitundu yonse, malirime, ndi fuko.

... *Ndipo iye ananena kwa ine, Awa ali...*

... *iye ananena kwa ine, Awa ali iwo omwe akubwera kuchokera mu chisawutso chachikulu, (mwa kulankhula kwina, Chisawutso chachikulu), ndipo atsuka miinjira yawo... ayipanga iyo yoyera mu magazi a Mwanawankhosa.*

Chotero iwo ali pamaso pa mpandowachifumu wa Mulungu, ndi kumutumikira iye usana ndi usiku mu kachisi wake: ndipo iwo... iye yemwe anakhala pa mpandowachifumu adzakhala pakati pa iwo.

Iwo sadzamvanso njala, ngakhale kuti iwo adzamva ludzu nkomwe; ngakhale dzuwa kuwala pa iwo—kuwala kwa dzuwa pa iwo, kapena kutentha kulikonse.

Pakuti Mwanawankhosa yemwe ali pakati pa mpandowachifumu adzawadyetsa iwo, ndipo adzawatsogolera iwo ku akasupe amoyo a madzi: ndipo Mulungu adzapukuta... misonzi yonse pa maso awo.

141 Tsopano ife tikutsegula... kufika ku Chisindikizo.

Kodi inu munazindikira, iwo anali... Poyamba, ife tikuyamba tsopano, Israeli.

142 Ndiyeno ife tikuwona mpingo wotsukidwa, osati Mkwatibwi; mpingo wotsukidwa, mwa Chisawutso, mwawona, mwawona, ukubwera apa, chiwerengero chachikulu cha mitima yodzipereka kwenikweni yomwe inabwera kuchokera ku—ku Chisawutso chachikulu. Osati Mpingo; Iwo wapita, Mkwatibwi. Apo pali mpingo.

143 Tsopano ife tikupeza, uko patsogolo pang'ono, Yesu ananena kuti Mpandowachifumu unayikidwa, ndi womwe... iwo akanadzayima mu chiweruzo, aliyense.

144 Tsopano, ife tikupeza tsopano kuti anthu awa anasindikizidwa ndi Chisindikizo cha Mulungu wamoyo (nkulondola uko?), Ayuda awa. Chisindikizo cha Mulungu wamoyo nchiyani?

145 Tsopano, ine sindikumutcha aliyense, kupweteka ku kumverera kulikonse. Ine ndikungonena, mwawona. Kodi inu mukudziwa, kuti, kuwera za masikolala ambiri omwe analemba pa izi, amanena kuti gulu ili apa, lotsukidwa—mmagazi, ali kwenikweni Mkwatibwi?

146 Kodi inu mumadziwa kuti masikolala ambiri nawonso amanena kuti zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi ndi Mkwatibwi? Chiyani. . . Pali chinachake chimene chikuyenera kukwanira apa, cholakwika. . . apa molondola, chifukwa apo pali chinachake cholakwika tsopano.

147 Zindikirani, abale athu a Chiadventisti amanena, kuti, “Chisindikizo cha Mulungu, ndi kusunga tsiku la sabata.” Inu mukudziwa izo. Koma ine ndikufuna chidutswa chimodzi cha Lemba pa izo, kuti awonetse kuti sabata, kapena kusunga tsiku la sabata, ndi Chisindikizo cha Mulungu. Mukuwona? Ziri chabe winawake anajambula lingaliro limenelo.

148 Koma ngati inu muti muwerenge Aefeso 4:30, iyo imati, “Musakwiyitse Mzimu Woyera wa Mulungu, womwe inu mwasindikizidwa nawo mpaka tsiku inu. . . la chiwombolo chanu,” inde, bwana, pamene ntchito ya ukhalapakati yachitidwa, ndipo inu mwabwera; Khristu akubwera kudzawombola Ake Omwe. Inu mwasindikizidwa; osati mpaka chitsitsimutso chotsatira. Pamene inu mwasindikizidwa kamodzi nawo Mzimu Woyera, ndi ntchito yotsirizidwa, kuti Mulungu wakulandirani inu, ndipo palibe kuchoka kwa icho.

149 Inu mukuti, “Chabwino, ine ndinali nawo Iwo, ndipo ine ndinachokapo.” Ayi, inu—inu munalibe Iwo.

150 Mulungu anati Iwo umapitirira mpaka ku Tsiku la Chiwombolo. Tsopano, a-ha, inu mungotsutsana naye Iye, ndipo inu mukuwona chomwe chimatanthawuza. “Mpaka Tsiku la Chiwombolo Chanu.”

151 Zindikirani. Pamene apo anali. . . Pamene iwo anali otsalira malingana ndi kusankha, Ayuda awa ali tsopano otsalira malingana ndi kusankha. Mu masiku a utumiki woyamba wa Eliya kwa Ayuda, pamene okhulupirira zikwi zisanu ndi ziwiri anayikidwa pambali ndi dzanja la Mulungu, tsopano pali mwa otsalira awa nthawi, akubwera ku nthawi yawo, kukakhala zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi molingana nako kusankha. Kuti, Uthenga pa nthawi imeneyo, kuti akakhulupirire Uthenga, kukhala zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi.

152 Tsopano, inu mukuti, “O, tsopano miniti yokha, m’bale, ine sindikudziwa za chinthu cha “kusankha” ichi. Chabwino, ine sindinawerengepo izo apo.”

153 Chabwino, tsopano tiyeni tiwone ngati ziri zolondola, kapena ayi. Tiyeni titsegulenso ku Mateyu, ndipo tifike mmusi apa ndi kupeza ngati ife sitingakhoze kupeza kakang’ono kenakake pa izi penapake. Ine ndikukhulupirira tsopano kuti ine ndikulondola. Ine sindinalembe izo apa, koma changobwera chabe ku malingaliro anga. Tiyeni titenge, pa mapeto, ndime ya 30; pamene ife tinapita usiku watha, kutha kwa Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi, pa ndime ya 30. Tsopano tiyeni

tiwerenge izo ndi kuwona tsopano kumene ife tikufika, ndime ya 31. Mukuwona? “Iwo adzawona Mwana wa munthu akubwera mu ulemerero.” Tsopano ndime ya 31.

Ndipo iye adzatuma angelo ake ndi kuwomba kwakukulu kwa lipenga, ndipo iwo adzasonkhanitsa pamodzi osankhidwa ake kuchokera ku mphepo zinai, kuchokera ku mathero amodzi a kumwamba kupita kwa ena.

154 “Osankhidwa” adzatuluka. Ndi chiyani icho? Ndipo nthawi ya Chisawutso. Mulungu adzayitana osankhidwa Ake, ndipo amenewo ali Ayuda pa nthawi imeneyo, osankhidwa. Baibulo limalankhula za izo. Paulo akulankhula za izo, “Malingana ndi kusankha.” Padzakhala zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi malingana ndi kusankha, omwe ati adzakhulupirire Uthenga, kuchokera mwa kwenikweni mamilioni omwe ati adzakhale kumeneko.

155 Analipo mamilioni mu Palestina, pa masiku a uneneri wa Eliya, ndipo zikwi zisanu ndi ziwiri anapulumutsidwa kuchokera mwa mamilioni.

156 Tsopano, “malingana ndi kusankha.” Kumene, mamilioni a Ayuda akusonkhana ku dziko la kwawo. Ilo likukhala fuko. Kudzakhala mamilioni mmenemo, koma zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi “osankhidwa” okha adzatengedwa. Iwo adzamva Uthenga.

157 Chinthu chomwecho chiri mu Mpingo wa Amitundu. Pali Mkwatibwi, ndipo Iye ali wosankhidwa. “Ndipo iye adzayitanidwa malingana ndi kusankha.” Zindikirani, izi zonse zikuyimira Mpingo, mwangwiro, okhulupirira osankhidwa.

158 Ena sali kukhulupirira. Inu mukhoza basi kudziwa icho. Iwe ukamuwuzwa munthu Chowonadi, ndi kulola icho kuti chitsimikiziridwe mwa Mawu, ndiyeno nkuvomerezedwera; iye akuti, “Ine sindikukhulupirira Izo.” Iwe ukhoza chabe . . .

159 Musapusitsidwenso nazo izo konse. Yesu ananena kuti musatero. Anati, “Ziri monga kuponyera ngale basi patsogolo pa nkumba.” Mukuwona? Anati, “Ingowasiyani iwo okha. Iwo adzapotoloka nakuponderani inu pansu pa mapazi awo. Iwo adzakusekani inu. Ingochokanipo ndi kuwasiya iwo. “Ngati wakhungu akutsogolera wakhungu . . .”

160 Ine ndinapita kwa mwamuna, osati kale litali; iye anabwera kwa ine, kani. Iye anali akutsutsa, konsekonse, kulikonse, motsutsa machiritso Auzimu. Ndipo iye anabwera, ndipo iye anati, “Ine sindimakhulupirira machiritso Auzimu ako.”

161 Ine ndinati, “Anga, ine ndikuganiza, sangakhale abwino konse, chifukwa ine ndiribe aliwonse.” Ndipo iye . . . ine ndinati, “Koma a Mulungu ali angwiro.”

Iye anati, “Palibe chinthu choterocho.”

162 Ine ndinati, “Iwe wachedwa kwambiri kunena zimenezo, mzanga. Eya, iwe wachita—iwe wadikira motalika kwambiri nacho icho. Iwe ukadayenera kutsutsa, zaka pang’ono zapitazo, koma pabwera m’badwo wina tsopano. Alipo mamilioni kuti achitire umboni, mwawona.” Ine ndinati, “Iwe uli—iwe wachedwa kwambiri tsopano, mzanga, kuti unene zimenezo.”

163 Iye anati, iye anati, “Chabwino, ine sindikukhulupirira izo; ine sindikusamala zomwe iwe umachita.”

Ine ndinati, “Ndithudi ayi. Iwe sungakhoze.” Mukuwona?

164 Iye anati, “Ndikanthe ine ndi khungu!” Anati, “Ngati iwe uli nawo kwenikweni Mzimu Woyera, monga Paulo,” anati, “ndikanthe ine ndi khungu.”

165 Ine ndinati, “Ine ndingachite bwanji izo pamene iwe uli kale wakhungu?” Ine ndinati, “Atate ako akuchititsa iwe khungu kwa Chowonadi.” Ine ndinati, “Iwe, ndiwe kale wakhungu.”

166 Ndipo iye anati, “Ine sindingakhulupirire; ine sindikusamala chomwe iwe ungakhoze kuchita, umboni wochuluka motani umene iwe ungakhoze kutsimikizira, kapena chirichonse monga icho. Ine sindikukhulupirirabe izo.”

167 Ine ndinati, “Ndithudi. Izo sizinali za kwa osakhulupirira. Izo zinali kokha kwa okhulupirira. Ndi zimenezo.” Mukuwona?

168 Chinali chiyani icho? Mwawona, iwe umadziwa pomwepo, kuti kusankha kwakanika. Basi musati mupusitsidwe nazo izo, nkomwe. Yesu anachita chinthu chomwecho, Iye anati, “Asiyeni iwo okha. Ngati wakhungu atsogolera wakhungu, kodi onsewo sagwera mu dzenje?”

169 Koma pamene Iye anabwera kwa hule laling’ono, [M’bale Branham akhwatchitsa chala chake kamodzi—Mkonzi.] icho chinayatsa moto! Chinali chiyani icho? Iyo inali mbewu yosankhidwiratu itagona pamenepo, mwawona, yomwe yawona Icho pakali pano. Pamene Icho chinabwera kwa Petro, panali mbewu yosankhidwiratu ikugona pamenepo, mwawona, ndipo iwo anawona Icho. “Ndipo onse omwe Atate anandipatsa, anandi” (zochitika kale) “anandipatsa Ine, iwo adzabwera. Iwo adzabwera kwa Ine.” O, mai! Ine ndimakonda izo! Inde, bwana. Zindikirani, okhulupirira amakhulupirira Icho.

170 Osakhulupirira sangakhoze kukhulupirira Icho. Kotero, tsopano, ngati aliyense afuna kutsutsa za mbewu ya serpenti ndi zinthu, ndipo iwe nkuyesa kuwawonetsa iwo, iwo nkusamvera kwa Icho; ingochokapo. Ingowasiya iwo okha. Mwawona, Mulungu samatsutsana, ngakhalenso ana Ake.

171 Zindikirani, Ayuda zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi osankhidwa a Mulungu samagwadira kwa chirombo, zachipembedzo zake, kapena mafano, kapena chirichonse, ngakhale fuko lawo liri mu pangano ndi izo panthawiyo. Israeli

ali mu pangano, koma apa pali zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi omwe sakachichita icho. Ndiwo osankhidwa.

172 Chinthu chomwecho chiri pomwe apa mu Mpingo wa Amitundu tsopano, liri gulu losankhidwa. Inu simungawakokere iwo ku chinthu cha mtundu umenewo. Iwo sadzachikhulupirira icho. Ayi, bwana. Pamene Kuwala kunawakantha iwo kamodzi, izo zinakhazikitsa icho pomwepo. Iwo amawona . . . amawona icho chikuchitika, ndiye nkuchiwona icho chikuvomerezedwa ndi kutsimikiziridwa monga choncho. Ndipo iwo amayang'ana pansa apa mu Baibulo, kuwawona Mawu amene akumangopita. Chabwino, inu basi—inu basi mukhozanso kungosiya kumapusitsana nawo iwo, chifukwa iwo amakhulupirira Icho. Ndizo zonse. Ndizo zonse. Ngakhale iwo sangakhoze kuchifotokoza Icho, koma iwo amadziwa kuti iwo ali nacho Icho. Kotero, monga ine ndikuti, pali zinthu zambiri zomwe ine sindingakhoze kuzifotokoza, koma ine—ine ndikudziwa ziri zenizeni mulimonse. A-ha. Chabwino.

173 Nthawi iyi inali pakati pa Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi ndi Chachisanu ndi chiwiri, yomwe Iye akuyitana anthu awa, omwe analankhulidwa ndi Yesu mu Mateyu mutu wa 24 ndipo ndime ya 31, yomwe ife tawerenga kumene, mwawona. Malipenga apa, mboni ziwiri za . . . Pamene lipenga liwomba, ndilo lipenga la mboni ziwiri za m'badwo wa chisomo kwa Ayuda. Kuwomba kwa lipenga limodzi, inu mukuzindikira, kuwomba kwa lipenga limodzi. Iye anati, “Ndi kuwomba lipenga.” Tsopano zindikirani cha apa, ya 31.

Ndipo iye adzatumiza angelo ake (osati mmodzi, mwawona; apo pali awiri a iwo) ndi kuwomba kwakukulu kwa lipenga, . . .

174 Nchiyani icho? Pamene Mulungu akukonzekera kuti alankhule, pali kuwomba kwa lipenga. Ndilo nthawizonse Liwu Lake. Ndilo kuyitanira ku nkondo, mwawona. Mulungu amalankhula. Angelo awa adzatulukira ndi kuwomba kwa lipenga.

175 Ndipo inu zindikirani, pa Uthenga wa mngelo wotsiriza, lipenga likuwomba. Uthenga wa mngelo woyamba, lipenga likuwomba; wa mngelo wachiwiri, lipenga linawomba, pamene Iye anawutumiza iwo. Zindikirani, koma pamene Zisindikizo zinalengezedwa, izo zinali zonse mu chinthu chimodzi, Chauzimu, kukayitanira gulu la anthu; apo panali lipenga limodzi linawomba, ndipo Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri zinamatulidwa.

176 Zindikirani, “Kusonkhanitsa Ayuda osankhidwa Ake kuchokera ku ngodya zinai za miyamba.”

177 Iye anatchula Zisindikizo zisanu ndi chimodzi, monga ife tawonera, koma osati Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri. Iye

sananene konse kanthu umu za Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri, paliponse.

178 Mwawona, pomwepo, ndime ya 32, akutembenukira ku mafanizo, a nthawi ya kuyitana kwa Ayuda osankhidwa. Tsopano yang'anani apa, mwawona.

179 “Ndipo Iye adzatumanga angelo ndi lipenga, ndi kukasonkhanitsa osankhidwa kuchokera ku ngodya zinayi za kumwamba.” Tsopano Iye akuyamba. . .

180 Mwawona, Iye sakunena kanthu za Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri apa. Mukuwona? Iye analankhula za Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi; Choyamba, Chachiwiri, Chachitatu, Chachinayi, Chachisanu, ndi Chachisanu ndi chimodzi.

181 Koma zindikirani:

Tsopano phunzirani fanizo la mtengo wa mkuyu; Pamene nthambi zake ziri zanthetebe, ndipo zikuphuka masamba, inu mumadziwa kuti dzinja liri pafupi:

Kotero chomwechonso inu, pamene inu mudzawona zinthu zonse izi, mudzadziwa kuti iyo ili pafupi, ngakhale pakhomo.

182 Lotsiriza lija, funso lija lomwe iwo anamufunsa Iye, “Ndipo chidzakhala chiyani chizindikiro cha kutha kwa dziko?”

183 “Pamene inu muwona Ayuda awa. . . Pamene inu muwona zinthu zina izi zikuchitika, inu mukudziwa chomwe chikuchitika. Tsopano, pamene inu mudzawawona Ayuda. . .” Akulankhula kwa Ayuda! Tsopano yang'anani. Ndi gulu lotani lomwe Iye akulankhula nalo, Amitundu? Ayuda! Ayuda! Mukuwona?

184 Tsopano Iye anati, “Inu mudzadanidwa ndi mafuko onse chifukwa cha Dzina Langa,” ndi zina zotero, monga.

185 Tsopano, “Pamene,” Iye anati, “mukawona Ayuda awa akuyamba kuphukira masamba awo cha kutsidyako,” pamene Israeli uyo akuyamba kubwereranso, kufika ku dziko lawo. Pamene iye adzafika kumeneko, (Mpingo uli wokonzeka kuti Ukwatulidwe), pali zaka zitatu ndi theka zatsalira kumka mu kutha kwa dziko lakale, ndipo ilo likutuluka mu chisokonezo, ndipo mkati mukubwera Zakachikwi, kwa latsopano—dziko lapansi latsopano. Anati, “Ngakhale pakhomo!” Tsopano, zaka chikwi chimodzi pa dziko lapansi ziri kokha tsiku limodzi kwa Mulungu. Ndipo zaka zitatu ndi theka, zingafike kuti izo? Mphindi zingapo zokha, mu nthawi ya Mulungu. Ndicho chifukwa chake Iye anati, “Iyo ili pakhomo.”

Indetu Ine ndinena kwa inu, kuti, M'badwo uno sudzatsirizika, kuthedwa, anthu awa, mpaka zinthu zonse izi ziri. . .

186 Chiyani, nchiyani chomwe sichidzathedwa? Iwo ayesera kuti amuphe Myuda, kuwachotsa pa dziko lapansi, nthawi zonse. Iwo sadzakhoza konse kuchita izo.

187 Koma zindikirani. M’badwo umene wa Ayuda womwe unawona kubwerera, mmbuyo ku Palestina, m’badwo umenewo udzawona zinthu izi zikuchitika. Ndipo chabe zaka ziwiri zotsiriza, iye anali mwathunthu atakhala fuko, ndi ndalama yake ndi chirichonse. Apo iye ali.

188 Tsopano ife tiri kuti, amzanga? Zisindikizo ndi chirichonse zikutseguka; tsopano ife tikuzitenga izi pakati apa. Apo izo ziri. Mukuwona pamene ife tiri? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.]

189 Ine ndikuyembekeza kuti inu mukumvetsa Izo. Ine ndiribe maphunziro. Ine ndikudziwa chomwe ine ndikulankhula, koma mwinamwake ine sindingakhoze kufotokoza—kufotokoza Izo, kuti zimveke kwa inu. Koma ine ndikuyembekeza kuti Mulungu atenga Mawu amene asakanizidwa, ndi kuwagawa iwo molondola, mwawona, ndi kukulolani inu kudziwa chomwe Icho chiri. Chifukwa, ili, ife tiri pakhomo. Ife tiri apa pa nthawi. Tsopano zindikirani.

190 Mwawona, pomwepa tsopano, Iye akutembenukira kwa Ayuda awa, ndipo pa—nthawi yotsiriza. Iye akunena zomwe ziti zidzachitike. Ife tikudziwa ngakhale izo tsopano... Ife tikudziwa, tikuzindikira bwino, kuti mafuko ali omwazikana. Iwo akhala ali, kwa zaka mazana makumi awiri ndi asanu. Iwo analoseredwa kuti adzamwazikana ku mphepo zinai. Kodi inu mumadziwa zimenezo? Ife tikudziwa zimenezo.

191 Chifukwa, ife sitichita kubwerera mmbuyo ndi kukatenga, kukatenga izo, chifukwa ine ndiri nacho chinachake apa chofunikira kwenikweni chomwe ine ndikufuna inu kuti muchiwone, musanafike inu potopa kwambiri, ndipo ine kufika pfooka.

192 Zindikirani. Ife tikudziwa, ngakhale fuko lirilonse, uwo ndi mndandanda wa fuko, kapena chirichonse chomwe inu mukufuna kuchitchula icho, kapena kafukufuku, kapena malo a fuko, sali konse pamodzi. Iwo amwazikana, kulikonse.

193 Ayuda, akusonkhana ku Yerusalemu, sali . . . Iwo sakudziwa ngakhale mafuko awo. Iwo alibe konse mbendera za mafuko kapena chirichonse. Chonse chomwe iwo akudziwa, ndiye, kuti iwo ali Ayuda. Iwo analoseredwa kuti adzakhala mwanjira imeneyo, mu dziko lonse. Tsopano, mabuku awo awonongedwa. Iwo sakudziwa.

Inu mukati, “Ndiwe wa fuko liti?”

“Ine sindikudziwa.”

“Fuko liti?”

“Ine sindikudziwa.”

194 Mmodzi wochokera kwa Benjamini, mmodzi wochokera ku *ili*, ndipo mmodzi wochokera kwa *ilo*. Iwo sakudziwa kumene iwo akuchokera. Mabuku awo awonongedwa, kupyolera mu nkondo, ndipo kwa zaka mazana makumi awiri ndi asanu. Chinthu chokha chimene iwo akuchidziwa, iwo ali Ayuda. Ndicho chonse. Koteru, iwo akudziwa kuti iwo abwerera ku dziko la kwawo. Iwo komabe... Zindikirani, ngakhale iwo sakudziwa mafuko awo, koma Mulungu akudziwa.

195 Ine ndikungokonda izo! Inu mukudziwa, Iye ngakhale anati pali... “Tsitsi lililonse pa mutu wanu ndi lowerengedwa.” Hum! Zindikirani, Iye samataya kanthu. “Ine ndidzaliwukitsa ilo kachiwiri pa tsiku lotsiriza.”

196 Ngakhale iwo ataya zawo—zawo—mbendera zawo za fuko, ndi *yemwe* mmodzi uti ali, ndipo kaya iwo ali *ichi* kapena *icho*; iwo sakudziwa kaya iwo ali ochokera kwa Benjamini, kapena kaya iwo ali ochokera kwa Rubeni, kapena—kapena Isakara, kapena kumene iwo akuchokera. Koma, chonchobe, Mulungu akuwayitanira iwo apa.

197 Tsopano zindikirani, mu Chivumbulutso 7, ife tikuwerenga izi. “Zikwi khumi ndi ziwiri” za fuko lililonse, la osankhidwa, kuchokera mwa onse a iwo. Pali zikwi khumi ndi ziwiri kuchokera mu fuko lililonse, ndiwo osankhidwa, ndipo ayikidwa pomwe apa mwa dongosolo. O, mai! Ali chiyani iwo? Iwo ali mu dongosolo lafuko. Komabe, iwo sali tsopano, koma iwo adzakhala. Iwo ali mu dongosolo lafuko. Nchiyani chiti chidzakhale mu dongosolo lafuko? Osati Myuda wamba, ayi. Koma iwo omwe asankhidwa, zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi, adzayikidwa mu dongosolo la fuko. O, mai!

198 Momwe ine ndikanakondera kukuwonetsani inu! Ife sitipita mu izo. Koma ndizo chimodzimodzi zomwe Mpingo unayenera kukhala, a-ha, mu dongosolo kumene.

199 Tsopano ine ndikufuna inu muyang’ane mwatcheru kwenikweni ndi kuwerenga nane ine, kwa miniti. Tsopano apa pali chinachake chomwe mwinamwake inu simunachizindikire konse mu k—kuyitana kwafuko. Ine ndinakuwuzani inu, kanthawi kapitako, kuti muwerenge Chivumbulutso 7. Werengani nane ine, ndipo yang’anani mafuko amenewo. Mu Chivumbulutso 7, Dani ndi Efraimu akusowa ndipo sakuwerengedwa nawo iwo. Kodi inu munazindikira izo? Yosefe ndi Levi analowezedwa mu malo awo. Kodi inu munazindikira izo? Dani ndi Efraimu sali pamenepo. Ayi, bwana. Koma, Yosefe ndi Levi analowezedwa mu malo a—a—a Dani ndi Efraimu.

200 Chifukwa? Iwo... Mulungu wokumbukira nthawizonse amakumbukira lonjezo lililonse la Mawu Ake. O, ndikufuna nditalalikira pa izo. Mukuwona? Mulungu sayiwala kanthu, ngakhale izo zimawoneka ngati.

²⁰¹ Monga Iye anamuwuzwa Mose. Israeli anali ali kumusi uko, “zaka mazana anayi.” Iwo ankayenera kupita uko nthawi imeneyo. Iye anamuwuzwa Abrahamu, “Ndipo mbewu yake idzakhala ikuyenda mu dziko lachirendo kwa zaka mazana anayi, ndiye Iye adzawatulutsa iwo ndi dzanja lamphamvu.” Koma ndiye Iye anati kwa Mose, “Ine ndakumbukira lonjezo Langa, ndipo Ine ndabwera pansu kuti ndipange bwino chomwe Ine ndanena.”

²⁰² Mulungu samayiwala. Iye samayiwala matemberero Ake, ngakhale Iye samayiwala madalitso Ake. Koma, lonjezo lililonse lomwe Iye analipanga, Iye amakhala nalo ilo.

²⁰³ Apa pali chifukwa chomwe iwo anali kusowera, tsopano, ngati inu mungayang’ane. Tsopano werengani. Ine ndikufuna inu muwerenge ndi ine tsopano. Pitani ku Deuteronomo, twente- . . . ndime ya 29 pamenepo, kapena mutu wa 29, kani. Apo pali chifukwa chomwe mafuko awa sakukhalira pamenepo. Chirichonse chiri nacho chifukwa kwa icho. Deuteronomo, ife tikufuna kutenga m—mutu wa 29 wa Deuteronomo. Tsopano, Ambuye chotero atithandize ife, kuti ife tingakhoze kumvetsa tsopano. Tsopano ife tikufuna kuyambira mu Deuteronomo, mutu wa 29, pa ndime ya 16. Tsopano mverani. Mose akulankhula.

(Pakuti inu mukudziwa momwe ife takhalira mu dziko la Igupto; ndi momwe ife tinabwera kupyola mu mafuko amene ife tinawadutsa;

Ndipo inu mwawona zoyipa, ndi mafano awo, mtengo . . . mwala, siliva . . . golide, zomwe zinali pakati pa iwo:)

²⁰⁴ Aliyense ankanyamula kenakake kakang’ono, kapena china, chifano chaching’ono cha Sisiliya Woyera. Inu mukudziwa, chinachake chonga icho, mwawona. “Kuti chotero . . .” Mverani.

Kuti pasakhale pakati pa inu mwamuna, . . . mkazi, kapena banja, kapena fuko, yemwe mtima wake utembenukire kutali tsiku ili kuchoka kwa YHOVA Mulungu wathu, kupita ndi kukatumikira milungu ya mafuko awa; kuti pasakhale pakati pa inu muzu wakubala ndulu ndi mwavi;

Ndipo kuchitika kuti, pamene iye amva mawu a themberero ili, kuti iye—kuti iye adzidalitsa iyeyekha mu mtima wake, ndi kunena, ine . . . ndiri nawo mtendere, ngakhale ine ndiyenda mu kulingalira kwa mtima wanga womwe, . . .

²⁰⁵ Mwawona, anthu amanena, “O, iye amadzidalitsa yekha.” Inu mukudziwa, kupanga kamtanda kakang’ono kapena chinachake, monga iwo amachita tsopano, inu mukuwona; chinthu chomwecho, mwawona. Ndipo inu mukuwona ndiko kachitidwe kachikunja, mwawona, c—chikunja.

... iye amadzidalitsa yekha mu mtima wake, ...
kulingalira kwake komwe mu mtima wake momwe, *kuti*
awonjezera kuledzera kwa ludzu:

206 “Zimwani basi, izo sizimapanga kusiyana kulikonse; malingana ngati inu mukupita ku mpingo, inu muli bwino.”

Ndiye YEHOVA sadzamulekerera iye, koma ndiye *mkwiyo wa YEHOVA*... nsanje yake idzafuka motsutsa munthu ameneyo ndi matemberero onse omwe alembedwa mu bukhu ili (“Musati muchotse Mawu amodzi kwa Ilo, kapena kuwonjezera amodzi kwa Ilo,” mwawona.) *adzagona pa iye, ndipo YEHOVA adzafafaniza lake... kufafaniza dzina lake kuchokera pansi pa kumwamba.*

207 Ndipo pamene iye ali apa pa dziko lapansi, mwawona, “pansi pa kumwamba.”

Ndipo YEHOVA adzalekanitsa kwa iye *choyipa kuchokera ku mafuko onse a Israeli, malingana ndi temberero lonse la pangano lomwe lalembedwa mu bukhu ili la chilamulo:*

208 Chotero, “Ngati munthu aliyense adzatumikira fano, kapena kusunga fano pa iye, kapena kudzidalitsa yekha mwa kulingalira kwake komwe kwa mtima wake, ndi kutumikira mafano,” Mulungu anati, “mwamuna, mkazi, banja, kapena fuko, dzina lake lidzafafanizidwa kwathunthu, kuchotsedwa pakati pa anthu.” Tsopano, nkulondola uko? [Osonkhana, “Ameni.”—Mkonzi.] Kuwona kwake!

209 Kupembedza mafano kunachita chinthu chomwecho mu mpingo, zaka zapitazo, ndipo zikuchita lero. Ndipo ine ndikuzindikira... Yang’anani momwe wotsutsakhristu anayeserera kupanga kusuntha-kotsutsa. Ndi angati akudziwa kuti Mdierekezi amafanizira ndi kuyika dongosolo mokopera—mokopera oyera a Mulungu?

210 Nchiyani—tchimo nchiyani? Liri chinthu cholondola chopotozedwa. Bodza nchiyani? Liri chowonadi chonenedwa mokhota. Chigololo nchiyani? Chiri kachitidwe kolondola, kachitidwe kovomerezedwa, katachitidwa molakwika. Mukuwona?

211 Tsopano, mu kuyesera kuchita izi, “kulifuta dzina,” kodi inu munazindikira mu m’badwo wa mpingo, chirombo chomwecho chomwe chikupereka mafano a anthu akufa, ndi zina zotero, chinayesera kufuta Dzina la Ambuye Yesu Khristu, ndi kupereka mawudindo monga Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera. Chinthu chomwecho, ndi temberero ilo kuseri kwa icho, monga choncho.

212 Dani ndi Efraimu anachita kumene icho, pansi pa chinyengo cha mfumu mu Israeli, wonamizira, Yeroboamu. Tsopano, zindikirani, mu Mafumu Woyamba mutu wa 12. Ine ndikudziwa

ife tiri. . . Izi, kwa ine, izi—izi—izi zikuyika maziko pa chomwe ife tikhoza kudalirapo, chomwe ife tichiwona. Mafumu Woyamba, ine ndikufuna kupita ku mutu wa 12, ndime ya 25 mpaka ku ya 30.

Ndiye Yeroboamu. . . Sekemu mu phiri la Efraimu, ndipo anakhala uko; ndipo anapita mu. . . ndipo anakamanga Penueli.

Ndipo tsopano Yeroboamu ananena kwa. . . mu—mu mtima wake, (onani, kulingalira kwa mtima wake), Tsopano ufumu udzabwerera ku nyumba ya Davide:

²¹³ Iye ankayamba kuwopa, inu mukuwona, chifukwa anthu mwina angachokeko.

Ngati anthu awa akwera kuti. . . akapereke nsembe mu nyumba ya YEHOVA ku Yerusalemu, ndiye mtima wa anthu awa udzabwerera kachiwiri kwa ambuye, ngakhale kwa Rehoboamu mfumu ya Yuda, ndipo iwo adzandipha ine, ndi kupita. . . kwa Rehoboamu—Rehoboamu mfumu ya Yuda.

Potero mfumu inakhala upo, ndipo anapanga anaang’ombe awiri a golide, ndipo ananena kwa iwo, Kuli kokulemetsani inu kuti muzikwera ku Yerusalemu: onani milungu yamu, O Israeli, yomwe inakutulutsani inu. . . kuchokera ku dziko la Igupto.

Ndipo iye anayika mmodzi mu Beteli, ndipo winayo anamuyika iye mu Dani.

Ndipo chinthu ichi chinakhala tchimo: pakuti anthu anapita kukapembedza pamaso pa mmodzi, ngakhale ku Dani.

²¹⁴ Mwawona, Efraimu ku Beteli, ndipo Dani, ndipo iwo anayika mafano. Ndipo awa anapita kukapembedza izi.

²¹⁵ Ndipo apa ife tiri, mmusi momwe mpaka mu m’badwo wa Zakachikwi, pafupifupi, ndipo Mulungu akukumbukirabe tchimo limenelo. Iwo sakuwerengedwa ngakhale mmenemo. Heyi! Ulemerero! [M’bale Branham awombetsa manja ake pamodzi kamodzi—Mkonzi.] Motsimikiza basi monga Iye amakumbukirira lonjezo lirilonse labwino, Iye amakumbukira choyipa chimodzi chirichonse, nachonso. Tangokumbukirani, pamene. . .

²¹⁶ Ndicho chifukwa chake ine ndikukhulupirira, amzanga, ine ndayesera nthawizonse kukhala nawo Mawu amenewo, ziribe kanthu kaya Iwo awoneka achirendo chotani.

²¹⁷ Mwawona, tsopano, iwo sakanaganiza za icho pamenepo ndiye. Iwo sanaganize za icho pamenepo. Iwo anaganiza, “Chabwino, iwo adutsa nacho icho.” Chabwino.

218 Koma apa iwo ali cha apa mu m'badwo wa Zakachikwi uwo akukhalamo, pamene mayina awo ndi mafuko “zinafutidwa” kuchoka kwa iwo, chifukwa iwo anatumikira mafano, omwe Mulungu anawatemberera.

219 Kodi Iye sanati Iye “ankadana” nacho Chinikolai ndi Yezebeli uja? Khalani kutali ndi izo. Kodi Iye sanati Iye adzapha ana aakazi a Yezebeli ndi kupha kwa “imfa,” komwe kuli kulekana Mwamuyaya kuchoka mu Kukhalapo Kwake? Musati mudalire mwa izo, nkomwe. Chokani kwa izo. Kotero, Mulungu amakumbukira. Zindikirani.

220 Koma kodi inu munazindikira pamenepo, ilo linali loti “lifafanizidwe”? Chifukwa? Pansi pa Kumwamba panalibe Nsembe ya mwamsanga yomwe ikanakhoza kumupatsa iye Mzimu Woyera, kuti umulole iye apenye zinthu izi. Koma iye anachita icho, chonchobe, mwa malingaliro ake omwe awumbombo.

221 Koma, Ezekieli, mu masomphenya ake, mu Zakachikwi, iye akuwawona iwo kachiwiri mwa dongosolo langwiwo. Ezekieli, ngati inu mukufuna kuwerenga izo. Ingolembani izo, ndipo inu mukhoza kukawerenga izo, posunga nthawi. Ezekieli 48:1 mpaka 7, ndiponso kawerengeni 23 mpaka 29. Ezekieli anawona fuko lililonse chimodzimidzi basi mu dongosolo. Chabwino.

222 Ndipo, ndiponso, mu Chivumbulutso 14, Yohane anawawona iwo kachiwiri mwa dongosolo la fuko, uko nkulondola, fuko lililonse ku malo ake. Chinachitika nchiyani?

223 Inu mukukumbukira, Iye anati, “Pansi pa miyamba, pomwe dzina lake liti lidzafutidwe pa chochitika chafuko.” Malingana ngati iye anali pansi pa miyamba, apo sipakanakhalanso. Ndipo zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi awa adakali pansi apa mu gawo lafuko. Kulondola. Koma, inu mukuwona, iwo anali atachititsidwa khungu. Iwo anali nazo chabe nsembe za ng'ombe ndi mbuzi. Mukuwona? Tsopano zindikirani, Iye anawafuta iwo, “pansi pa kumwamba.”

224 Koma Wamitundu, mu masiku a Mzimu Woyera, kutsutsa Ichu; dzina lako linali kuchotsedwa kwathunthu ku Bukhu la Moyo, “ndipo sukanakhoza konse kukhala nacho chikhululukiro, mu dziko lino kapena dziko lakudza.” Nkulondola uko? Kotero apo ndi pamene ife tikuyima.

225 Israeli, pansi pa mbuzi, nkhusa, iwo—iwo anali nawo malo. Malingana ngati iwo anali pa dziko lapansi pano, mafuko awo anali kusowa. Iwo sakanakhoza konse kuphatikizidwa. Tsopano, onse. . . Pamene Iye anawayitana iwo, cha uko, zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi, iwo anali kusowa. Uko nkulondola. Iwo sakuwerengedwa ngakhale mmenemo. Ndipo Yosefe ndi Levi ayikidwa mu malo a Dani ndi Efraimu. Tsopano inu mukhoza kuyang'ana pa icho. Pomwe apo izo ziri, patsogolo panu, mwawona. Ndipo apa pali lonjezo la Mulungu,

kumboyo uko, zaka mazana ndi mazana izo zisanachitike. [M'bale Branham agogoda pa guwa kambiri—Mkonzi.]

226 Tsopano, chinachitika nchiyani? Iwo anatsukidwa mu nthawi ya Chisawutso chowopsya.

227 Tsopano, ngati Mulungu ati akatsuke uyo—namwali uyo, yemwe anali mkazi wabwino, koma iye anangolephera kupeza mafuta mu nyali yake, ndipo Iye akukamutsuka iye kupyolera mu kuzunzidwa mmenemo. Iye akuwayika mafuko awo mkati momwemo, kwa chinthu chomwecho, ndi kuwatsuka iwo mu nthawi ya Chisawutso. Chifukwa, icho chiri k—kutsuka. Chiri chiweruzo. Koma, inu mukuwona, iwo, kutatha. . . Ndipo, penyani apa, apa pakubwera zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi, kutatha kutsuka kwa Israeli. Ndipo apa pakubwera nayenso namwali wogona, akubwera, wotsukidwa, ndipo wavala miinjira yoyera. Mukuwona? Zangwiro bwanji! Nzokongola bwanji izo ziri!

228 Basi ngati Yakobo, mu nthawi ya vuto, mwawona. Iwo. . . Yakobo, mu nthawi ya vuto. Iye anali atachita cholakwika. Koma iye anapita kupyola mu nthawi yotsukidwa chifukwa iye anali atamulakwira m'bale wake, Esau. Mukuwona? Iye ananyenga, kuti atenge ufulu wobadwa nawo wake. Koma iye anapita kupyola mu kutsukidwa iye asanakhale nako kusintha kwa dzina lake kuchokera ku Yakobo kukhala Israeli, chomwe chiri choyimira cha dongosolo la Mulungu, kuyimiridwa lero.

229 Tsopano, ife titsegula tsopano ku ndime ya 8 ya. . . kapena ndime ya 1, ine ndikutanthawuza, ya mutu wa 8; wa Chivumbulutso 8:1.

230 Ine ndikudziwa inu mwatopa. Koma, tsopano, tangoyesani kumvera chabe kwa maminiti pang'ono tsopano. Ndipo, Mulungu wa Kumwamba atithandize ife, ndilo pemphero langa.

231 Ife tiyenera kukumbukira kuti Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri ichi ndicho kutha kwa nthawi, ya zinthu zonse. Uko nkulondola. Zinthu zomwe zalembedwa mu Bukhu Losindikizidwa—Kasanu ndi kawiri, losindikizidwa, la dongosolo la chiwombolo kuchokera ku maziko a dziko asanakhazikitsidwe, chikutsirizitsa chidutswa chirichonse. Icho chiri mapeto; icho chiri mapeto a dziko lopuluputa. Chiri mapeto a chirengedwe chopuluputa. Chiri mapeto a chirichonse. Mkati umo, ali mapeto a Malipenga. Ndi mapeto a Mbale. Ndi mapeto a dziko lapansi. Ndi. . . Ndi ngakhale kutha kwa nthawi.

232 Nthawi ikutha. Baibulo linanenachoncho. Mateyu, mutu wa 7. . . ine ndikutanthawuza, Chivumbulutso, wa 7 mut-. . . mutu wa 10 ndipo n. . . ndipo ndime 1 mpaka ya 7. Nthawi ikutha. Mngelo anati, "Sipadzakhalanso nthawi," pamene icho, mu masiku a chinthu chachikulu ichi kuti chichitike.

233 Chirichonse chikutha, mu nthawi iyi, mapeto a—a. . . pa mapeto a Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri ichi.

Zindikirani. Ndi mapeto a m'badwo wa mpingo. Ali m—mapeto a Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri. Ali mapeto a Malipenga. Ali mapeto a Mbale, ndipo ngakhale mapeto a kulowetsamo kwa Zakachikwi. Ndizo pa Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri.

²³⁴ Ziri monga ngati kuponyera makombola mu mlengalenga. Ndipo chombo chimenecho nkuphurikira *apa*, ndipo icho nkukwera ndiyeno nkukaphulika kachiwiri. Icho chikutulutsa nyenyezi zisanu. Imodzi ya nyenyezi zimenezo ikuphulika ndi kuphulitsa nyenyezi zisanu kuchokera kwa iyo; ndiyeno imodzi mwa nyenyezi zimenezo ikuphulika ndi kukankhira kunja nyenyezi zisanu kuchokera kwa iyo. Mwawona, izo zikungozimilirabe ndi kutha.

²³⁵ Ndicho, chomwe, Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri. Icho chikungotsirizitsa nthawi ya dziko. Icho chikutsirizitsa nthawi ya *ichi*. Icho chikutsirizitsa nthawi ya *icho*. Icho chikutsirizitsa nthawi ya *ichi*. Icho chikutsirizitsa nthawi. Chirichonse chinangotsirizira pa Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri icho.

²³⁶ Tsopano, Iye achita motani izo? Ndicho chimene ife sitikuchidziwa. Sichoncho? Ife sitikudziwa.

²³⁷ Ili ngakhale nthawi ya zinthu zonse izi, ndi kulowetsedwamo kwa Zakachikwi.

²³⁸ Zindikirani, kumatuka kwa Chisindikizo ichi kunali kwakukulu, mwakuti, Kumwamba kunachititsidwa bata ndi Icho, “mu kachetechete, kwa danga la theka la ora.” Tsopano, nchachikulu Icho! Ndi chiyani Icho? Inachititsidwa bata, Miyamba. Uko kunalibe kanthu komwe kanasuntha, kwa theka la ora.

²³⁹ Tsopano, theka la ora mwinamwake silingakhale lalitali ngati inu mukukhala ndi nthawi yabwino. Koma, mu kubanika kwa pakati pa imfa ndi Moyo, zimawoneka monga Zakachikwi. Icho chinali chachikulu chotero!

Yesu sanatchule konse Icho. Palibe aliyense wa iwo.

²⁴⁰ Yohane sakanakhoza ngakhale kulemba za Icho. Ayi, iye analetsedwa kuti alembe *apa*. [M'bale Branham asasa Baibulo lake kawiri—Mkonzi.] Mwawona, apo pali basi...basi...Iye sanalembe Icho, koma aka ndi kachetechete.

²⁴¹ Ndipo akulu makumi awiri ndi anayi omwe anayima pamaso pa Mulungu, Pamenepo, akuyimba ndi azeze awo; iwo anasiya kuwomba azeze awo.

Angelo anatontholetsa kuyimba kwawo, Kumwamba.

²⁴² Ganizani! Akerubi oyera ndi Aserafi, amene Yesaya anawawona Iwo mu kachisi, ali nawo maseti asanu ndi amodzi...kapena maseti atatu a mapiko. Atatu...Awiri pa nkhope yake, ndipo awiri pa mapazi ake, ndi kuwuluka. Ndipo usiku ndi usana, Iwo ali pamaso pa Mulungu,

akuyimba, “Woyera, woyera, woyera, ali Ambuye Mulungu Wamphamvuzonse!” Ndipo ngakhale pamene Iwo alowa mkati, kapena kulowa mu kachisi, ziwundo za kachisi zinkasuntha, ndi kwawo—kukhalapo kwawo.

²⁴³ Ndipo Aserafi oyera awa anatonthola. Angelo anasiya kuyimba. A-ha. Psyii! Akuwuluka mu Kukhalapo kwa Mulungu, akuyimba, “Woyera, woyera, woyera,” Iwo anatseka pakamwa. Panalibe Angelo akuyimba. Panalibe matamando. Kopanda—kopanda kutumikira pa guwa. Kopanda, kanthu. Uku kunali chete; kutonthola, kachetechete mwa imfa Kumwamba, kwa theka la ora.

²⁴⁴ Khamu lonse la Kumwamba linali chete kwa theka la ora ili, pamene chinsinsi cha Chisindikizo-Chachisanu ndi chiwiri ichi mu Bukhu la Chiwombolo chinamatulidwa motseguka. Ganizani za icho. Koma, Icho chamatulidwa. Mwanawankhosa akumatula Icho. Inu mukudziwa chiyani? Iwo anawopsyetsedwa ndi Icho, ine ndikukhulupirira. Iwo sankadziwa; apo Icho chinali! Iwo anangoyima.

²⁴⁵ Chifukwa? Ndi chiyani Icho? Tsopano, palibe aliyense wa ife akudziwa. Koma, ine ndiri—ine ndikuwuzani inu, mu langa—vumbulutso langa la Icho.

²⁴⁶ Ndipo, tsopano, ine sindiri woyandikira kuti ndikhale wotentheka. Ngati ine ndiri, ine ndiri wosadziwa za icho, mwawona. Ine ndiri. . . ine sindinapatsidwe zotero monga zikhumbo zoyipa zomangopitirira ndi zinthu zongolingalira.

²⁴⁷ Ine ndalankhula zinthu zina, mwina zinali ngati zachirendo kwa anthu ena. Koma pamene Mulungu abwera pozungulira, kuseri kwa Icho, ndi kuchitsimikizira Icho ndi kunena kuti Icho chiri Chowonadi, ndiye ndiwo Mawu a Mulungu. Mukuwona? Izo zikhoza kuwoneka zachirendo, mwanjira iyo. Mukuwona?

²⁴⁸ Ndipo tsopano, motsimikiza monga ine ndikuyimira mu nsanja usiku uno, ine ndinali nalo vumbulutso lomwe linawulula. Chiri mu chikhalidwe chofutukuka patatu. Izo ine ndilankhula kwa inu, mwa kuthandiza kwa Mulungu, za kufutukuka kwa Icho. Ndiyeno inu. . . Tiyeni tidutse pa izo, poyamba. Apa pali vumbulutso, kuti ndiyambe zomwe ine ndikufuna kukuwuzani inu, chomwe Icho chiri. Chimene chikuchitika, chiri chakuti. . . Mabingu Asanu ndi awiri awo omwe iye anawamva akugunda, ndipo analetsedwa kuti alembe; ndicho chimene chinsinsi chiri, chagona kuseri kwa Mabingu Asanu ndi awiri otsatana awo akulindimuka. [M’bale Branham agogoda pa guwa nthawi zingapo—Mkonzi.]

²⁴⁹ Tsopano, chifukwa? Tiyeni ife titsimikizire izo. Chifukwa? Izo ziri chinsinsi chimene palibe mmodzi akudziwa za icho. Yohane analetsedwa kulemba za Icho, ngakhale—ngakhale kulemba chophiphiritsa cha Icho. Chifukwa? Ichi ndi chifukwa chomwe uko kunalibe chochitika mu—chochitika Mmwamba:

icho chikhoza kupereka chinsinsi. Kodi mukuziwona izo tsopano? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.]

²⁵⁰ Ngati Icho chiri chachikulu, Icho chiyenera kuphatikizidwa, chifukwa Icho chiyenera kuchitika. Koma pamene Mabingu Asanu ndi awiri . . .

²⁵¹ Tsopano zindikirani. Pamene Angelo asanu ndi awiri anabwera kudzawomba Malipenga awo, apo panali bingu limodzi. [M’bale Branham agogoda pa guwa kamodzi—Mkonzi.] Pamene Israeli anasonkhanitsidwa, panali lipenga. “Pamene sipadzakhalanso nthawi,” lipenga lotsiriza, bingu limodzi.

²⁵² Koma apa pali Mabingu Asanu ndi awiri olunjika, kumene mu mzere: wanu, thuwu, firii, folo, faifi, sikisi, seveni, ndiyo nambala yangwiro. Mabingu Asanu ndi awiri mu mzere, analankhula, osati . . . kupanga basi—basi wani, thuwu, firii, folo, faifi, sikisi, seveni, molunjika. [M’bale Branham anagogoda pa guwa kasanu ndi kawiri—Mkonzi.] Ndiye, Miyamba siyikanakhoza kulemba Icho. Miyamba siyikanakhoza kudziwa za Icho, palibe chirichonse, chifukwa apo palibe kanthu kuti kazipitirira. Iyo inali nthawi ya kumasuka. Icho chinali chachikulu chotero, mpaka, Icho chinasungidwa chinsinsi kwa Angelo.

²⁵³ Tsopano, chifukwa? Ngati Satana akanachigwira Icho, iye mwina akanachita kuwononga kwakukulu. Apo pali chinthu chimodzi chomwe iye sakuchidziwa. Tsopano, iye akhoza kumasulira chirichonse chimene iye akufuna kutero, ndi kukopera mphatso ya mtundu uliwonse, (ine ndikuyembekeza inu mukuphunzira), koma iye sangakhoze kudziwa Ichi. Icho sichinalembedwe nkomwe mu Mawu. Icho chiri chinsinsi kwathunthu.

²⁵⁴ Angelo, chirichonse, kutseka pakamwa. Ngati iwo akanapanga kusuntha kumodzi, icho mwina chikanapereketsa chinachake, kotero iwo iwo anangotseka pakamwa, kusiya kuyimba azeze. Chirichonse chinayima.

²⁵⁵ Zisanu ndi ziwiri, nambala yangwiro ya Mulungu. Zisanu ndi ziwiri, [M’bale Branham agogoda pa guwa kasanu ndi kawiri—Mkonzi.] basi mpaka mmusi mwa mzere. Mabingu Asanu ndi awiri analankhula molunjika pamodzi, monga iwo anali kutchula chinachake. Zindikirani, pa nthawi imeneyo, Yohane anayamba kulemba Icho. Iye anati, “Usati ulembe Icho.”

²⁵⁶ Yesu sanalankhule konse za Icho. Yohane sakanakhoza kulemba Icho. Angelo sadziwa kanthu za Icho. Nchiyani Icho? Ndicho chinthu chimene, Yesu anati, “Ngakhale Angelo a Kumwamba sankadziwa” kanthu za Icho. Mukuwona? Mukuwona? Iye sanachidziwe Icho, Iyemwini. Anati, “Mulungu yekha” angachidziwe Icho.

²⁵⁷ Koma Iye anatiwuza ife, pamene ife “tidzayamba kuwona zizindikiro izi zikubwerapo.” Tsopano inu mukufika

kwinakwake? [Osonkhana, “Ameni.”—Mkonzi.] Chabwino. Zindikirani, ife “tikuyamba kuwona zizindikiro izi zikubwerapo.” Mukuwona?

Ngati Satana akanachigwira Icho. . .

258 Ngati inu mukufuna chinachake kuti chichitike. . . Tsopano inu mudzayenera kutenga mawu anga kwa izi. Ngati ine ndikukonzekera kuchita chinachake, ine ndikudziwa bwino kuposa kuwuzwa aliyense za icho. Osati kuti munthu ameneyo adzachinena icho, koma Satana adzachimva icho. Mukuwona? Iye sangakhoze kuchipeza icho, mu mtima wanga umo, malingana ngati Mulungu wachitsekera icho ndi Mzimu Woyera, kotero chiri pakati pa ine ndi Mulungu. Mukuwona? Iye sakudziwa kanthu za icho mpaka inu mutachilankhula icho, ndiye iye amachimva icho. Ndipo ine ndayesera. . . ine ndimawawuza anthu ine ndidzachita chinthu chakuti-chakuti, ndipo yang’anani Mdierekezi amadula gudumu lililonse limene iye angakhoze, kuti akafike kumeneko, mwawona, kuti andipambane ine kwa icho. Koma ngati ine ndipeza vumbulutso kuchokera kwa Mulungu, ndipo nkusangonena kanthu za ilo, ndiye icho nchosiyana.

259 Kumbukirani, Satana adzayesa kukopera. Iye adzayesa kukopera chirichonse chimene Mpingo uti udzachte. Iye wayesera kuchita izo. Ife tikuzindikira izo, kupyolera mu wotsutsakhristu.

260 Koma ichi chiri chinthu chimodzi chimene iye sangakhoze kukopera. Apo sipadzakhala kutsanzira kwa ichi, mwawona, chifukwa iye sakuchidziwa Icho. Palibe njira kuti iye adziwe Icho. Icho chiri Chikoka Chachitatu. Iye basi sakudziwa kanthu za Icho. Mukuwona? Iye sakuchimvetsa Icho.

261 Koma apo pali chinsinsi chikugona pansu pa Icho! [M’bale Branham agogoda pa guwa kamodzi—Mkonzi.] Ulemerero kwa Mulungu wa Mmwambamwamba! Ine sindingakhoze konse kuganiza mofanana, moyo wanga wonse, pamene ine ndinawona. Tsopano, ine sindikudziwa chomwe. . . ine ndikudziwa sitepe yotsatira pamenepo, koma ine sindikudziwa chomwe, momwe ndingamasulire icho. Sizikhala motalika. Ine ndalemba apa, pamene icho chinachitika, ngati inu mungakhoze kuwona apa, “Yima. Usapite patali kuposa izi pomwe apa.” Ine sindiri woyandikira kuti ndikhale wotentheka. Ine ndikungonena Chowonadi.

262 Koma inu mukukumbukira, nsapato yaying’ono, yomwe ine nthawizonse ndayesera kufotokoza momwe kuti moyo untagona pafupi ndi *chakuti-ndi-chakuti*, ndi chikumbumtima cha mkati, ndi zinthu za mtundu umenewo? Chomwe, chinangopanga gulu lalikulu la zokopera kuyambikira pa icho. Momwe iwo ayenera kulinyamula dzanja, ndi kuwagwira anthu, ndi kukhala ndi manjenje? Aliyense anali nako kunjenjemera mu manja awo?

263 Koma inu kumbukirani, pamene Iye ananditengera ine pamwamba apo, ndi kunena, “Ichi ndi Chikoka Chachitatu chija, ndipo palibe mmodzi adzachidziwe Icho.” Inu mukukumbukira izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Masomphenya samalephera konse. Iwo ali mwangwiro Chowonadi.

264 Tsopano zindikirani. Kumbukirani masomphenya a kuwundana? Charlie, ine. . . Apa inu muli.

265 Chinachake chikuchitika, ine ndinakuwuzani inu, sabata ino, kuti inu. . . Izo zakhala zonse pozungulira inu, koma ine ndikudabwa ngati inu munazindikira izo.

266 Kumbukirani kuwundana, kwa masomphenya a Angelo, pamene ine ndinachoka kuno kuti ndipite ku Arizona? [Osonkhana ati, “Ameni.”] Inu mukukumbukira “*Ndi Nthawi Yanji Ino, Mabwana?*” [“Ameni.”—Mkonzi.] Inu mukukumbukira izo? Zindikirani, apa panali kuphulika kumodzi kokha kwa bingu, ndipo Angelo asanu ndi awiri anawonekera. Nkulondola uko? [“Ameni.”] Kuphulika kumodzi kwa bingu, Angelo asanu ndi awiri anawonekera.

Ndipo ine ndinawona Mwanawankhosa pamene iye anali atatsegula chisindikizo choyamba, ndipo ine ndinamva, ngati ilo linali liwu la bingu, ndipo chimodzi cha zamoyo zinayi chinati, Bwera ndipo dzawone.

267 Zindikirani, bingu limodzi, Mauthenga Asanu ndi awiri omwe asindikizidwa ndipo sangakhoze kuwululidwa mpaka tsiku lotsiriza, la m’badwo uno. Mukuwona chimene ine ndikutanthawuza? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.]

268 Tsopano, kodi inu mwalizindikira gawo lachinsinsi la sabata yino? Ndicho chomwe Icho chiri. Ndicho chomwe Icho chakhala chiri. Icho chakhala chisali munthu wokhalapo, m—mwamuna. Icho chakhala chiri Angelo a Ambuye. Zindikirani.

269 Pali mboni, za atatu, akhala mkati muno, kuti sabata yapitayo, kupitirira pang’ono sabata yapitayo, ine ndinali pamwamba, kutali uko mu mapiri, pafupifupi ndi ku Mexico, ndi abale awiri omwe akhala apa. Ndikutola chisoso, kapena zomatirira, kuchokera pa mwendo wa thrauzo yanga; ndipo kuphulika kunachitika, komwe pafupifupi, kunawoneka ngati, kunagwedezera mapiri pansu. Tsopano, uko nkulondola. Ine sindinawawuze konse abale anga, koma iwo anazindikira kusiyana kwake.

270 Ndipo Iye ananena kwa ine, “Tsopano konzekera. Pita kummawa. Apa pali kumasulira kwa masomphenya aja.” Mukuwona? Tsopano, kuti ndikudziwitseni inu, M’bale Sothmann sanayipeze nyama yomwe iye anapitira. Ife tinali kuyesera kumupezera iyo iye. Ndipo Iye anati, “Tsopano, usiku uno, mwa chizindikiro kwa iwe, iye sachita izo. Iwe uyenera kudzipatulira wekha pa nthawi yino kukucheza kwa

Angelo awa.” Ndipo ine ndinamverera ngati ndasokonezeka, inu mukukumbukira.

271 Ndipo ine ndinali kumadzulo. Angelo anali kubwera kummawa. Ndipo pamene Iwo anali kubwera apo, ine ndinanyamulidwa nawo Iwo, (inu mukukumbukira izo?) akubwera kummawa. [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.]

272 Ndipo M’bale Fred, muno usiku uno, ali mboni, ndi M’bale Norman. Pamene ife timapita kumusi, ine pafupifupi ndinamukakamiza mwamuna ameneyo kuti atsale ndi kupeza nyama yake. Nkulondola uko, M’bale Sothmann? [M’bale Fred Sothmann, “Ameni.”—Mkonzi.] Eya, apo, akuyima pomwe apo. Ine ndinamukakamiza; koma, apobe, Iye anati, “Iye sachita izo.” Ine sindinalankhule konse kanthu; ndinapitirira.

273 Chinachake, nditakhala cha pambali ya chihema, tsiku limene. . . Inu mukukumbukira, M’bale Sothmann. Ndipo ine, mwamsanga pamene zinthu zina zinali kunenedwa, kuti ine ndinakupikani inu ndi M’bale Norman. . . M’bale Norman ali kuti? Kumbuyo uko. Ndinawayika iwo pansi pa lumбириro kuti iwo sadzanena zomwe zinali kuchitika. Nkulondola uko? [Abale ati, “Ameni. Izo nzowona.”—Mkonzi.] Kodi ine ndinatembenuka ndi kuchokapo ku chihema chija, monga *chonchi*? Nkulondola uko? [“Uko nkulondola.”]

274 Chifukwa, ichi nchimene chinali, chimodzimidzi chomwe chinali, ndipo kudziwa kuti ine sindikanakhoza kunena icho mpaka icho chitachitika, kuwona ngati anthu akanadzachimvetisa icho.

275 Ndipo kodi inu munazindikira? “Mngelo mmodzi uja,” ine ndinati, “mkati umo, munali Mngelo wachirendo.” Iye ankawoneka mochuluka kwa ine kuposa aliyense wa Iwo. Inu mukukumbukira izo? [Osonkhana, “Ameni.”] Iwo anali mu kuwundana; atatu pa mbali, ndipo mmodzi pamwamba. Ndipo mmodzi woyandikira kumene kwa ine apa, kuwerenga kuchokera kumazere kupita kumanja, akanakhala Mngelo wachisanu ndi chiwiri. Iye anali wowalirapo, ananthawuza mochuluka kwa ine kuposa onse a Iwo. Inu mukukumbukira? Ine ndinati, “Iye anali atatulutsa chidali chake, monga *chonchi*, ndipo anali kuwulukira chakummawa” (inu mukukumbukira) “monga *chonchi*.” Ine ndinati, “Iye anandinyamula ine mmwamba; kundikwezera ine mmwamba.” Inu mukukumbukira izo? [“Ameni.”]

276 Apa Icho chiri, yemwe ali nacho Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri, chinthu chimene ine ndachidabwa moyo wanga wonse. Amen! Zisindikizo zina izo zinanathawuza zochuluka kwa ine, zedi, koma, o, inu simukudziwa chomwe Ichi chatanthawuza, kwa nthawi imodzi mu moyo! [M’bale Branham anagodga pa guwa kambiri—Mkonzi.]

277 Ine ndinapemphera, ine ndinalirira kwa Mulungu. Ine—ine—ine . . . Utatha msonkhano uja wa ku Phoenix . . . Onse a anthu, kumeneko ndi ine, tikudziwa. Ine ndinagona mu mapiri.

278 Mmawa umodzi, ine ndinawuka ndipo ndinapita mmwamba mu Sabino Canyon, mapiri akulu, akale, aatali awo. Ndipo ine ndinapita pamwamba mmenemo. Ndipo uko kuli kanjira-kamapazi kakang'ono, iwe utatha kuyamba, kupita pamwamba ku Phiri la Lemmon, komwe kuli kuyenda kwa mailosi makumi atatu, pafupifupi chisanu cha mapazi makumi atatu pamwamba apo. Kotero, pamwamba mu phiri, mmawa kwenikweni kusanache, ndikupita pamwamba kupyola mu kanjira-kamapazi kakang'ono aka, ndikugudubuza miyala potsatira. Ine ndinamverera kutsogozedwa kuti nditembenukire ku njira *iyi*. Ndipo ine ndinapotoloka, ndi kupita mmwamba mu miyala yina yayikulu, yosongoka, o, mai, mazana a mapazi mmwamba.

279 Ndipo ine ndinagwada pansu pakati pa miyala imeneyo. Ine ndinagoneka pansu Baibulo *ili*, ndi kugoneka pansu bukhu ili . . . bukhu la zolemba laling'ono *ili*. [M'bale Branham awonetsa Baibulo lake ndi bukhu la zolemba—Mkonzi.] Ine ndinati, “Ambuye Mulungu, masomphenya awa akutanthawuza chiyani? Ine—ndiri—ndiri . . .” Ine ndinati, “Ambuye, iwo . . . Kodi iwo akutanthawuza kufa kwanga?”

280 Inu mukukumbukira, ine ndinakuwuzani inu, “Ine ndinkaganiza iwo akanatanthawuza imfa yanga, chifukwa chinachake chinaphulika mpaka chinangondigwedzera ine ku zidutswa.” Inu mukukumbukira izo. Ndi angati akudziwa izo, anamvapo izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Bwanji, zedi, mwawona, nonse a inu. Ndipo ine ndinakganiza iyo ikanakhoza kutanthawuza imfa yanga.

281 Ndiyeno mu chipinda, ine ndinati, “Anali . . . Anali—anali—anali chiyani iwo, Ambuye. Chiyani—akutanthawuza chiyani iwo? Kodi iwo akutanthawuza kuti ine ndikukafa? Ngati izo ziri, chabwino, ine sindiriwuzana banja langa. Ingondirolani ine ndizipita, mwawona, ngati ntchito yanga yatha.” Ndipo ine ndinati . . .

282 Tsopano, chinali chiyani icho? Koma Iye anatumizanso umboni, inu mukukumbukira ine ndikukuwuzani inu, kuti izo zinali iyo. Uko kunali kupitiriza kwa ntchito yanga. O, o, o! Inu mukumva izo! [Osonkhana, “Ameni.”—Mkonzi.] Mukuwona? Ndipo nditakhala pamwamba mu Sabino Canyon . . .

283 Atate Akumwamba akudziwa ichi. Mowona basi monga inu mukuwona izo zikufika pochitika, Angelo amenewo kubwera mpaka mmusi ndi kutsimikizira Uthenga uliwonse kuti uli momwemo. Ndiye, inu mukudziwa ngati Iwo ukuchokera kwa Mulungu, kapena ayi. Izo zinaloseredwa, inu, mwa

masomphenya. Ine sindikanakhoza kukuwuzani inu mpaka misonkhano itatha, chifukwa ine ndinaletsedwa kutero.

284 Mu Sabino Canyon, nditakhala pamwamba apo mmawa uja, ine ndinali nditakweza manja anga mmwamba. Ndipo changa... Mphepo inali itakupizira pansi chipewa changa chakuda chakale. Pamene... ine ndinali kuyimirira pamenepo, ndi manja anga mmwamba, ndikupemphera. Ine ndinati, “Ambuye Mulungu, ichi chikutanthawuza chiyani? Ine sindingakhoze kumvetsa izo, Ambuye. Kodi ine ndizichita chiyani? Ngati ili nthawi yanga yopitira Kwathu, ndiroleni ine ndipite pamwamba pano, ndi pamene iwo sadzandipeza konse ine. Ine sindikufuna aliyense kumadzabuna pozungulira, ngati ine ndikupita. Ine—ine ndikufuna basi banja kuti liganize kuti ine ndinangokayenda. Ndipo iwo sadzandipeza ine. Ndibiseni ine penapake. Ngati ine nditi ndipite, bwanji, ndiroleni ine ndipite. Mwina mwake Joseph adzalipeza Baibulo langa litagona apa, tsiku lina, ndipo muloleni iye adzaligwiritse Ilo ntchito. Mwawona, ngati ine ndikuchokapo, ndiroleni ine ndipite, Ambuye.” Ndipo ine ndinali ndi manja anga mmwamba. Ndipo, zonse mwadzidzidzi, chinachake chinagunda dzanja langa.

285 Ine sindikudziwa. Ine sindingakhoze kunena. Kodi ine ndinali nditagona? Ine sindikudziwa. Kodi ine ndinkayenda ndiri mtulo? Ine sindikudziwa. Kodi anali masomphenya? Ine sindingakhoze kukuwuzani inu. Chinthu chokha ine ndingakhoze kunena chiri chomwe ine... Chinthu chomwecho basi momwe Angelo awo analiri!

286 Ndipo icho chinakhuza dzanja langa. Ndipo ine ndinapenya, ndipo ilo linali lupanga. Ndipo ilo linali ndi chikumbu cha ngale, chokongola kwenikweni; ndipo chinali ndi chotetezera pa ilo, chiri ndi golide. Ndipo mpeniwo unkawoneka monga chinachake monga koromu monga siliva, kokha unali wowala kwenikweni. Ndipo iwo unali wa mbali zakuthwa mowopya, o, mai! Ndipo ine ndinaganiza, “Sichiri icho chinthu chokongoletsa!” Langokwanira dzanja langa! Ine ndinaganiza, “Ndicho chokongola kopitirira. Koma,” ine ndinati, “heyi, ine nthawizonse ndimawopa zinthu zimenezo, lupanga.” Ine ndinaganiza, “Ine ndichita nalo chiyani ilo?”

287 Ndipo basi pomwepo Liwu linagwedezera pansi kupyola pamenepo, lomwe linaswa miyala. Linati, “Ndilo Lupanga la Amfumu!” Ndiyeno ine ndinatuluka mwa izo.

288 “Lupanga la Amfumu.” Tsopano, ngati Ilo likanati, “Lupanga la mfumu...” Koma Ilo linati, “Lupanga la Amfumu.” Ndipo pali mmodzi yekha “Amfumu,” ndipo ndiye Mulungu. Ndipo Iye ali nalo Lupanga limodzi, ndilo Mawu Ake, womwe ine ndakhala nawo moyo. Ilo, kotero ndithandizeni ine, Mulungu; ndikuyimirira pa gome Lake Loyera apa, ndi Mawu awa oyera atagona apa! Ilo liri Mawu! Amen! O, ndi tsiku

lanji lomwe ife tikukhalamo! Ndi chinthu chachikulu bwanji! Mukuwona chinsinsi ndi chobisika? Chachitatu . . .

289 Nditayima pamenepo pamene ichi chinandichokera ine, Chinachake chinangobwera kwa ine ndipo chimati, “Usati uwope.” Tsopano, ine sindinamve liwu lililonse. Monga mkati mwa ine, munalankhula. Ine ndikungoyenera kukuwuzani inu chowonadi, chimodzimodzi basi chomwe chinachitika. Chinachake chinagunda, ndipo chinati, “Usati uwope. Ichi ndi Chikoka Chachitatu chiya.”

290 Chikoka Chachitatu! Inu mukuchikumbukira Icho? [Osonkhana, “Ameni.”—Mkonzi.] Iye anati, “Iwe wakhala nazo zokopera zambiri pa ichi, zomwe iwe umayesera kufotokoza. Koma,” anati, “usati ngakhale uyesere, Ichi.” Inu mukukumbukira izo? Ndi angati akukumbukira masomphenya aja? [“Ameni.”] Bwanji, ndiponseponse. Izo zinajambulidwa, ndipo kulikonse. Izo zakhala pafupi zaka zisanu ndi chimodzi zapitazo, zisanu ndi ziwiri zapitazo. Zakhala zaka zisanu ndi ziwiri zapitazo. Anati, “Usati uyesere kufotokoza Icho.” Anati, “Ichi ndi Chikoka Chachitatu, koma Ine ndidzakakomana nawe iwe mkati umo.” Nkulondola uko? [“Ameni.”] Iye anati, “Usati uyesere . . .”

291 Ine ndinali kuyima ndi n—nsapato ya mwana wamng’ono, pamene Iye anandiwuza ine. Anati, “Tsopano panga Chikoka Choyamba chako. Ndipo pamene iwe utero, nsomba idzathamangira nyambo.” Anati, “Ndiye uyang’anire Chikoka Chachiwiri chako,” anati, “chifukwa Icho chidzangokhala kansomba kakang’ono.” Iye anati, “Ndiye Chikoka Chachitatu chidzayigwira iyo.”

292 Ndipo azitumiki onse awo anandizungulira ine, anati, “M’bale Branham, ife tikudziwa inu mukhoza kuchita izo! Aleluya! M’bale Branham!” Ndipo pamene ine nthawizonse ndimazingirira, ndi gulu la azitumiki. Mukuwona? Ine ndimakonda anthu. Iwo amafuna kuti iwe ufotokoze chirichonse, *ichi, icho*.

293 Ndipo ine ndinati, “Chabwino, ha, ha, ha,” Ine ndinati, “Ine sindikudziwa.” Ine ndinati, “Ine ndamvetsa kupha kwa nsomba. Tsopano,” ine ndinati, “tsopano, chinthu choyamba iwe umachita . . . Apa ndi momwe zimachitidwa. Iwe umawona nsomba zonse pozungulira; iwe uyenera kugwedeza nyambo.” Chabwino, ndizo chimodzimodzi machenjerero owedzera nsomba. Kotero ine ndinati, “Gwedezani nyambo. Tsopano, inu mukuwona, pamene ine ndinagwedeza nyambo, nthawi yoyamba, tsopano nsomba imatsatira iyo.” Koma iwo anali aang’ono. Ndipo ndimo monga momwe iwo anali kuphera.

294 Kotero ndiye ine—ine ndinati, “Ndiye inu mudza—inun mudzayika . . .” Ndipo ine ndinayigwedeza nkuyitulutsa iyo, pa gombe. Ndipo ine ndinali ndi nsomba, koma iyo inkawoneka

ngati kakhungu pa nyambo, iyo inali chabe...iyo inali yaying'ono kwambiri.

²⁹⁵ Ndiyeno ine ndinali kuyimirira pamenepo, ndipo Chinachake chinati, "Ine ndinakuwuzwa iwe kuti usachite izo!"

²⁹⁶ Ine ndinayamba kulira. Chingwe chonse chinali chitamangana mondizungulira ine, monga *chonchi*. Ndipo ine ndinali...ndinali nditayima pamenepo, ndikulira, ndi mutu wanga pansu monga *choncho*. Ine ndinati, "Mulungu! O, ine... Ndikhululukireni ine! Ine—munthu wopusa. ndinali...ndinali kuyimirira apo, ndikulira, mutu wanga pansu monga *chonchi*. Ine ndinati, "Mulungu! O, ine... Mundikhululukire ine! Ine—ine ndine munthu wopusa. Ambuye, musati... Mundikhululukire ine." Ndipo ine—ine ndinali nacho chingwe ichi.

²⁹⁷ Ndipo icho, chimene ine ndinali nacho mu dzanja langa, inali nsapato ya mwana wamng'ono, pafupi yotalika *chonchi*. Ndipo ine ndinali nacho chingwe icho, chinali pafupi monga kunenepa kuzungulira chala changa, pafupi theka la incheshi, ngati. Ndipo kachibowo mu nsapato iyi kanali chabe pafupi usinkhu wa... locheperapo kuposa w—wani sikisitini, mwinamwake, ya incheshi, mu kachibowo. Ndipo ine ndinali kuyesera kuyimanga nsapato yaying'ono iyi, ndi chingwe cha incheshi yayikulu ichi. Ha!

²⁹⁸ Liwu linabwera, linati, "Iwe sungakhoze kuwaphunzitsa makanda Achipentekoste zinthu zauzimu." Anati, "Tsopano, asiye iwo okha!"

²⁹⁹ Ndipo basi ndiye Iye anandinyamulira ine mmwamba. Iye ananditengera ine mmwamba, ndi kundikhazika ine pamwamba kwambiri patali, kumene msonkhano unali kuchitika. Amawoneka ngati chihema kapena kachisi, wa mtundu wina. Ndipo ine ndinapenya, ndipo apo panali kabokosi kakang'ono, monga, malo aang'ono mkati mwake. Ndipo ine ndinawona Kuwala uko kunali kulankhula kwa winawake, pamwamba pa ine, Kuwala kuja kumene inu mumakuwona pa chithunzi apo. Iko kunazungulira kuchoka kwa ine, monga *chonchi*, ndipo kunapita pamwamba pa chihema icho. Ndipo anati, "Ine ndikakumana nawe iwe kumeneko." Ndipo anati, "Ichi chidzakhala Chikoka Chachitatu, ndipo iwe sumuwuza Ichi aliyense."

Ndipo mu Sabino Canyon, Iye anati, "Ichi ndi Chikoka Chachitatu."

³⁰⁰ Ndipo pali zinthu zitatu zazikulu zomwe zikupita nacho Icho. Ndipo chimodzi chafutukulidwa lero...kapena dzulo; chimodzi chinacho chafutukulidwa lero; ndipo pali chinthu chimodzi chimene ine sindingakhoze kumasulira, chifukwa icho chiri mu chilankhulo chosadziwika. Koma ine ndinayima pomwepo ndi kuyang'ana molunjika kumene pa Icho. Ndipo ichi chiri Chikoka Chachitatu chikubwera. [M'bale Branham

agogoda pa guwa katatu—Mkonzi.] Ndipo Mzimu Woyera wa Mulungu...O, mai! Ndicho chifukwa kumwamba konse kunali chete!

³⁰¹ Tsopano, ine—ine kulibwino ndiyimire pomwe apa, mwawona. Ine basi—ine basi ndikumverera kuyimikidwa, kuti ndisanene zochulukwa za Icho. Mukuwona?

³⁰² Kotero, ingokumbukirani, Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri, chifukwa chomwe Icho sichinatsegulidwe. [M'bale Branham agogoda pa guwa kasanu ndi kamodzi—Mkonzi.] Mwawona, chifukwa chimene Icho sichinawulule Icho, palibe mmodzi ayenera kudziwa za Icho.

³⁰³ Ndipo ine ndikufuna inu mudziwe, ine ndisanadziwe ngakhale Mawu aliwonse za Icho, masomphenya aja anabwera zaka zapitazo. Inu mukukumbukira izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ndipo apa Icho chiri, monga momwe ichi china chakhala, kugwera molunjika mu Mawu chimodzimodzi pamene Icho chinali. [M'bale Branham agogoda pa guwa kawiri.] Ndipo Mulungu akudziwa mtima wanga, ine sindinaganizapo nthawi imodzi za chinthu chotero monga Icho, ndipo apa Icho chinali. Iyo yatha kuposa momwe ife tikuganizira. A-ha. O, mai!

³⁰⁴ Izo zikusonyeza kuti Icho ndi chochokera kwa Mulungu, pakuti, onani, Icho chikukwanira mwangwiro mu malonjezo a Mulungu, kuchokera kumapeto a—a Uthenga, Inu zindikirani. Zindikirani tsopano, pakuti Uthenga-wa-nthawi-yotsiriza, Chisindikizo ichi. Kuwonjezera apo, Iye—Iye wawulula Zisindikizo zisanu ndi chimodzi zonse, koma Iye sakunena kanthu za Chachisanu ndi chiwiri. Ndipo Chisindikizo cha nthawi-yotsiriza, pamene Icho chiyamba, chidzakhala mwamtheradi chinsinsi kwathunthu, malingana ndi Baibulo, ife tisanachidziwe Icho. Ndipo kumbukirani, Chivumbulutso 10:1-7, 1 mpaka 7, mutu 10:1 mpaka 7, “Pa mapeto a Uthenga wa mngelo wachisanu ndi chiwiri zinsinsi zonse za Mulungu zidzaziwika.” Ife tiri pa nthawi yotsiriza, kutsegula kwa Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri.

³⁰⁵ Tsopano, ine ndinadziwa chotani? Tsiku lina, Lamlungu latha, sabata yapitayo, pamene ine ndinali kulalikira pa “Khalani odzichepetsa! Khalani odzichepetsa! Kumbukirani, Mulungu amachita mu zinthu zazing'ono.” Ine sindinazindikire chomwe kwenikweni chinali kulankhulidwa. Ndipo tsopano ine ndikuchiwona icho. Izo ziri mu njira yophweka chotero! Inu mukanaganiza kuti chinachake monga icho chikanadzawululidwa ku Vatikani kapena...Koma Icho chikubwera monga ngati Yohane M'batizi. Icho chikubwera monga kubadwa kwa Ambuye wathu, mu khola. Ulemerero kwa Mulungu! Kotero ndithandizeni ine, ora liri pafupi! Amenii! Ife tiri pano. O, mai!

306 Tsopano kodi inu mukuchiwona icho, Chowonadi cha masomphenya a Mulungu, Angelo asanu ndi awiri kundibweretsa ine kuchokera kumadzulo? Iwo anali kubwera kuchokera kumadzulo, kubwerera kummawa, kundibweretsera kuno chifukwa cha Uthenga uwu usiku uno. [M'bale Branham agogoda pa guwa kawiri—Mkonzi.] O, mai!

307 Tsopano, Liwu la bingu lalikulu lija, ndi kutuma kumene kunabweretsedwa apa, kwawululidwa, kuti Icho...ndipo chatsimikiziridwa kuti Icho chinali cha Mulungu. Tangoganizani tsopano. Ine sindinkazidziwa Zisindikizo izi, ndipo izo zawululidwa sabata yino. Kodi aliyense amaganiza za izo, za Angelo asanu ndi awiri awo kukhala Ichi, kukhala Uthenga umene unali kubwera. Angelo awo kundibweretsera ine kuno chifukwa cha Icho? Mukuwona?

308 Kumbukirani, Mtumiki wachisanu ndi chiwiri anali... Atumiki asanu ndi awiri anali... Mmodzi wodziwikayo kwa ine, Mngelo wachisanu ndi chiwiri, Iye amawoneka mochulukwa kwa ine kuposa aliyense. Tsopano, penyani, iwo anali kuyima munga *chonchi*. Tsopano, ife tikungofuna kuti inu muzindikire. Ndipo ine ndinali kuyimirira *apa*, ndipo ine ndinali kuwayang'ana enawo...

309 Mwawona, limodzi, gulu loyamba, la mbalame zazing'ono, nthenga zonse ziri yaya. Inu mukukumbukira izo? Ndipo izo zonse zinawulukira chakummawa. Ndipo gulu lachiwiri, zinali zowalirapo, mbalame zokulirapo zinkawoneka ngati nkhunda, zamapiko osongoka. Izo zinawulukira chakummawa. Chikoka Choyamba, Chikoka Chachiwiri, ndiye chotsatira anali Angelo. Ndipo munga...

310 Ine ndinali kuyimirira pomwepo, ndipo kuphulika uku kunasiya. Ndipo ine ndinali kuyang'ana njira *iyi*, moloza kumadzulo, ndipo Iwo anabwera ndipo basi anandinyamulira ine mmwamba, mkati Umo. Ine ndinapita kutali kwa kudziwa kwanga. Ndipo mmodzi wa Iwo, kubwera, anali Mmodzi yemwe ankawoneka wachirendo kwambiri kwa ine, anali Mmodzi kwanga...Kukhale kumamzere, pamene ine ndinalowera mukuwundanako. Koma kuwerenga kuchokera kumamzere kupita kumanja, iye akanadzakhala Mngelo wachisanu ndi chiwiri, mwawona, akubwera chodutsa. Tsopano, kumbukirani, Atumiki asanu ndi awiri.

311 Kodi inu mukukumbukira piramidi ya Mwala woyera, ya maloto a Junior Jackson omwe ine ndinamasulira kwa inu? [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.] Mukuwona? Zindikirani, usiku umene ine ndinachoka, ndipo ine... Apo panali maloto asanu ndi amodzi anabwera, ndipo limodzi lililonse la iwo molunjika ku chinthu chomwecho. Ndiye masomphenya anayamba, ndipo ananditumiza ine kumadzulo. Ndipo, Junior,

iyе anali kuyang'anira pamene . . . Zindikirani. Penyani ungiwiro wake!

³¹² Tsopano, ine ndiri—ine ndiri kuyembekezera ndi kudalira kuti anthu inu mukuzindikira kuti ine ndikuyesera kuyika chisomo ichi pa Yesu Khristu, Yemwe ali Mlembi wa Icho chonse. Ndipo chifukwa chokha chomwe inu simunandimve ine ndikulankhula monga chonchi kale, mu moyo wanu, koma ora ili likuyandikira. Mukuwona? Mukuwona? Zindikirani.

³¹³ Tsopano kuti ndipange izo motsimikizika, kwa inu, kotero izo zikhoza kukhomeredwa pansi. Ine ndikukonzekera kukusiyani inu kachiwiri. Ine sindikudziwa komwe nditi ndipite. Ine ndiyenera kulalikira Uthenga ku malo ena. Koma tsopano, kuti . . .

³¹⁴ Inu mukhoza kunena, “Ine ndamva izo zonse za mtundu wa kutentheka.” Ine sindikudziwa chiyani; ine sindingakhoze kuweruza munthu wina aliyense.

³¹⁵ Ine ndikuyenera kokha kukayankha kwa Mulungu pa zomwe ine . . . kwa—kwa inendekha. Koma panakhalapo konse nthawi imodzi yomwe ine ndinakuwuzanipo inu chirichonse mu Dzina la Ambuye, chomwe sichinali cholondola, mu zaka zonse izi? [Osonkhana ati, “Ayi.”—Mkonzi.] Palibe aliyense angakhoze kunena choncho, chifukwa ine nthawizonse ndimachinena icho basi momwe Iye ananenera icho.

³¹⁶ Tsopano ndiroleni ine ndingokuwonetsa inu kuti izi ziri chimodzimodzi zowona, ndi kutsimikizira izo.

³¹⁷ Tsopano kumbukirani, “Ngati pakhala wauzimu kapena mneneri, Ine Ambuye ndidzalankhula kwa iye mu masomphenya, ndi kuzindikiritsa kwa iye mwa maloto.” Kumasulira maloto, kumeneko. Yosefe, iye amakhoza kumasulira maloto, ndi kulankhula ndi—ndi kuwona masomphenya. Kodi izo nzowona? [osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.]

³¹⁸ Tsopano zindikirani ichi. Kutu, tsopano, pamene ichi chinachitika, Junior anali kuyimirira mu munda womwe unali nawo u—unali nawo piramidi yayikulu kwa iwo, monga choncho. Ndipo pamenepo panali chinachake chinalembedwa pa miyala, ndipo ine ndinali kuwululira Icho kwa anthu. Nkulondola uko, Junior? [M'bale Junior Jackson ati, “Ndiko kulondola.”—Mkonzi.] Pafupi chaka izo zisanachitike.

³¹⁹ Ndipo zindikirani chinthu chotsatira tsopano. Ine ndinatenga chinachake chokhala ngati chitsulo ndi kuwudula Iwo, ndipo mkatimo munali Mwala woyera umene unalibe kanthu kolembedwa pa Iwo. Ndipo, pa nthawi imeneyo, ine ndinayamba kupita kumadzulo. Ndipo ine ndinawawuza iwo onse, ine ndinati, “Musati mupite kumadzulo. Khalani pano ndipo ziyang'anani pa Ichi mpaka ine nditabwerera.” Ndinapita kumadzulo, kwa kuphulika; ndinabwereranso kummawa, ndi

Mzimu Woyera kumasulira Mawu osalembedwa awa. Tsopano, ngati izo siziri mwangwiro Mulungu Wamphamvuzonse, ine ndikufuna inu mudziwe chomwe icho chiri.

³²⁰ Ine ndikuyesereranji kunena izi, amzanga? Chiri kuti ndikuwonetseni inu kuti ife tiri pa nthawi yotsiriza. Tsopano, ngati iwo enawo ali mwangwiro pa dontho ndi Mawu, kotero chiri Ichi mwangwiro pa dontho ali Mawu! Ife tiri pano. Ife tiri pa mapeto, amzanga.

³²¹ Posachedwa idzakhala “nthawi itatha.” Mamilioni adzataya miyoyo yawo. Mamilioni adzakhala, omwe tsopano amakhulupirira kuti iwo apulumutsidwa, adzawerengedwa utuchi wa m’badwo wa atomiki. Ife tikukhala pa ora lotsiriza. Mwa chisomo cha Mulungu Wamphamvuzonse, mwa kuthandiza Kwake kwa anthu Ake, kuti iwo akakhoze kuyang’ana patsogolo ku kuwonekera kwaposachedwa kwa Khristu! “Motalika chotani, M’bale Branham?” Mwinamwake zaka makumi awiri; mwinamwake mu zaka makumi asanu; mwinamwake mu zaka zana. Ine sindikudziwa. Ndipo mwinamwake mmawa; mwinamwake usiku unobe. Ine sindikudziwa. Ndipo yense yemwe anena kuti iwo akudziwa, iwo akulakwitsa. Mukuwona? Iwo sakudziwa. Mulungu, yekha, akudziwa.

³²² Tsopano zindikirani. Kotero ndithandizeni ine, mwa Mulungu, ine ndikunena Chowonadi, kuti Izi ziri zodziwidwa mwauzimu kwa ine, zodziwidwa mwa Mzimu Woyera. Ndipo, mwa chimodzi chirichonse cha Izo, zazindikira malo Ake mu Baibulo.

³²³ Tsopano, chomwe chinsinsi chachikulu ichi chiri chimene chikugona pansu pa Chisindikizo ichi, ine sindikudziwa. Ine sindikudziwa icho. Ine sindikanakhoza kuchimvetsa icho. Ine sindikanakhoza kuchidziwa Icho, chabe chomwe Icho—chabe chomwe Icho chinanena, koma ine ndikudziwa kuti Icho chinali Mabingu Asanu ndi awiri awo akulankhula iwoeni moyandikirana kumene pamodzi, basi kumagunda nthawi zisanu ndi ziwiri zosiyana. Ndipo Iwo anafutukulidwa mu chinachake chimene ine ndinachiwona. Ndiye, pamene ine ndinachiwona Icho, ine ndinayang’anira kumasulira. Icho chinawuluka kudutsa pamenepo, ndipo ine sindinakhoze kuchizindikira Icho. Uko nkulondola chimodzimodzi. Mukuwona? Ora silinafikebe la Icho.

³²⁴ Koma, Icho chikusunthira mu mkombero umenewo, mwawona. Icho chikubwera pafupi. Kotero, chinthu choti inu muchite ndicho kukumbukira kuti ine ndikulankhula kwa inu mu Dzina la Ambuye. Khalani okonzekera, pakuti inu simukudziwa nthawi yomwe chinachake chingakhoze kuchitikira.

³²⁵ Tsopano, pamene izo zifika pa tepi, chomwe Icho chiri, izo mwina zidzatumiza zikwi khumi za abwenzi anga kutali ndi

ine. Chifukwa, iwo akanena, kuti, “M’bale Branham akuyesera kudziyika yekha, ndi kudzipanga yekha, w—wantchito kapena mneneri, kapena chinachake, pamaso pa Mulungu.” Ndiroleni ine ndikuwuzeni inu, abale anga, uko nkulakwitsa.

³²⁶ Ine ndikukuwuzani inu kokha zomwe ine ndawona ndi zomwe zawuzidwa kwa ine. Ndipo tsopano inu—inu muchite chirichonse chimene inu mukufuna kuchita. Ine sindikudziwa yemwe aka . . . chomwe chiti chikachitike. Ine sindikudziwa. Ine ndikungodziwa kuti Mabingu Asanu ndi awiri awo akugwirizira chinsinsi icho. Miyamba inali chete. Aliyense akumvetsa? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Iyo ikhoza kukhala nthawi, ikhoza kukhala ora tsopano, yomwe munthu wamkulu uyu yemwe ife tikumuyembekezera kuti awuke powonekera akhoza kuwuka powonekera.

³²⁷ Mwinamwake utumiki uwu, womwe ine ndayesera kuwatengera anthu kubwerera ku Mawu, wayika maziko; ndipo ngati iwo watero, ine ndidzakhala ndikukusiyani inu, kosabweranso. Sipadzakhala awiri a ife apa nthawi yomweyo. Mukuwona? Ngati izo ziri, iye adzakula; ine ndidzachepe. Ine sindikudziwa.

³²⁸ Koma ine ndakhala nawo mwayi, mwa Mulungu, kuti ndipenye ndi kuwona chomwe Icho chinali, mwawona, kupenya chikufutukulidwa mwa kuchuluka choncho. Tsopano, icho ndi Chowonadi.

³²⁹ Ndipo ine ndikutsimikiza kuti inu mwazindikira zinthu izi zomwe zakhala zikuchitika sabata yino. Ine ndikutsimikiza inu munazindikira mnyamata wamng’ono uja wa a Collins atagona apo, akufa, usiku wina; wamng’ono uja, msungwana wa leukemia.

³³⁰ Ufumu wa Mulungu ukubwera. Ndipo Icho chikubwera kwambiri kuchoka ku chithunzi kupita ku chenicheni, monga zakhala ziriri. Tsopano, izo sizikanamawatsamwitsa anthu. Kuchoka ku kulungamitsidwa, kupita ku kuyeretsedwa, mpaka ku ubatizo wa Mzimu Woyera, ndiyeno *apa, apa*. Mukuwona? Ife tikungoyandikira kwa Mulungu, nthawi zonse.

³³¹ Kodi inu simukukhoza kuwona, azitumiki a Chimethodisti, momwe uthenga wanu wa kuyeretsedwa unali pamwamba pa uwo umene Lutera analalikira?

³³² Inu a Chipentekoste, kodi simukuwona uthenga wanu wa ubatizo kuti uli kuposa iwo womwe Amethodisti ankalalikira? Inu mukudziwa chimene ine ndikutanthawuza?

³³³ O, ife tinali nazo zinthu zambiri zikupitirira! Ndipo uko nkulondola. Ndipo ngati alipo aliyense amene amatsutsa cholakwika, ndipo anthu kumanena chinachake chomwe chiri makamaka mabodza ndipo osati Chowonadi, ine ndimadana nazo izo.

334 Koma ine—ine ndimakonda Chowonadi cholimba, ziribe kanthu kaya mochuluka bwanji Icho chisokonezere njira *iyi* kapena njira *iyi*. Ngati Icho chiri Chowonadi, Mulungu potsiriza adzachiwonetsa Icho monga Chowona. Ndipo ngati Iye sachita izo, limodzi la masiku amenewa posachedwa, ndiye masomphenya anga sanali olondola. Tsopano inu mukuwona pamene ine ndinangodzigoneka ndekha.

335 “Chidzakhala liti icho, M’bale Branham?” Ine sindingakhoze kukuwuzani inu. Ine sindikudziwa.

336 Koma, limodzi la masiku awa, ngati ife sitikumana kachiwiri pa dziko lapansi lino, ife tikakumana kutsidya pa—pa mpando wa chiweruzo wa Khristu. Ndipo inu mudzapeza, kuti, mu chipinda chija, vumbulutso kubwera kuchokera kwa Mulungu, monga ngati zina zonsezo zachitira, kuti Izo... Chimodzi cha chinsinsi cha Chisindikizo icho, chifukwa chimene Icho sichinawululidwe, Icho chinali Mabingu Asanu ndi awiri omwe analankhula maliwu Awo. Ndipo apo Icho chiri, mwangwiwo. Chifukwa, palibe kanthu kakudziwa chirichonse za Icho. Icho sichinalembedwe konse. Kotero, ife tiri pa nthawi yotsiriza. Ife tiri apa. Ine ndikuthokoza Mulungu chifukwa cha Mawu Ake.

337 Ine ndikumuthokoza Iye chifukwa cha Yesu Khristu. Pakuti, popanda kumutumiza Iye kwa chi—chitetezero cha machimo athu, ife tonse tikanakhala mu thope lalikulu la tchimo, wopanda chiyembekezo. Koma, mwa chisomo Chake, Ake—Magazi Ake akutsuka tchimo lonse. Basi ngati dontho la inki mu chibekete cha Cloroxi, inu simungayipezenso inkiyo. Pamene machimo athu avomeredzedwa, iwo amayikidwa mu Magazi a Yesu Khristu; iwo sadzaziwika konse kachiwiri. Mulungu amawayiwala iwo; iwo sanachitidwe konse. Ndipo malingana ngati Nsembe imeneyo ikugona pamenepo mwa chitetezero kwa ife, ndiye ndizo zonse. Ndi zimenezzo, mwawona. Ife—ife sitiri ochimwa konse. Ife tiri Akhristu, mwa chisomo cha Mulungu. Kumbukirani, mwa ife eni ake ife tikhoza kukhala mwina-oyipa monga ife tinali kale. Koma, mwawona, chisomo cha Mulungu chawonekera kwa ife, ndipo ndicho chomwe chatipanga ife chimene ife tiri lero, abale ndi alongo Achikhristu.

338 Iyi yakhala sabata yopambana kwa ine. Ine ndatopa. Malingaliro anga atopa. Chifukwa ine—ine ndiri...ndi zopambana zomwe ine ndikanakhoza kuchita. Ndipo chinachake chachirendo chikuchitika, tsiku lirilonse. Ine ndimadabwitsidwa; kuyenda mu chipinda, ndi kukhala mmenemo kwa maminiti pang’ono, ndi kuwona Chinachake chikungonditembenuza ine mozungulira kwathunthu.

339 Ndipo, apa, ine ndimapita mkati umo ndi kukatenga zolemba. Ine ndimatenga mabuku a Dr. Smith, Uriah Smith, ndi, o, onse a—olemba ndi chirichonse, ndi kuwerengamo, kuwerenga mu mabuku awo. Ine ndikuti, “Tsopano *apa* pali Chisindikizo

Chachisanu ndi chimodzi. *Apa* pali Chisindikizo Chachinai. Tsopano munthu uyu akunena chiyani? Iye amakhoza kunena, ‘Chabwino, Icho chinali *ichi*, *icho*, kapena *chimzake*.’ Ine nkudzayang’ana cha *apa* ndi kutenga munthu wina. Iye anati Icho chinali *chakuti-ndi-chakuti*. Ndipo izo zimawoneka ngati ine basi. . . Izo basi sizimagwira ntchito molondola. Mukuwona?

³⁴⁰ Ndiye ine ndinaganiza, “Chabwino, ndi chiyani Icho, Ambuye?” Ndipo ine ndimayendayenda pansi kwa kanthawi. Ine ndimagwada pansi ndi kupemphera. Kubwerera ndi kukatenga Baibulo; kukhala pansi, kuwerenga. Kubwerera mmbuyo ndi patsogolo.

³⁴¹ Ndiye, zonse mwadzidzidzi, pamene ine ndimakhala chete, *apa* Icho chimangofutukulidwa monga choncho. Ndiye ine ndimagwira cholemba mwamsanga ndithu, ndi kupita kukalemba Icho pansi monga chonchi, chirichonse chimene ine ndinali kupenya ndi kuchita. Kuchiyang’ana Icho, monga choncho, mpaka ine nditachilemba Icho apo.

³⁴² Ndiye ine ndimatenga, tsiku lonse, ndi kupita kumusi ndi kukachifufuza Ichi, ndi kuwona ngati Icho chinamangiriza njira yonse mmusi kupyola mu Malemba. Ndiye, “Kutsimikizira zinthu zonse.” Mukuwona? Ine ndiri ndi Ichi *apa*.

³⁴³ Ndipo ine ndikuganiza, “Tsopano, alipo anthu ambiri anali nawo masomphenya. Alipo ambiri akhala mu mavumbulutso.” Ngati izi ziri zosiyana ndi Mawu, zisiyeni izo zokha; uko nkulondola, zisiyeni izo zokha.

³⁴⁴ Tsopano, tsopano, ndiye ine ndimachiyendetsa Ichi ngakhale mpaka mmusi monga *chonchi*, kuchiyendetsa icho mmusi monga *chonchi*. Ine ndimalemba pansi zinthu zazing’ono *apa*. Ine ndinaganiza, “Chabwino, tsopano, kalasi ikakondwa kumva izi, chifukwa izo zikumangirira *apa* ndi kumangirira *apa*. Tsopano, tiyeni tiwone, ichi chikunena chiyani *apa*? Inde. Ndipo, eya, *apa* icho chiri, pomwe *apa*.” Mukuwona?

³⁴⁵ Ndi kuchibweretsa Icho mmbuyo kupyola mu Baibulo, ndi kumangirira chinthucho mmusi, kupyola mu sabata. Apo Icho chiri, *pa* matepi. Inu muli olandiridwa kwa iwo. Ndipo ine ndinachita izo mwa kupambana kwa chidziwitso changa, pansi pa chiyanjano cha Chikristu, chisomo cha Mulungu, kwa anthu onse, mwa Yesu Khristu. Ine ndachita chopambana kumene chimene ine ndimachidziwa kachitidwe kake.

³⁴⁶ Inu mwakhala imodzi ya makalasi abwino. Palibe aliyense yemwe akanakhala mwa ubwino uliwonse woposa. Inu nonse mumabwera muno wani koloko mu tsiku, mpaka faifi koloko, mpaka pamene iwo amatsegula kachisi ndi kubweretsa k. . . kuwalola anthu kulowamo. Inu mwayimirira mu kuzizira; inu mwakhala mu chisanu; inu mwachita chirichonse; kuyima mozungulira makoma, mpaka miyendo yanu yonse kupweteka. Ine ndimawona amuna, atakhala pansi; kuwalola akazi kukhala.

Ndipo amodzi osiyana amayima monga choncho, mutakhala pozungulira. Ine ndinaganiza, “Ambuye, yonse. . .”

³⁴⁷ Iyi yakhala sabata yachinsinsi. Chinthu chonse chakhala chamtundu wachirendo, momwe, pamene anthu amabwera, kuwawona iwo atayimirira chozungulira panja, mu mazenera, mu zitseko, kumbuyo kuzungulira kumbuyo, paliponse, akumvera. Ndipo monga wolankhula, ine ndiri kutali kwa wolankhula. Ine—ine ndiri nalo luntha lochulukuka choncho, kudziwa kuti ine sindiri, kuti ine sindiri wolankhula. Koma anthu akanakhala pansu bwanji ndi kumamvera monga choncho? Iwo akanachita izo chifukwa chiyani? Iwo samabwera kudzamvera munthu wonga ine. Koma iwo akubwera chifukwa pali Chinachake mwa icho, chikuwakokera anthu kwa Ichu. Mukuwona? Apo pali Chinachake mwa icho, ndicho chikuwakokera iwo.

³⁴⁸ Monga mkazi wanga anayima apa pa nsanja ndi kuyimba, pamene ine ndinayamba:

Iwo amabwera kuchokera Kummawa ndi
Kumadzulo,
Iwo amabwera kuchokera ku dziko lakutali,
Kudzadya ndi Mfumu, kudzadya monga alendo
Ake”
Ali odala chotani amwendamnjira awa!
Kupenya nkhope Yake yowala
Kunyezimira ndi Kuwala Kwauzimu;
Odala ogawana nawo chisomo Chake,
Monga ngale mu korona Wake kuti awale.

³⁴⁹ Mutakumbukira inu zimenezo nthawizonse mu malingaliro anu, “Kuti mukhale ngale mu Korona wa Yesu Khristu.” Paulo ananena kwa Mpingo, “Inu muli—inu muli miyala yowala, ngale za Korona Wake.” Ife tikufuna kukhala ngale za Korona wa Yesu Khristu.

³⁵⁰ Ife sitikufuna, kuyika konse munthu mwa izo. Inu muyiwale chirichonse za ine. Ine ndine m’bale wanu, wochimwa wopulumutsidwa mwa chisomo, osati woyenera kukhala moyo. Ndicho chowonadi chimodzimidzi. Ine sindikunena izo kuti ndikhale wodzichepetsa; ndizo zoonu. Palibe kanthu mwa ine, wopanda kanthu kamodzi komveka, nkomwe.

³⁵¹ Koma chisomo cha Mulungu chalola maso anga osawuka, a mdima kuyang’ana kuseri kwa katani la nthawi ndi kuwona zinthu izo kutsidya, ndipo ine ndabwerera.

³⁵² Pamene ine ndinali mnyamata wamng’ono, ine ndinkawakonda anthu. Ine nthawizonse ndimakonda winawake kuti azindikonda ine ndi kumalankhula kwa ine. Palibe aliyense akanachita icho, chifukwa cha dzina la banja. Palibe aliyense akanalankhula kwa ine.

³⁵³ Koma pamene ine ndinapanga kugonjera kwanga kwa Mulungu, ndiye . . . Anthu athu, chiyambi, pokhala a Chiirishi, ine ndinaganiza, “Mwinamwake . . . Iwo anali onse Achikatolika, ndipo mwinamwake icho chikanakhala Chimenecho.” Ine ndinapita *kumeneko*, ndipo Iye anali njira yina. Ndipo ine ndinapita kumusi ku mpingo Woyamba wa Chibaptisti, ndipo Iye anali njira yina.

Ine ndinati, “Ambuye, apo payenera kukhala njira yina yomwe ili yowona.”

Ndipo Chinachake chinati, “Icho ndi Mawu.”

Ine ndawagwira Mawu amenewo. Kupenya pa masomphenya aliwonse, kulikonse.

³⁵⁴ Tsiku limene ine ndinayika mwalawapangodya uko, ndi kuwuyika iwo mkati umo, ine ndinalembe pamenepo chomwe Iye anandiwonetsa ine mmawa uja mu masomphenya. “Khala wosaleka mu nyengo, isali nyengo; dzudzula ndi chipiriro chonse cha Chiphunzitso. Pakuti nthawi idzabwera pamene iwo sadzapirira Chiphunzitso cholamitsa; koma mwakutsata zokhumbira zawo adzadziwunjikira kwa iwoeni pamodzi, monga aziphunzitsi, pokhala ndi makutu oyabwa; ndi kukhala otembenezidwa kuchoka ku Chowonadi, kupita ku nthano.” Ndipo ine ndayiwona mitengo iwiri iyo, yomwe ine ndinayima nayo, ikuchita chinthu chomwecho. Uko nkulondola. Ndipo apo ife tiri. Ndipo izo nzowona. Ndipo, tsopano, ife sitidza . . .

³⁵⁵ Kumbukirani. Ndiroleni ine ndikulimbikitseni inu kachiwiri. Musati munene, “Zikomo inu,” kwa aliyense, konse. Musati munene, kuganiza kuti, mtumiki wina kapena chinachake, munthu wina wachivundi; pali chirichonse chabwimo za iye. Chifukwa, iwo sali ayi. Ine sindikusamala yemwe iye ali. Palibe kanthu kabwino kwa munthu aliyense. Uko nkulondola.

³⁵⁶ Ngati pali gulu lonse la malipenga atagona apa, ndipo imodzi ya iyo itachita kuwomba nyimbo yinayake, uyo ndi munthu . . . Malipenga awo ali mwangwiro osalankhula. Ndi munthu yemwe angakhoze kuwomba lipenga, yemwe amadziwa chimene iye ati achite, yemwe amatenga lipenga. Lipenga liribe kanthu koti lichite. Mawu amachokera ku luntha kuseri kwa ilo. Uko nkulondola. Kotero, malipenga onse ali ofanana.

³⁵⁷ Anthu onse ali ofanana. Akhristu onse ali ofanana. Palibe anthu akulu pakati panu. Ife sitiri anthu aakulu, osati akazi aakulu. Ife tiri tonse abale ndi alongo, onse ofanana, mu bulangeti lomwelo. Ife sitiri “aakulu.” Mmodzi samamupanga mmodzi wamkulu kuposa mmodzi wina, osati kanthu konse, koti tichite. Ayi, bwana. Koma ife tiri chabe tonse anthu okhalapo.

³⁵⁸ Musati muyesere kumasulira zinthu. Musati muyesere kuchita chirichonse kuposa kungokhala moyo wapafupi, kupereka matamando ndi ulemu kwa Yesu Khristu. Aliyense

akumvetsa izo tsopano? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.]
Ameni. Mukondeni Iye ndi mtima wanu wonse. Kodi inu mukuchita izo? [“Ameni.”]

Ndimkonda Iye, (Ndipo Ine ndidzatero!),
ndimkonda Iye
Poti Iye anayamba kundikonda
Nagula chipulumutso changa
Pa mtengo wa Kalvare.

359 Mulungu alemekezeke! Kodi aliyense akumvetsa mwathunthu? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Kodi aliyense akukhulupirira? [“Ameni.”] Kumbukirani pamene ine ndinkayamba, “Ndani wakhulupirira uthenga wathu? Ndi kwa ndani komwe mkono wa Ambuye wavumbulukira?” Kodi Iye wawululidwa kwa inu, chifundo Chake, ubwino Wake? [“Ameni.”] Amen. Ingokumbukirani, mkondeni Iye ndi mtima wanu wonse.

360 Ine ndikubwerera kwathu tsopano. Ine ndidzabwereranso kuno, Ambuye akalola, cha poyamba pa Juni.

361 Mwinamwake, ngati Ambuye achiyika icho pa mtima wanga, mwinamwake nthawiyina koyambirira kwa chirimwe ichi, mnga Juni kapena penapake, mwinamwake koyambirira kwa kugwa kwa masamba, ngati Ambuye achedwa, ine ndikanafuna kubwerera ndi kudzakhala mausiku ena asanu ndi awiri, kwa Malipenga Asanu ndi awiri otsiriza. Kodi inu mukanadzakonda izo? Kodi inu mudzakonda izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Mungamandipempherere ine inu, kuti Mulungu adzandithandize ine? [“Ameni.”] Chabwino.

362 Mpaka ine ndidzakomane nanu inu kachiwiri, kumbukirani nyimbo yabwino yakale iyi:

Ndimkonda Iye, ndimkonda Iye
Poti Iye anayamba kundikonda
Nagula chipulumutso changa
Pa mtengo wa Kalvare.

363 Tsopano ine ndikufuna inu muweramitse mitu yanu. Ine ndikufuna ndikupempherereni inu. Abusa asanakubalalitseni, ine ndikufuna ndikupempherereni inu.

364 Atate athu Akumwamba, lolani anthuwa, Ambuye, amvetse. Chomwe, ine ndikutsimikiza kuti pali ena omwe sakumvetsa. Koma, Atate, mulole iwo—iwo adziwe cholinga. Ndipo mulole iwo amvetse, Atate, kuti—kuti ndi chisomo Chanu kwa iwo kuti zinthu izi zawululidwa. Ndipo ine ndikufuna kukuthokozani Inu, Ambuye, chifukwa cha chidziwitso chodziwira zinthu izi zomwe Inu mwaziwulula kwa ife.

365 Ndipo ine ndikupempherera aliyense yemwe ali muno, aliyense yemwe wakhalapo pa misonkhanoyi. Ngati pali

ena omwe sakukhulupirira, lolani, Ambuye, iwo akhale okhulupirira.

366 Ine ndikupempherera onse omwe ati adzamvere Mawuthenga pa tepi. Ndipo ngati Icho chigwera, chomwe Icho chidzatero, mosakayika, mu makomo ndi malo a osakhulupirira ambiri omwe ati adzatsutse; koma, Atate, ine ndikupempherera mmodzi aliyense, kuti iwo asanene mawu amwano aliwonse, kuti iwo poyamba akakhale pansu ndi kufufuza Malemba pa zomwe zalankhulidwa, ndiyeno anene kwa Inu kuti iwo mowona ali odzipereka ndipo akufuna kudziwa ngati ichi chiri Chowonadi, kapena ayi. Ndipo ine ndikuwapempherera iwo, Atate.

367 Ndipo ine ndikuwapempherera awa omwe ayima motsatira makoma awa, omwe anayima kunja, omwe anakhala mu magalimoto awo, kwa ana aang'ono, ndi kwa onse amene akhala mkati. Ndipo basi onse a iwo, Ambuye, ine ndikupempherera kwa iwo.

368 Ndipo ine ndikupemphera kuti mapemphero anga adzayankhidwa, kuti Inu mudzawadalitsa iwo. Poyamba, Ambuye, mupatseni mmodzi aliyense Moyo Wamuyaya. Ine ndikupemphera kuti pasakhale mmodzi wa iwo wotayika, osati mmodzi.

369 Ndipo tsopano, Atate, ife sitikudziwa pamene chochitika chachikulu ichi chiti chidzakhale. Koma pamene ife tiwona zizindikiro izi zikuwonekera, ndipo zikuchitika Mwamalemba, zimatenhethsa mtima wathu pamwamba pa muyeso. Ndipo ine ndikupemphera, Atate Mulungu, kuti Inu mutithandiza ife.

370 Ine ndikupemphera kuti Inu muthandize m'busa wathu wokonedwa, M'bale Neville. Mpangeni iye, Ambuye, wodzaza ndi chisomo ndi wodzaza mphamvu, ndi kumvetisa, kuti iye akatenge Chakudya chosungidwa ichi ndi kudiyetsa anaankhosa a Mulungu.

371 Ambuye, ine ndikupemphera kuti Inu mudzasunge matenda kutali ndi ife. Izo zitafika pochitika, kuti pamene anthu adwala, kuti iwo adzakumbukire kukhalapo ndi Magazi okwanira onse a Ambuye Yesu omwe ali pa guwa, kuti apange chitetezera. Ndipo ine ndikupemphera kuti iwo adzachiritsidwa mwamsanga.

372 Ndipo ine ndikupemphera kuti Inu mudzasunga mphamvu ya Satana kutali ndi iwo, yowakhumudwitsa iwo, kapena kuyesera kuwapanga iwo kupanga miyambo. Kapena, ingosungani mphamvu za mdani kutali, Ambuye. Tiyeretsemi ife kwa Mawu Anu. Perekani izi, Ambuye.


373 Ndiye, Ambuye, ine ndikupemphera kuti Inu mundithandize ine. Ine—ine—ine ndikuyamba kuzirala, Ambuye. Ine ndikudziwa kuti masiku anga sangakhozenso kukhala ochuluka kwambiri. Ndipo ine ndikupemphera kuti Inu mundithandize ine, kundirola ine kukhala woota, Ambuye, ndi kuwona mtima ndi kudzipereka, kuti ine ndikakhoze kunyamula

Uthenga motalika monga iwo wakonzedwera kwa ine kuti ndikawunyamule. Ndipo pamene iwo udzafika ku nthawi yoti ine ndiyenera kutula pansi, ndipo ndikufika ku Mtsinje, ndipo mafunde kuyamba kulowa mkati, O Mulungu, nditakakhoza ine kukapereka Lupanga ili lakale kwa winawake yemwe adzakhale woona mtima nalo Ilo, Ambuye, ndipo adzanyamula Chowonadi. Perekani izi, Ambuye. Ndipo, mpaka pamenepo, ndithandizeni ine kukhala wamphamvu ndi wathanzi, ndi kulimbika.

³⁷⁴ Thandizani mpingo wanga. Tidalitseni ife pamodzi, Ambuye. Ife tiri Anu. Ife tikumverera tsopano kuti Mzimu Wanu uli pakati pa ife. Ife tikukhulupirira kuti Inu muyankha mapemphero athu. Pakuti, ife tikudzipereka tokha kwa Inu, ndi Mawu Anu, kwa utumiki kwa masiku athu onse pa dziko lapansi lino, mu Dzina la Mwana wa Mulungu, Yesu Khristu, Mpulumutsi wathu wokonedwa, kwa ulemerero Wake. Amenii.

Ndi . . (Mulungu akudalitseni inu!) . . .
ndimkonda Iye, (ndi mtima wanga wonse),
Poti Iye anayamba kundikonda ine.

Mulungu akudalitseni inu, M'bale Neville.

³⁷⁵ [Osonkhana akupitiriza kuyimba *ndimkonda Iye*. M'bale Orman Neville abalalitsa mu pemphero—Mkonzi.] 

CHISINDIKIZO CHACHISANU NDI CHIWIWI CHIKUPITIRIRA

³⁷⁶ [Inu mwangotsiriza kumene kumvetsera *Chisindikizo Cha Chisanu Ndi Chiwiri* choyambirira monga icho chinalalikidwa mwathunthu Lamlungu usiku, Marichi 24, 1963 ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana. M'bale Branham sanafune kuti kujambula koyambirira uku kuti kuperekedwe kwa anthu. Tsiku lotsatira, Lolemba, Marichi 25, 1963, M'bale Branham anapita ku chipinda cha motel cha M'bale Fred Sothmann ndi M'bale James Maguire amene pa nthawi imeneyo anali oyangánira kupanga kwa matepi. M'bale Branham anawauza abale amenewa, “Ine sindikufuna uthenga uwu utumizidwe momwe iwo uliri.” Atatha kumvetsera tepiyo mwiniwake, iye anawalamulira abalewo kuti akaimikire tepiyo pa malo enaake, ndipo pa malo amenewo (kuyambira paragrafu nambala 261) anajambula gawo latsopano lotalika pafupifupi maminiti twente (paragrafu 377-415). Gawo latsopano ili zitatero linadzagwiritsidwa ntchito kulowa mmalo mwa kutsirizitsa koyambirira (paragrafu 261-373). Kujambula uku ndi kokhako kumene kunaperekedwa kwa anthu kwa “Chisindikizo Cha Chisanu Ndi Chiwiri” kufikira 1966. M'bale Branham atachokapo, borodi la William Branham Evangelistic Association lonse linagwirizana kuti litulutse tepi imene inajambulidwa moyambirira ku Kachisi. Kuyambira nthawi imeneyo, kujambula kuwiri konseko kwakhala kukuperekedwa

kwa anthu. Ife tsopano taika uthenga wowonjezera uwu wa M'bale Branham pa tepi imodzi, limodzi ndi "Chisindikizo Cha Chisanu Ndi Chiwiri" choyambirira. Liwu lotsatira limene muti mulimveli likhala la M'bale Branham mu chipinda cha motelo Lolemba, Marichi 25, 1963—Mkonzi.]

³⁷⁷ Chikhala chinthu chabwino kuti iye sakudziwa chirichonse za Icho. Chifukwa, ngati iye akanatero, ndiye iye akanadzakopera Icho. Ndiwo machenjerero ake mu kuchita zinthu.

³⁷⁸ Kotero, chotero, Mulungu wachipanga Icho mobisika chotero kwa dziko lonse, ngakhale Kumwamba, mwakuti palibe njira yakumvetsera Icho, kokha pamene Mulungu adzachiwulula Icho, Iyemwini.

³⁷⁹ Tsopano ine ndikufuna inu kuti muzindikire, usiku uno, kuti mu Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi, apo panali—cholinga chofutukuka patatu cha Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi.

Panali cholinga chofutukuka patatu cha okwera pa kavalo.

³⁸⁰ Pakhala pali cholinga chofutukuka patatu mu zinthu zonse izi. Izo zikutibweretsa ife mmbuyo ku zitatu. Ndi zisanu ndi ziwiri, kachiwiri, mwawona, Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri, Mbale Zisanu ndi ziwiri, ndi zina zotero. Tsopano, mu zitatu ndi zisanu ndi ziwiri, ndicho chiwerengero cha Mulungu mu masamu Ake a kuwulula Mawu Ake.

³⁸¹ Tsopano inu muzindikira, monga mu o—o—okwera, tsopano, apo panali akavalo atatu omwe anapita kunjira. Mmodzi wa iwo anali woyera, mmodzi anali wofiira, mmodzi anali wakuda. Ndiyeno, mu kavalo wachinai, bwanji, onse a iwo anasakanizidwa pamodzi. Mwawona, cholinga chofutukuka patatu.

³⁸² Tsopano, Mulungu anachita chinthu chomwecho. Mulungu anachita chomwecho pamene Iye anatumiza mkango Wake, womwe unali Mawu Ake, kuti ukamenyane ndi wotsutsakhristu.

³⁸³ Ndiye ife tikuzapeza kuti Iye anatumiza ng'ombe ija pa nthawi ya n—nthawi ya chisawutso, chinyama chansembe. Ndipo mu nthawi ya chisawutso iyi, ndicho chonse chimene anthu akanakhoza kuchita, chinali ntchito basi, ukapolo, ndi kudzipereka iwoeni kwa nsembe.

³⁸⁴ Ndiye ife tikupeza kuti, mu m'badwo wotsatira, umene unali m'badwo wa okonzanso, Mulungu anatumiza nzeru za munthu, mutu wonga wa munthu pa Chamoyo, yomwe inali mphamvu yomwe inatuluka mwa okonzanso.

³⁸⁵ Tsopano kodi inu munazindikira? Yense. . . Nzosadabwitsa kuti anthu a masiku awa akukhalabe moyo mu matsire, monga zinaliri kuchokera ku m'badwo wa okonzanso, chifukwa iwo anangochiwona icho mwa—njira yachipembedzo ya kuyang'ana pa icho. Iwo amawona icho mwa njira yomwe maseminare

aphunzitsira icho. Imeneyo inali njira ya Mulungu pa nthawi yina, koma ife takhala moyo kupyola iyo.

³⁸⁶ Tsopano ife tikulowa mu m’badwo wa mphungu, vumbulutso kuti chiwululidwe, chinthu chonse. Tsopano fanizirani izi ndi Chivumbulutso mutu wa 10, ndime 1 mpaka 7. Ndipo ife tiwona apa mu Vumbulutso ili, Chivumbulutso apa, 10:1 mpaka 7, kuti, “Mu masiku a kuwomba kwa Uthenga wa mngelo wachisanu ndi chiwiri, kunali kuti atsirize zinsinsi zonse za Mulungu.”

³⁸⁷ Tsopano ife tikupezamo, nafenso, mu izi, kuti Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi, tsopano kukhala chotsegulidwa, icho chinali kwa cholinga chofutukuka patatu. Tsopano, apa panali zolinga.

³⁸⁸ Chinthu choyamba, chinali, kuti anamwali ogona anali woti akapyola mu nthawi ya Chisawutso kwa kuyetsedwa. Iye amayenera kukatsukidwa machimo ake a kusakhulupirira ndi kuwukana Uthenga. Ichi, iye anachitidwa mu nthawi ya Chisawutso. Ife tikuwona iwo akuthera cha apa mu Chivumbulutso 7, pakati pa mutu wa 6 ndi wa 7 apa, kuti iye anali atatsukidwa, ndipo iye anali atapatsidwa miinjira yake. Tsopano, iye sali Mkwatibwi. Koma uli mpingo, anthu angwiro omwe—omwe—omwe sanakhale nawo mwayi, mwinamwake, kuti alandire Uthenga, kapena mwanjira yina kuti iwo anachititsidwa khungu ndi aneneri abodza awa. Ndipo iwo—iwo sanapeze mwayi, ndipo apobe iwo ali odzipereka kwenikweni mu mtima. Ndipo Mulungu akudziwa mtima wawo. Ndipo apa iwo ali kutsukidwa, mu nthawi iyi.

³⁸⁹ Inu muzindikira izo kuti, nthawi yina ya kutsuka, ndiyo ya Israeli, pamene iye akusonkhana. Ndiko kufutukuka kwachiwiri. Mulungu akutsuka Israeli mu nthawi ya Chisawutso. Kuchokera mwa mamilioni omwe ati adzasonkhane kumeneko, apo padzakhala osankhidwa zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi, ndipo iwo adzatsukidwa, nawonso. Mulungu akutsuka Israeli.

³⁹⁰ Zindikirani, apo pali dziko lapansi lonse kuti likatsukidwe. Apo padzakhala chinthu choterocho monga mwezi, nyenyezi, ndi chirengedwe chonse, chidzatsukidwa. Inu mukuwona chomwe icho chiri? Dziko lapansi likudzikonza mwatsopano lokha, likutsukidwa, kukonzekera Zakachikwi. Zakachikwi zikubwera. Ndipo, mwawona, chirichonse chimene chiri ndi uve uliwonse mwa icho chiri choti chikatsukidwe nthawi ya Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi.

³⁹¹ Tsopano, tsopano, kodi inu mukuzindikira? Pa kutsegula kwa Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri ichi, chiri nachonso mu chinsinsi chofutukuka patatu. Chimodzi ichi, ine ndiri . . . ndilankhula ndipo ndalankhula, kuti chiri chinsinsi cha Mabingu Asanu ndi awiri. Mabingu Asanu ndi awiri Mmwamba adzafutukula chinsinsi ichi. Icho chidzakhala pa Kudza kwa

Khristu kumene, chifukwa Khristu anati palibe mmodzi akudziwa pamene Iye ati adzabwerere.

³⁹² Kodi inu munazindikira, pamene Ayuda anamufunsa Iye izo? Kudziwa...Pamene ife tinafaniziritisa Lemba apa ndi Mateyu 24, ndi Zisindikizo zisanu ndi chimodzi, Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri chinasiyidwa. Chifukwa, inu mukuwona, Khristu anati, “Mulungu yekha Mwiniwake akudziwa; osati ngakhale Angelo.” Nzosadabwitsa, Icho sichinalembedwe nkomwe. Inu mukuwona, iwo anatonthola; palibe kanthu kanachitika pamenepo. Angelo sakuchidziwa Icho. Palibe aliyense akudziwa pamene Iye akubwera.

³⁹³ Koma apo padzakhala—apo padzakhala m—Maliwu Asanu ndi awiri, a Mabingu awa, omwe ati adzawulule vumbulutso lalikulu pa nthawi imeneyo. Kotero, ine ndikukhulupirira, kwa ife omwe...Ngati ife sitikuchidziwa Icho, ndipo ngati ife... Icho sichidzaziwika mpaka nthawi imeneyo. Koma icho chidzawululidwa mu tsiku limenelo, mu ora lomwe icho chikuyenera kuwululidwamo. Kotero, chinthu choti ife tichite ndicho kukhala awulemu pamaso pa Mulungu, ndi kumutumikira Iye, ndi kuchita zonse zomwe ife tikudziwa kachitidwe kake, ndi kukhala moyo mwabwino, miyoyo ya Chikhristu. Apa, tsopano, ife tikupeza kuti Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi chatsegulidwa kwa ife; ife tikuchiwona Icho. Ndipo ife tikudziwa kuti Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri ichi sichingamatulidwe poyera mpaka ora ilo litafika.

³⁹⁴ Tsopano, apo panali chifukwa china chomwe Mulungu analolela Maliwu Asanu ndi awiri awa kuti abingulidwe. Chifukwa, Icho chiyenera kubwera, mwawona. Pakuti i...Ife tikupeza kuti Khristu, Mwanawankhosa, anatenga b—Bukhu mu dzanja Lake, ndipo Iye anatsegula Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri icho. Koma, inu mukuwona, icho ndi chinsinsi chobisika. Palibe mmodzi akuchidziwa Icho. Koma, Icho—Icho, motsatira kumene ndi zomwe Iye ananena, “Palibe mmodzi ati adzadziwe Kudza Kwake.” Iwo nawonso sadzadziwa za chinsinsi cha Mabingu-Asanu ndi awiri ichi. Kotero, inu mukuwona, izo nzolumikizana pamodzi.

³⁹⁵ Mwakuchuluka uko, ife tiri nako kumvetsa kwa Icho, lero, chifukwa chonse cha Icho chonse chafutukulidwa; koma ichi sichinafutukulidwe. Koma nditakhala mu chipinda changa, ndipo ine ndinamva ichi...kapena, osati kumva icho, kani, koma ndinawona Icho chikufutukuka kwa Mabingu Asanu ndi awiri awa. Tsopano, ndimo mwakutalikira momwe ife tingakhoze kupitira, pomwepo.

³⁹⁶ Ndipo tsopano ine ndikudalira kuti mmodzi aliyense wa inu adzatumikira Mulungu ndi kuchita icho chimene chiri

cholondola. Ndi kumukonda Iye, moyo wanu wonse, ndi kumutumikira Iye. Ndipo Mulungu adzasamalira zinazo.

³⁹⁷ Tsopano, ife tiri nazo, mu kutsirizitsa apa tsopano, mwa chisomo cha Mulungu, zinsinsi zonse za Zisindikizo zisanu ndi chimodzi zomwe zasindikizidwa, ndipo ife tikumvetsa ndi kudziwa apa kuti Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri sichiri choti chikadziwike poyera.

³⁹⁸ Tsopano, Kudza Kwake, pa ora ilo la Kudza Kwake, pamene chiwonongeko cha dziko lapansi, inu mukudziwa. Iye ananena pamenepo, “Chidzakhala chiyani chizindikiro cha kubwera kwa kutha kwa dziko?” Mu Mateyu 24, apo pamene iwo anamufunsa Iye funso limenelo. Iye anapita mmusi kwa icho. Iye anawawuza za Israeli kukhala akusonkhanitsidwa monga fuko, mu ndime ya 31, ya Mateyu 24:31. Koma ndiye Iye anayamba kupita pa mafanizo, mwawona. Ndiye inu mukuwona. . . “Phunzirani fanizo la mtengo wa mkuyu. Pamene inu muwona iwo ukuphukira masamba ake, bwanji, inu mudziwa kuti dzinja liri pafupi. Ndiyeno pamene inu muwona izi zikufika pochitika, ndiye dziwani kuti nthawi ili pafupi.” Mwawona, Israeli akusonkhana mu dziko lakwawo lomwe. Koma, inu mukuzindikira, Iye anasiya vumbulutso la Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri ichi.

³⁹⁹ Ndipo apa, pamene Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri, pamene Iye anatsegula Ichu, Iyenso anachidumpha Ichu kachiwiri, mwawona. Kotero ife tikuwona kuti Ichu chiri chinsinsi chathunthu, chotero ora silinafikebe kuti chinsinsi ichi chidziwike. Chotero, ife tafika apa, ndipo zotsala za Ichu zidzadziwika pomwepo pafupi nthawi yomwe Yesu akuwonekera pa dziko lapansi kachiwiri, kwa Mkwatibwi Wake, kapena chirichonse chimene chikuchitika pa nthawi imeneyo. Tsopano, mpaka nthawi imeneyo, tiyeni tonse tizingopemphera, kukhala moyo mwabwino, miyoyo yolunjika, ya Chikhristu, kuyang’anira patsogolo Kudza Kwake.

⁴⁰⁰ Ndipo tsopano ngati tepi iyi ikanadzakhala kuti yagwa mu dzanja la anthu ena kwina kwake, musati muyesere kupanga mtundu uliwonse wa mchitidwe kuchokera pa iyo. Chinthu chokha inu muchite, muzingopitirira kumutumikira Mulungu. Chifukwa, chinsinsi chachikulu ichi chiri chachikulu kwambiri mwakuti Mulungu sanamulole ngakhale Yohane kuti achilembe Ichu. Ichu chinabingula, koma Iye. . . podziwa izo, kutilonjeza ife kuti Ichu chidzatsegulidwa. Koma, mpaka pa nthawi yino, Ichu sichinatsegulidwe.

⁴⁰¹ Ndipo tsopano ife tiri oyamikira kwa Mulungu pa zomwe Iye watiwonetsa ife. Ine ndakhala ndikukhala mu chipinda kumtunda uko kwa masiku asanu ndi atatu. Ndipo Uthenga umene ine ndangotsiriza kumene kufotokozwa kwa inu, ambiri a inu pano adzamvetsa. Ndipo ine ndinalonjeza kuti panali

chinachake chimachitika, chauzimu, nthawi zonse, chomwe ine ndinali wotsimikiza kuti inu munali kuchiphonya icho. Ndipo apa pali chomwe icho chiri; ndicho kutsimizira kwamtheradi kwa kumasulira uku kwa Malemba kukhala kotumizidwa ndi Mulungu.

⁴⁰² Chifukwa, ife tisanati ngakhale kulowa mu Icho, ndipo ine ndinachoka kupita kumadzulo, Ambuye anandiwonetsa ine masomphenya tsiku limodzi, pafupi teni koloko, mmawa umodzi. Ndipo ine ndinabwera ndipo ndinawafotokoza iwo pano, kuti ine ndinali nditawawona iwo; ine sindinadziwe chomwe iwo anali. Kunali kuwundana kwa Angelo asanu ndi awiri. Ife tidzakumbukira zimenezo. Inu mudzazipeza izo pa tepi, yotchedwa, *Ndi Nthawi Yanji Ino, Mabwana?* Chabwino, tsopano, icho chiri chimodzimodzi chimene inu mukuwona tsopano. Angelo asanu ndi awiri. . . ine ndinali kumadzulo.

⁴⁰³ Inu mukukumbukira, atumiki ang'ono kwambiri; iwo anapita kummawa. Atumiki achiwiri, nkhunda, mbalame zokulirapo, iwo anapita kummawa. Ndiyeno ine ndinapenya . . . Iwo anali ndi ine, nthawi yonse. Zimenezo zinali Chikoka Choyamba ndi Chachiwiri.

⁴⁰⁴ Tsopano, Chachitatu chinabwera kuchokera kumadzulo, kusesera patsogolo ndi liwiro lalikulu, lowopsya, ndipo Iwo anandinyamulira ine mmwamba. Omwe anali kubwerera kummawa, ndi chinsinsi cha Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri izi. Monga ngati zinanenedwa mu—mu loto la Junior Jackson, lomwe Ambuye anandirola ine kumumasulira iye uko, “Mkati mwake mwa piramidi imeneyo, munali Mwala woyera umene sunalembedwepo.” Ndicho chifukwa ine ndinayenera kupita kumadzulo, kuti ndikalumikizane nawo Uthenga wa Angelo awa kuti, ndibwerere kuno kudzawulula Izo kwa mpingo. Kumbukirani, ine ndinati, “Zinthu zotsatira zomwe ziti zichitike zidzakhala pano pa mpingo.” Ndizo chimodzimodzi basi.

⁴⁰⁵ Chinthu china, ine ndikufuna inu muzindikire chimene chinachitika. Ndipo ngati inu mukumvetsera kwa tepi, ya *Ndi Nthawi Yanji Ino, Bwana?*, inu mudzazindikira kuti Mngelo mmodzi anali wozindikirika kwa ine. Ena onse a Iwo basi anali kuwoneka mwawamba. Koma Mngelo uyu anali Mngelo wozindikirika. Iye anali kumamzere kwanga, mu kuwundana mu mawonekedwe a piramidi.

⁴⁰⁶ Ndipo, kumbukirani, munali mu piramidi, momwe Mwala woyera wachinsinsi siwunalembedwepo. Ndipo Angelo ananditengera ine mkati mwa piramidi iyo ya Iwoeni, zinsinsi za Mulungu zodziwika kokha kwa Iwo. Ndipo, tsopano, Iwo anali Atumiki omwe anali atabwera kuti adzamasulire piramidi imeneyo, kapena Uthenga umenewo wa chinsinsi cha Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri izi zomwe zikugona mkati mwa piramidi.

407 Tsopano, Mngelo uyu, anali kumamzere kwanga, akanakhala kwenikweni wotsiriza, kapena Mngelo wachisanu ndi chiwiri, ngati ife tikanawawerenga Iwo kuchokera kumamzere kupita kumanja. Chifukwa, Iye anali kumamzere kwanga; ine ndikuyang'ana kwa Iye, kuloza kumadzulo, Iye akubwera cholozza kummawa, akanakhala ku mbali ya kumamzere. Kotero, uwo ukanakhala Uthenga wa mngelo wotsiriza, wozindikirika. Kumbukirani momwe ine ndinanenera kuti Iye anali nawo Wake, analoza mutu Wake kumbuyo; ndipo mapiko Ake akulu, akuthwa; ndipo momwe Iye anawulukira molunjika kwa ine. Tsopano, icho ndicho Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri ichi. Icho chikanali chinthu chozindikirika. Ndipo ife tiri . . . Ife sitikudziwa chomwe Icho chiri, pakali pano, chifukwa Icho sichikuloledwa kuti chimatulidwe.

408 Koma tsopano, mmodzi aliyense wa inu mu msonkhano wazindikira kuti, wakhala msonkhano bwanji! Aliyense amangowoneka kukhala pamapeto kumene a mpando wawo. Ndipo aliyense kuyimirira pozungulira apa, pa wani, thuwu koloko madzulo, kuyembekezera kuti zitseko zitseguke, ndi kubwera mpaka kuno kutsogolo. Kuyimirira mozungulira makoma; miyendo yadzanzi, ndi chirichonse.

409 Nchiyani icho? Iwo wakhala uli Mzimu Woyera ukutumiza Atumiki awa, ndipo Iwo akhala akuwulula Izo kwa ife. Ndiyeno zindikirani momwe Izo zagwirizirana nawo Mawu, chimodzimodzi.

410 Ndiyeno kuti akudziwitseni inu nonse kuti izi ziri Chowonadi, Iye ananeneratu izo pafupi—pafupi miyezi iwiri tsopano, kapena kupitirira, izo zisanachitike nkomwe. Kutu, pamene ine ndinapita kumadzulo, mosadziwa Izo; kubwerera kuno ndi kumasulira monga Iye waperekera Izo. Tsopano kumbukirani, mu masomphenya, Iye sanandiwuze ine kanthu kamodzi mu masomphenya pamene Iye ananditengera ine mmwamba. Ine ndinali wamantha, kuwopa kuti ndimapita kukafa, kuphedwa mu kuphulika. Inu mukuwona, Iwo sakanakhoza kuchita izo.

411 Kumasulira kunabwera basi pamene ine ndinali ndi kusowa kwa Izo, umo munali mchipinda, ndipo ine ndinazipereka Izo basi momwe Iye amaperekera Izo.

412 Tsopano, inu mukuwona, amzanga, masomphenya samalephera. Iwo ali nthawizonse angwiwo. Iwo ali owona chimodzimodzi basi.

413 Tsopano, masomphenya, kuphatikiza Mawu, kuphatikiza mbiriyakale, kuphatikiza mibadwo ya mpingo, ndi zonse, zikugwirizana pamodzi. Kotero, ine ndikhoza kunena mowona, kuti, mwakukhoza kwa kumvetsa kwanga, ndi malingana

ndi Mawu a Mulungu, ndi masomphenya, ndi vumbulutso, kumasulira kwake kuli PAKUTI ATERO AMBUYE.

⁴¹⁴ Tsopano, Ambuye atakudalitsani inu nonse, mmodzi aliyense, molemerera kwenikweni, pamene ife tikuyima tsopano ndi kuyimba nyimbo yabwino yakale iyi ya mpingo. Mulungu akudalitseni inu, mmodzi aliyense. Ameni.

⁴¹⁵ [M'bale Branham akuwonjezera mizere yotsatira inayi, yotengedwa kuchokera ku paragirafu 374 ya Uthenga wake usiku watha, Malichi 24, 1963.—Mkonzi.]

Ndi . . . (Mulungu akudalitseni inu!) . . .
ndimkonda Iye, (ndi mtima wanga wonse),
Poti Iye anayamba kundikonda.

Mulungu akudalitseni inu, M'bale Neville.



CHIVUMBULUTSO CHA ZISINDIKIZO ZISANU NDI ZIWIRI
(The Revelation Of The Seven Seals)

Mauthenga khumi awa analalikidwa ndi M'bale William Marrion Branham pa Marichi 17 mpaka pa Marichi 24, 1963, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., ndipo *Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri* chinapitirira pa Marichi 25 ku Sherwood Motelo. Titapeza matepi apachiyambi omveka ndi otsirizika kwathunthu, Mauthenga awa abwerezedwanso molingana ndi dongosolo latsopano. Kuyesesa konse kwapangidwa pochotsa molondola Uthenga wolankhulidwa pa matepi a maginito kupita ku tsamba losindikizidwa, ndipo atsindikizidwa mkatimu mosachotsera mawu ena.

Maufulu onse mu bukhu ili ndi osungidwa. Bukhu ili silingagulitsidwe, kapena kusindikizidwanso, kumasuliridwa mu zilankhulo zina, kapena kugwiritsidwa ntchito popezera ndalama wopanda kufotokoza kwa chilolezo cholembedwa cha William Branham Evangelistic Association. Kunasindikizidwa kachiwiri mu 2005.

CHICHEWA

©1994 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org